KHALANI OKONZEKERA MAVUMBULUTSO ATSOPANO!!

Mulungu adamupanga munthu kukhala wolenga. Iye wapereka kwa munthu mphamvu ya kulenga ya Mulungu. Mkati mwa munthu muli mphamvu yolenga yotere yomwe ikhoza kusintha moyo wako.

TSOPANO MUZUNDIKIRA ZINTHU IZI MU BUKULI

. Umo Mulungu akufunira mzimu wako kukhala woonetsera mphamvu yake ya kulenga.
. Umo ungathe kumva kulankhula kwa Mulungu mkati mwako
. Umo ungayende mu uzimu pamene mphamvu yakulenga ikuyenda mwa iwe
. Zakuya za Mulungu za mphamvu yake ya kulenga
. Kuvumbuluka kwa chikonzekero cha Mulungu pa moyo wako Chiyanjano chako ndi Mulungu chikhala chozama pamene ukuwerenga buku ili pamodzi ndi kugwiritsa ntchito fundo zonse za mubukuli.

Mark Virkler adalandira digrili ya maphunziro aza uzimu komanso filosofa ku koleji ya Robert Wesleyani digriri ya masiter ndi udotolo wa za baibulo. Adaphunzira ku mpigo wa baptist ndi Free Methodist komanso adaphunzitsidwa ndi aphunzitsi ena a gulu la za chitsitsimutso la (Charistimatic). Kuzama kwa Mark Virkler pa za baibulo ndi zotsatira za kukhala mu ziphuzitso zokuya za aphunzitsi osiyanasiyana. Iye wagwira ntchito ya ubusa pa zaka 20. Iye ndi woyambitsa wa bungwe lotchedwa "spirit Born-creativity Inc kagulu kosindikiza mabuku a za uzimu komanso kuphunzitsa zachitsitsinutso ndi njira ya chiyanjano ndi Mulungu pa dziko lonse lapansi. Mark Virkley pamodzi ndi banja lake amakhala ku Buffalo-NY ku America.

photo

Destiny Image
P.O. Box 351
Shippensburg
PA 17257
Losindikizidwa ku America
Logawidwa ku dziko lonse lapansi
ISBN # 0-56043-004-4

EUROPE, AFRICA, ASIA AUSTRALIA 20%

Chonde mudikire kwa masabata 6-8 kuti mumulandire.
Kutumiza zonse pamodzi ($2.50)
C.O.D. ikupezeka ku US (Amerika) basi zonse pamodzi.

CHIDZIWITSO: Ngati siudasangalatsidwe ndi mabuku awa, uwabweze pasadathe masiku 30 ndipo udzapatsidwa ndalama zako zonse ndapereka. Ndalama zonse zitumizidwe ku; Communion with God Pulishera, 1431 Bullisa Road, Elmony 14059, 716-55-0647.

- Kope lofotokoza za umo mungaitanitsire mabuku awa aulele lilpo lofotokoza pafupifupi maphunziro makumi asanu (50) (makaseti komanso ma vidiyo amene Mark Virkler pamodzi ndi Patt alemba. Mabuku awa ndi othandiza kwa munthu ailyense payekha. Magulu aang'onoang'ono anthu, mapemphero ochitika mnyumba ndi mnymba, Sande sukulu ya maphunziro komanso zina ndi zina zofunikira. Poonjezera apo pali mabuku ena ofotokoza za madera monga "kukhala mwa Yesu" Mphamvu Yesu," mphamvu ya kulenga," maloto," Kumasula madalitso pa chuma, kupemphera mwa mzimu ndi zina zotero.

- Kope laulele lokudziwitsa zinthu zochitika mu utumiki wa Mark Vikler pamodzi ndi Patt komanso mapulogramu awo.

- Kope laulele lofotokoza maphunziro 13 ochitika ndi Mark Virkler lilipo.

Ndikadakonda kulankhula nawe pa telefomi ngati uli ndi funso lililonse....." (407-269-6702).

M'busa Judson Cornwall, THD....."Mulungu wapereka chisomo chapadera kwa m'bale Mark Virkler kuthandiza anthu kuti akazindikire umo angakhalire mu "chiyanjano ndi Mulungu." Ndakhala ndi mwayi woona ichi pa nthawi koma tsopano ndaganiza zokhala naye pamodzi m'bale Mark Virkler kuti chiphunzitso ichi chipite patsogolo kwa anthu amene ali thupi la Yesu Khristu.

Ine ndichitira umboni kuti m'bale Mark Virkler pamodzi ndi utumiki wake ndi njira yozindikira chifuniro cha Atate. Kaphunzitsidwe kake kali kodabwitsa ndi kodalirika. Iye akuzamitsa anthu mwakuya komanso mu kapembedzedwe

UTUMIKI WA CHIYANJANO NDI MULUNGU

DZINA.....TELEFONI.....

ADIRESI.....MZINDA.....ZIP.....

MTUNDU WA BUKU
MITENGO

| | |
|---|---|
| Chiyanjano ndi Mulungu (Buku la wophunzira) | $13.95 |
| Chiyanjano ndi Mulungu (Buku la mphunzitsi) | $11.95 |
| Chiyanjano ndi Mulungu (Makaseti) | $42.00 |
| Chiyanjano ndi Mulungu (matepi a vidiyo) | $299.00 |



| | |
|---|---|
| -HS - Beta<br>VHS - Beata<br>(akubweretsa) | $99.00 |
| Kulankhula ndi Mulungu | $6.95 |
| Mulungu amalankhula kupyolera Aheberi | $7.95 |

KULANGIZIDWA NDI MULUGU

| | |
|---|---|
| Kulangizidwa ndi Mulugu | $6.95 |
| Kulangizidwa ndi Mulungu (buku la wophunzira) | $8.95 |
| Kulangizidwa ndi Mulungu (buku la mphunzitsi) | $9.95 |
| Kulangizidwa ndi Mulungu (Matepi a vidiyo) | $42.00 |

| | | |
|---|---|---|
| VHS - Beta (kugula) | = | $299 |
| VHS - Beta (kubweretsa) | = | $99 |

KUFUKULA MPHAMVU YA KULENGA

| | |
|---|---|
| Mphamvu ya kulenga (buku) | $8.95 |
| Mphamvu ya kulenga (buku la phunzitsi) | $4.95 |
| Zomwe baibulo likamba pa siliva ndi golidi | $3.95 |
| Fundo makumi awiri kayendetsedwe | $9.95 |

KUTUMIZA NDI MITENGO YAKE

| | |
|---|---|
| US | 8% |
| CANADA | 12% |
| SOUTH AMERICA | 16% |

KULANKHULANA NDI MULUNGU - Ili ndi buku la masamba 250 lodzadza ndi maumboni osiyanasiyana komanso muli zolemba za anthu osiyanasiyana pafupifupi masamba 30. $6.95

MULUNGU WATHU AMALANKHULA KUPYOLERA MWA AHEBERI - Ili ndi buku lolembedwa ndi m'busa Petro Lord. Mu zolembedwa zonse muli vesi yochokera mu chiheberi komanso zimene Mulungu adalankhula kupyolera mwa Petrol Lord kukhudzana ndi vesi iliyose. $7.95

MAUMBONI KUCHOKERA KWA ANTHU OSIYANASIYANA

Dr. Richard Watson - Oral Roberts University.

Buku la "chiyanjano ndi Mulugu" lolembedwa ndi Patii Virkler lasintha modabwitsa kapempheredwe kanga. Ndikutha kulumikizana ndi Ambuye kosavuta. Ndikuchitira umboni kuti lili lothandiza kwa aliyense ndikukhulupiria kuti buku ili lotsitsimutsa kwa anthu pa nthawi ino.

M'busa Thomas Reid - Full Tabernacle Gospel

Buku la "Chiyanjano ndi Mulungu lisintha anthu a dziko lapansi pokonzanso anthu a m'bado watsopano amene akhoza kumva kulankhula kwa Mulungu pamodzi ndi maloto a Mulungu.

MPHAMVU YAKULENGA MWA MZIMU - ZIPANGIZO ZOFUNIKIRA

Ili ndi buku lophunzitsa kamasulidwe ka mphamvu yakulenga ya Mulungu kupyolera mu mtima wa munthu wokhulupirira. Buku lamasamba 238 ili labwino kwa anthu a bizines, makolo komanso aliyense amene akufuna kukhala wolenga. &8.95



KULANGIZIDWA NDI MULUNGU - ZIPANGIZO ZOFUNIKIRA

Ili ndi buku lofokoza umo ungapezere machilitso ku zosoweka za moyo wako. Limafotokoza umo ungachilitsidwire ku kwiyo, mantha kupweteka mtima komanso umo ungafungatirire kulankhula kwa Mulungu pamodzi ndi masomphenya. Ndi lothandiza kwa aliyense komanso kukhoza kugwiritsa ntchito pagulu - &6.95 (masamba 130)
KULANGIZIDWA NDI MULUNGU - LA MPHUNZITSIDWA - Lokhala ndi mitu 22 komanso fundo zake zopezeka mu ma vidiyo 22 = $8.95

KULANGIZIDWA NDI MULUGU (MAKASETI amaora 11 - Mark Virkler
akuphunzitsa = $42.00

MARK VIRKLER ALI WOPEZEKA

Mark amayendayenda kumupangitsa maphunziro a "kuyanjana ndi Mulungu" pamodzi ndi dziko lonse lapansi. Mu khoza kulankhula naye pochita telefoni pa nambala iyi kuti mukonze dongosolo umo angafikire ku mpingo wanu.

MAUMBONI

M'busa Petro Lord - Park Aenue Baptist Church

....."Ndakhala m'busa wa mpingo wa Baptist pa zaka 37 ndipo ndichitira umboni kuti maphunziro monga akuyanjana ndi Mulungu," kukhala mwa Yesu," kulangizidwa ndi Mulungu" ali ofunikira ku kumangirira moyo wa mkati wa uzimu. Pa nthawi ino tiri ndi maphunziro 6 a "kuyanjana ndi Mulungu" pogwirira ntchito matepi a vidiyo a Mark Virkler. Mu kalasi lina ali pa phunziro la "kulangizidwa ndi Mulungu." Ine ndikuchitira umboni kuti Mark Virkler pamodzi ndi utumiki wake ndi mdalitso kwa aliyense.

wake (Genesis 16:2) Sara adaganiza kuti a khala ndi ana kupyolera mwa zakazi wake Hagara. Lingaliro ili lidapangitsa matsutsano kuyambira pa nthawiyo mpaka lero monga anthu obadwa kuchokera kwa Sara ndi Hagara akumenyana mpaka lero. Mulungu sadavomereza mphamvu zawo za thupi kuti chozizwitsa chikachitike (Genesis 17:19).

IFENSO TIYENERA KUDIKIRA MWA CHIPIRIRO PA MULUNGU POZINDIKIRA KUTI MPHAMVU ZANTHU ZATHUPI ZIMANGOONONGA CHABE ZINTHU

F. KUPEMBEDZERA OLUNGAMA (GENESIS 18:20-23)

Atamva kuti chiweruziro cha Sodomu ndi Gomora chayandikira, Abraham adayamba kupembedzera oyeramtia onse - kumapempha Mulugu kuti awapulumutse. Zotsatira zake Mulungu adachita chozizgwa ndipo anthu adapulumutsidwa.

IFENSO TIYENERA KUPHUNZIRA KUPEMBEDZERA ANTHU OLUNGAMA

G. CHIDULE CHA MAPHUNZIRO AMENE ABRAHAM ADAPHUNZIRA

1. Chikhulupiriro chophweka

2. Kuremera kophweka

3. Chikondi chopanda malire

4. Kukhulupirika kwa Mulungu

5. Kugonjetsa mphamvu za umunthu wathu

6. Kupembedzera oyera mtima



CHIYANJANO NDI MULUNGU - ZIPANGIZO ZAKE

Ichi ndi chiphunzitso chapadera chophunzitsidwa ponse ponse pa dziko lapansi kuphunzitsa akhristu umo angakhalire pa chiyanjano ndi Mulungu. Pafupifupi magawo makumi asanu ndi anayi mphamvu zisanu ndi zinayi (99%) mwa ena onse ayamba kugwiritsa ntchito masomphenya mu mapemphero awo ndipo alemba zinthu zambiri zokhudzana ndi chiyanjano chawo cha tsiku ndi tsiku ndi Mulungu. Ngati siudakhutitsidwe ndi buku ili ukhoza kutumiza pasadathe masiku makumi atatu ndipo udzabwezeredwa ndalama zako zonse udagulira bukulo.

CHIYANJANO NDI MULUNGU - BUKU LA WOPHUNZIRA LOGWIRITSIRA NTCHITO:

Buku ili ndi masamba 150 ndipo mu bukuli, Mark Virkler akuphunzitsa kupyolera mu bukuli koma pa vidiyo pamodzi ndi pa kaseti mtengo wake ndi $13.95.

CHIYANJANO NDI MULUNGU - BUKU LA WOPHUNZITSA:

Mu buku ili muli maphunziro 22 komanso ogwirizana ndi ma vidiyo 22 ndipo muli maphunziro abwino a mtsogoleri. $11.95.

CHIYANJANO NDI MULUNGU - TEPI YA VIDIYO.

Mu matepi awa, Mark Virkler amakhala akuphunzitsa pa maora 22 mu kalasi. $299 (kubwereka = $99.00)

CHIYANJANONDI MULUNGU - MAKASETI

Mu makaseti awa otenga ma ora 22, Mark Virkler akuphunzitsa zakukhala mu chiyanjano ndi Mulungu. Pali kaseti yina yoonjezera mmene amaphunzitsa za umo ungazitonthozere wekha (kukhala chete) Usadafike pamaso pa Mulungu $42.00

MUTU D

MAPHUNZIRO ENA ABRAHAM ADAPHUNZIRA MU KUYENDA KWAKE MWA CHIKHULUPIRIRO

A. KUMVERA PANG'ONO KUFIKIRA KU KUMVERA KWAMPHUMPHU

Kuyenda kwa chikhulipiriro kwa Abraham kudayamba pa Genesis 12:1-3 ndi mawu olankhulidwa a Mulungu (rhema) kuvumbulutsa chitsogozo cha Mulungu pa moyo wake - kumpatsa malonjezano aakuru a fuko lalikuru limene lidzaturuka mchuuno mwake. Iye adali ali ndi zaka makumi asanu ndi awiri ndi mphambu zisanu (75) panthwiyo. Abraham poyamba sadayambe kumvera kwamphumphu pa nthawi iyi, mmalo mosiya abale ake onse, adatenga loti pa ulendo wake (Genesis 12:4).

Apa mutha kuona kuti Mulungu amafunakukula kwapadera kuchokera pa mumvera kwamphumphu. Izi zidalekanitsa ndi abale kwamthumthu kulola kuti malonjezano ake akwanilitsidwe (Genesis 13:14-18).

Pa nthawi imene Abraham amafika zaka 33 adali ataphunzira kwa nthunthu za kumvera. (Genesis 17) Pamene Mulungu adaonjezera lamulo la mdulidwe, Abraham adamvera "tsiku lomwelo...." (Genesis 17:23). Izi zidatsegula njira kuti Abraham ayambenso kulumikizana mu chiyanjano ndi Mulungu (Genesis 18:1) pomwe kusamvera kwake koyamba kudabweretsa kuduka kwa chiyanjano pakati pa Iye ndi Mulungu pa nthawi yaitali.

IFE TIPHUNZIRE KUTI KUMVERA KWAMPHUMPHU KUMASUNTHA DZANJA LA MULUNGU

B. KUKAIKIRA KUKHULUPIRIRA PA MULUNGU

Pa Genesis 12:10-20, tikutha kuona kuti kukaika pamodzi ndi



mantha zinagwira mtima wa Abraham. Iye adali kuopa kuti Aigupto adzatenga mkazi wake ndi kumupha iye - uko kudali kukaikira mphamvu ya Mulungu yomusunga iye. Patapita zaka zingapo, iye adakumana ndi vuto lomwe la chikaikiro (Genesis 20:1-18, kulankhula bodza kuti ateteze moyo wake). Abraham adaphunzira kukhulupirira Mulungu pamene yesero lidaperekedwa ndilo lakuperekedwa mwana wake Isake paguwa lansembe - apa Abraham adakhulupirira mphamvu, pamodzi ndi kupatsa kwa Mulungu. Iye adakhuluprira Mulungu kuti akhozanso kumudzutsa kwa akufa (Genesis 11:17).

IFENSO TIYENERA KUSAMAKAIKIRSA PA MULUNGU

G. CHIKONDI CHOPANDA MALIRE GENESIS 13:14

Pa Genesis 13, Abraham adapereka njira yothetsera mkangano pakati pa iye ndi Loti poyamba kuti asankhe dera la malo lomwe iye adakonda Loti adasankha dera labwino kuposa Abraham adatenga.

Pa Genesis 14 tikuona kuti Loti adali mu mavuto ambiri ndipo Abraham adafika ku zamunthandiza mwa chikondi.

IFENSO TIYENERA KUTHANDIZA AMNZATHU MWA CHIKONDI AMENE ATILAKWIRA

D. KUKHULUPIRIKA KWA MULUNGU (GENESIS 14:17-24)

Ngakhale Abraham adali ndi ufulu wotenga zinthu zonse koma sadatero koma kuti iye adasunga lumbiro adachita kwa Mulungu (Genesis 14:22-24).

IFENSO TIYENERA KUSIYA ZINTHU PADERA CHIFUKWA CHA MAWU A MULUNGU

E * KULEPHERA KWA MPHAMVU ZATHU ZA THUPI (Genesis 16)

Pamene amadikira Mulungu kuti akwanilitse lonjezo, Abraham adachita molakwika potsatira malingaliro a kusapilira a Sara - mkazi

3. VUTO LACHITATU KUDULA MPHAMVU YA MASOMPHENYA NDI CHOLINGA KUTI ULEWE TCHIMO LA KUSILIRA

Anthu ena akhala akufuna kuthetsa vuto lakusilia podula mphamvu yakuona. Anthu otere amalephera kuona kenakalikonse kuphatikizapo bedi ya kuchipinda kwao.

Pofuna kuchilitsa vuto ili, munthu ayenera kuchita izi;

1. Ayenera kuzindikira kuti pali njira zamphamvu zothetsera kusilira osati kudula mphamvu za kuona.

2. Phunzira kugwiritsa njira ntchito zina zothetsera kusilira

3. Aynera kulapa chifukwa chodula mphamvu za kuona

4. Ayenera kupempha Mulungu kuti abwezeretse pamodzi ndi kulenganso mphamvuyo.

5. Ayenera kuyamba kugwiitsaso ntchito mphamvuyo.

6. Ayenera kupempha Mulungu kuti adzadze mpahmvu yakuonayo ndi masomphenya.

VUTO LA CHINAYI - KUDULA MPHAMVU YAKUONA NDI CHOLINGA KUTI ASAMATHE KUONA ZINTHU ZOIPA

Anthu ena akhala akudula mphamvu ya kuona zinthu ndi cholinga kuti asamapenye zinthu zoipa. Zinthu zake ndi monga maloto, kuona njoka, ndi zina zotere. Iwo amaona kuti njira yabwino yoletsa kumaona  zoterezi ndi kudula mphamu za kuona.

Pofuna kuchilitsa uto ili munthu ayenera kuchita izi:

1. Ayenera kuzindikira pamodzi ndi kupeza chifukwa chenicheni chodulira mphamvu ya kuona.



2. Awapemphe Ambuye kuti akuonetsere kanthu kena kake

3. Upemphe Ambuye kuti abwezeretse mphamvu ya kuona

4. Uyambe kuyenda mu masomphenya.

5. Upereke maso ako mkati mwa mtima wko ndipo upemphe Mulungu kuti a wadzadze ndi masomphenya.

Mwachidule izi ndi zoletsa zomwe zimapangitsa anthu kuti asagwiritse ntchito maloto, masomphenya, komanso malingaliro. Aliyense wa ife ayenera kugwiritsa ntchito mphamvu izi zimene Mulungu adaika mwa munthu.

MUTU C

DIAGRAM

MUTU B

KULOLA MULUNGU KUTI ABWEZERETSE MPHAMU YAKO YA MASOMPHENYA

Anthu ena amaona kuti ndi chinthu chosatheka kukhala ndi masomphenya. Payenera kukhala zifukwa zingapo zomwe iwo alinazo. Ndi chinthu chabwino kufunafuna Ambuye kuti akupatse vumbulutso la zoletsa komanso uwapemphe Ambuye kuti akuonetsere njira zake zimene ungatsatire kuti uchilitsidwe kuvutolo.

Awa ndi ene mwa mavuto odziwika bwino komanso njira zake zogonjetsera zomwe zakhala zotsimikizika kuti zothandiza:

1. VUTO LOYAMBA KUPEMBEDZA MAFANO PAMODZI NDI WOSAKHULUPIRIRA MASOMPHENYA

Anthu ambiri ali opembedza komanso sakhulupirira za masomphenya. Samawatenga masomphenya monga mphatso imodzi za Mulungu. Sailemekezanso ngati mphatso ya Mulungu.

Pochilitsa vuto ili munthu ayanera kuchita izi:

1. Ayenera kulapa chifukwa chakusalemekeza pamodzi ndi kusagwirizana, kusagwiritsa ntchito mphatso ya Mulungu yoikidwa mwa iye.

2. Ayenera kulapa chifukwa chokhala ndi mzimu wa mafano mkati mwake

3. Ayenera kupereka pamodzi ndi kuyamba kulemekeza mphatso ya Mulungu.

4. Ayenera kupempha Mulungu kuti amuuziremphweya pamodzi ndi kubwezeretsa mphamvu yake ya kuona masomphenya



pamodzi ndi kuwakhulupirira.

5. Ayenera kumakhala wopereka maso ake amkati kwa Mulungu pamodzi ndi kupempha Mulungu kuti awadzadze ndi masomphenya.

2. VUTO LACHIWIRI MANTHA KUTI UNGAKHALE WA MIZIMU

Ena akhala asakugwiritsa mphatso yao ya masomphenya kuopa kuti angatchedwe opembedza mizimu.

Pofuna kuchilitsa vuto ili, munthu ayenera kuchita izi:

1. Ayenera kuzindikira kuti mphamvu ya kuona masompheya idaperekedwa ndi Mulungu osati satana ayi

2. Ayenera kuzindikira kuti ngakhale satana amapereka masomphenya kuona masomphenya koma kumakhala kukopera chabe - Mulungu ndiye mwini wake.

3. Ayenera kuzindikira kuti Mulungu sakufuna kuti ife tikhale opanda masomphenya koma kuti tikhale odzadzidwa nawo nthawi zonse.

4. Ayenera kuthamangitsa mzimu wa mantha popeza ndi wa satana koma kuti akhale ndi chikhulupiriro ndi kuchivomereza ndi pakamwa pake.

Ayenera kulapa mantha monga ali tchimo ndi kulandira mphatso ya Mulungu mwa chikhulupiriro.

6. Ayenera kuzindikira kuti satana amabweretsa maganizo komanso masomphenya. Maganizo pamodzi masomphenya ziyenera kuperekedwa pamaso pa Ambuye.

Iye amalolera zofooka zanga ndi kunditenganso mmanja mwake kuti ndipeze chisomo pamaso pake. Inde, ali ndi njira zambiri zondisungira ine kukhalapo wodzichepetsa pamaso pake komaso pa abale anga.

Ndikuganizira kuti ndi munthu yekhayo amene akulephera kukhala mu chiyanjano ndi Mulungu amene angayambe kunyada pamodzi ndi kudzikweza kuphatikizapo ndi mwano. Mwa ichi ndikukulimbikitsani kukhalabe mu chiyanjano ndi Mulungu ndipo kunyada sikudzakhala mu moyo wako. Ngati ulephere kukhala mu chiyanjano ndo Mulungu, nkosavuta kuti kunyada pamodzi ndi kudzikweza kukuononge moyo wako wa uzimu.

KUKHALA OMASUKA AcHIMWEMWE, PAMODZI NDI MOYO WOSANGALALA

Tiyenera kukhala nthawi zonse omasuka osakakala. Mulungu yekha ndi amene uyenera kukhala womuopa pochita zinthu umutenge Iye monga moyo wako. Uzitenge wekha monga munthu chabe wokungotengedwa mu mzimu wake. Khala moyo womasuka ndi wa chimwemwe ndi anthu ndipo nthawi zonse ukhale pamaso pa Mulungu kupenyerera kukongola kwake. Khala wosangalala ndi moyo wokhala ndi moyo wokhala mu chiyanjano ndi Iye. Zindikira kuti pamene ukukhala moyo womasuka ndi wachimwemwe, Iye adzachita zazikuru moyo wako.

Pempho langa ndiloti Mulungu awale pa moyo wako umene ukukhala. Mtendere!

ZOLEMBA ZAKO
Ambuye kodi ndikupereka ulemelero wonse pa chilichonse kwa Inu? Chonde ndilankhuleni.

MITU YA KUMAPETO



MUTU A - Kumvetsa mphamvu ya mawu (rhema) "mawu olankhulidwa"

MUTU B - Kulola Mulungu kuti abwezeretsenso mphamvu ya masomphenya

MUTU C - Chinthunzi cha kufa kwa masomphenya

MUTU D - Maphunziro ena Abraham adaphunzira mu kuyenda kwake kwa chikhulupiriro.

MUTU - A

| | MTUNDU WA RHEMA | CHITSANZO MU BAIBULO |
|---|---|---|
| Wopereka moyo kwambiri | Ndikulankhula zimene Mulungu akulankhula (kutanthauza mawu otuluka (rhema) kuchokere mkama MWAKE (rhema ya Mulungu) | ....."Mawu (rhema) amene ndinena ine sikwa ine ndekha koma atate wokhala mwa ine achita ntchito zake....." (Yohane 14:10) ....."Mau (rhema) amene munandipatsa ine ndinapatsa iwo..." (Yohane 17:8) ...."Onani pa Luka 1:38, 5:5, Yohane 5:19, 20 30, 8:26 38, 28, 3:34, 6:63, Machitidwe 10:13, 2 Akorinto 12:4, Aefeso 6:17 Aheberi 11:3, 12:19) |
| Operekako moyo | Kulankhula mawu olembedwa a Mulungu | ....."Ndipo imirirani mulankhule mkachisi kwa anthu onse mawu a moyo umene....." (Machitidwe 5:20 |
| Kukhala pakatikati (Naitral) | Kuzilankhulira ine ndekha | ..."Mau onse opanda pake (rhema) amene anthu adzalankhula adzawerenga mlandu wake tsiku lake lakuweruza...." |
| Owoononga kwambiri | Kulankhula MAWU A Satana omwe ndawamva mmbuyomo | ...."Tinamva iye alikunenera Mose ndi Mulungu mawu (rhema) amwano "Machitidwe 6:11 ...."Ndipo lilime ndilo moto ....liyatsa mayendedwe achibadwidwe ndipo lidzayatsidwa ndi gehena. "(Yakobo 3:6) |
| Zoononga | Kulankhula zimene satana akulankhula mkati | |

kanthu kenakake. Kodi tsopano uli mkati mobereka masomphenya amene Mulungu waika mu mtima mwako? Ngati zili chomwecho, fotokoza umo zilili.

PEMPHERO:
Ndiyamika inu Ambuye kuti mwasankha kubereketsa ufumu wanu kupyolera wa anthu - mwa atumiki anu osankhika.

Chaputala 12

Tsopano muli nacho. Ntchito ya kubereka yatha. Zonse zatha. Ali yense ali wosangalala. Aliyense akuyamikira. Chinthu chodabwitsa bwanji chimene takwanilitsa!

Kodi timagwira bwanji ulemelero umene umafika pamene tagwiritsidwa ntchito modabwitsa ku kukwanilitsa zolinga za Mulungu? Zimatipangitsa kuona bwino kukhala mu nthawi zonga zoterezi. Komabe inu ndi ine timadziwa kuti sizili mphamvu zathu zidachita chozizwa ichi. Kapena adali maganizo athu ozama. Sitidali ife amene tidakhazikitsa zinthu zonse mwangwiro, komanso mu nthawi yake. Tidangokodwa mu mphamvu ya Mulungu. Mchimwemwe chotani kukodwa mu mphamvu ya Mulungu!

Kodi tsopano timachita chiyani pamene anthu afika kudzatiyamikira? Poyamba timadziwa kuti ndi Mulungu mwaife amene akumuyamikira ndipo ife mkati mwathu timangolankhula motere, "Zikomo Yesu. Ndi chinthu chabwino kukhala ndi Inu komanso kukhala mdalitso kwa anthu ena" izi zimachitika mkati koma kunja muno timalankhula motere...."Ndili mdalitso kwa inu kapena kuti "Ambuye alemekezeke. Mulungu aliwodabwitsa, sichoncho kodi?"



| | SENSI | KAGWIRITSIDWE NTCHITO UMO IMFA | CHITSANZO CHA M'BAIBOLO | SITEJI |
|---|---|---|---|---|
| 1. | MAKUTU AMKATI KHUTU LA MKATI | KULANDIRA MAWU A MULUNGU | GENESIS 12:1-3 | KATENGA PAKATI |
| 2. | MASO A MKATI 2 CHIVU LUTSO 4:1 | KULANDIRA MASO MPHENYA A MULUNGU | GENESIS 15:5-6 | |
| 3. | MALINGALIRO AMKATI LUKA 2:19 | KULINGALI MAGANIZO A MULUNGU | AROMA 4:20-21 | KUFUNGATIRA |
| | CHIFUNIRO CHA MKATI MACHITIDWE 19:21 | KULANKHULA MAWU AMULUGU | GENESIS 17:5 | |
| | ZOTSATIRA ZAKE | KUFA KWA MASOPHENYA | GENESIS 16:2<br>GENESIS 17:18-19 | KUBADWA |
| | | KUUKA KWA MASO MPHENYA | GENESIS 21:1-2<br>AGALATIYA 4:4 | |

Timaseka pamodzi ndi kukhala mu chiyamiko pamodzi ndi chikondwerero chifukwa choti timazindikira kuti adali Mulungu.

Timadziwa kuti Iye ali Alefa ndi Omega, woyamna ndi womaliza ndipo palibenso wina koma Iye yekha. Kudzidalira kwathu kwapasuka chifukwa choti watitenga ife ndi kutipyoletsa mu imfa ya masomphenya. Tikudziwa kuti chiri chifukwa chisomo chake. Ife tiri ofooka ndipo Iye ali wamphamvu. Moyo upezeka pamene kufooka kwathu kwalumikizana ndi mphamvu yake. Moyo yathu yabisika mwa Iye. Mwa ichi tikhoza kulankhula motere....."Zikomo inu."

KODI SITIOPA PAMENE KUNYADA KULOWA MWA IFE?
Ine sindikuganiza chomwecho. Ngatui tikuopa pamodzi ndi kupereka ulemu kwa Mulungu komanso kukhala naye mu chiyanjano, Iye amasamalira zina zonse. Ndimaona pamene ndikulemba kuti Iye amandikumbutsa za chimene Iye ali. Ndikayamba kuti ndikhoza kuchita zomwe ndekha, ndipo mwa ine ndekha, Iye amandiuza kuti ndigwade pansi ndipo ndilambire ndipo munthawi yotere amandikumbutsa za ubale wathu pakati pa Iye ndi ine.

Tsopano tili okonzeka kukhala mutu osati mchira-obwereketsa osati obwereka. Opatsa zipatso osati otemberedwa. Taphunzira kuyenda ndi mphamvu yodabwitsa ya Mulungu. Tsopano palibenso malire mu moyo wathu ndi Mulungu yekha. Mwa Mulungu mulibe malire. Ambuye akukhala akulankhula ndi ine kawirikawiri kulankhula motere,..."Mariko, tsopano palibe malire ena alionse mu moyo wako. Walowa tsopano mu mphamvu yanga ukulu wanga. Palibe malire tsopano mu moyo wako....."

Mchosangalatsa bwanji! Sindilinso ndi malire ndi mphamvu yanga, chiyambi changa, kufooka kwanga. Tsopano ndikhoza kulowa mu kuya kwa Mulungu. Mwayi wotani! ulemu wotani! Ulemelero ukhale ku dzina lake. Tsopano inunso mukhoza kulowa mu kupanda malire kotere komanso ukuru wa Mulungu wotere. Inunso mulibe malire mu moyo wanu. Inunso mwapatsidwa mphamvu ndi ulamuliro komanso ukuru kuposa maonekedwe. Mwawapatsidwa mphamvu ndi ulamuliro komanso ukuru kuposa maonekedwe a thupi lanu. Mwalowa tsopano mu dziko lauzimu la mphamvu ya kulenga. Mwaphunzira kubereka zolinga za Mulungu. Mwabwezeretsedwanso kukhala monga wolamulira pamodzi ndi khristu Yesu mmwambamwamba pa dzanja lamanja la Mulungu.

KUBEREKA KUMAFUNANSO KUDZIPEREKA KWAPADERA

Pa nthawi ya kubereka kwako, mphamvu zako zonse zimafunika. Uyenera kudziperka kotheratu ku icho chili pafupi kuti chibadwe. Ndi ntchito yaikuru ndi yolimba kuti ubereke mwana amene Mulungu waika mwa iwe. Mwa ichi, uyenera kuyembekezera nthawi zoterezo mu moyo mwa iwe. Mwa ichi, uyenera kuyembekezera nthawi zoterezo mu moyo wako. Uyenera kuzindikira kuti izo ndi "nthawi zake chabe." Sizikhala ku nthawi zonse. Koma uyenera kukhala wovetsera ku izo mu nthawi imene zikuberekedwa.



CHITSANZO CHANGA

Mu chaka 1987, Ambuye adayamba kulankhula kwa ine zakuyamba kupeza zi[angizo zosindikizira mabuku mu mnyumba. Tidali kuononga zikwizikwi za ndalama (ma dolla) mwezi uli wonse pa ntchito yathu yosindikiza mabuku ndipo zimaonetsa kuti pena pake tikhoza kusiya panjira. Patadutsa miyezi itatu kapena inayi yaa kulemba pamodzi ndikuchita kafukufuku, (zimene Ambuye adandiuza kuchita mu zolemba zanga), tidalingalirabe kulowa mu nyumba yina kukagwira ntchito yosindikizabe mabuku. Ndidaganiza motere,...."Tsopano ntchito yatha....."Kodi ndidali nkudabwa! Apa mutha kuona kuti ndidali wamkuru woyang'anira izi koma sindidali kudziwa kwambiri za izo. Ndidali wokhunzidwa kuona kuti ntchito yonse ikuyenda bwino poona kuti iwo amene adaziperekawo kugwira ntchitoyo adali ophunzira pamodzi ndi odziwa bwino za ntchitoyo ndipo pa chifukwa cha ichi idali kuyenda bwino kwambiri. Poonjezera apo, ndidayenera kusunga kaundula wabwino pa zinthu zimene tidagulitsa zokwanira zana kamodzi (100) zomwe tidagulitsa kwa anthu zikwizikwi. Kuti ndibereke ichi padera, nthawi yaitali. Izi zidali chomwecho popeza sindidali kuzindikira kena kalikonsee kokhudzana ndi ntchito yosindikiza mabuku (printing). Ndidayenera kukhala wodzipereka kwambiri komanso wotchera khutu kuzochitikazo. Ambuye adandilangiza kuti andipatsa chithandizo cha kumvetsa bwino. Patangodutsa nthawi, ndidayamba kudziwa bwino.

Apa mutha kuona kuti pamakhala nthawi mu moyo wako pamene ukuti ubereke ku chinthu china chake - cha uzimu - pulani ya Mulungu ndipo mu nthawi zoterzo uyenera kudzipereka kwathunthu ku zinthu zimene ukuchita. Uyenera kuzindikiranso kuti izi uchita pa nthawi yochepa basi. Udzafika mu nthawi ya mpumulo usadabereknso kanthu kena katsopano.

ZOYENERA KULEMBA

Fotokoza nthawi imene Mulungu adali nawe mkati mwa kubereka

Chaputala 11

KUBEREKA MAWU (RHEMA) PAMODZI NDI MASOMPHENYA A MULUNGU WAPHAMVU YONSE.

UFUMU WANU UDZE, KUFUNA KWANU KUCHITIKE PANSI PANO.....

Tsopano, tili nacho ichi. izi ndi zolingaza Mulungu kubadwa kupyolera wa mzimu wa Mulungu yemwe adalenga zonse amakhala mu chilengedwe chake kukwanilitsa zolinga zake. Edeni akubwezeretsedwanso,

Ichi ndi chimene aneneri adanenera. Ichi ndi chimene Yesu adaonetsera. Ichi ndi chimene dziko lapansi likusowa. Awa ndi makwanilitsidwe a zokhumba za mtima wa Mulungu. Ichi ndi chiwalitsiro cha ulemelero wa Mulungu kukhala pakati pathu. Apa ndi kugwira ntchito kwa chikhristu monga chiyenera.

Ambuye adanena kuti pamene anthu adaona machitidwe odabwitsa a Mulungu pakati pawo monga (kuchilitsidwa kwa odwala, kuturutsidwa kwa ziwanda ndi zina zotere). apa ndiye kuti ufumu wa Mulungu wa Mulungu uli pafupi. Udali pakati pawo. Udali mkati mwao. Iye adawaphunzitsa ophunzira ake kuti azipemphera motere,....Ufumu wanu udze, kufuna kwanu kuchitike monga kumwamba, chomwecho pansi pano....." Ili silidali pempho mu chilankhulo cha chigiriki. Lidangokhala ngati lamulo basi.



| | SENSI | KAGWIRITSIDWE NTCHITO UMO IMFA | CHITSANZO CHA M'BAIBOLO | SITEJI |
|---|---|---|---|---|
| 1. | MAKUTU AMKATI KHUTU LA MKATI | KULANDIRA MAWU A MULUNGU | GENESIS 12:1-3 | KATENGA PAKATI |
| 2. | MASO A MKATI 2 CHIVU LUTSO 4:1 | KULANDIRA MASO MPHENYA A MULUNGU | GENESIS 15:5-6 | |
| 3. | MALINGALIRO AMKATI LUKA 2:19 | KULINGALI MAGANIZO A MULUNGU | AROMA 4:20-21 | KUFUNGATIRA |
| | CHIFUNIRO CHA MKATI MACHITIDWE 19:21 | KULANKHULA MAWU AMULUGU | GENESIS 17:5 | |
| | ZOTSATIRA ZAKE | KUFA KWA MASOPHENYA | GENESIS 16:2 GENESIS 17:18-19 | KUBADWA |
| | | KUUKA KWA MASO MPHENYA | GENESIS 21:1-2 AGALATIYA 4:4 | |

Tsopano tiyenera kuphunzira kulankhula mwa ulamuliro pa zinthu zimene tkuona mu masomphenya muzimu kudziona izo zikumasulidwa pa dziko lapansi. Izi ndi zimene adalamulira ophunzira ake kuchita. Izi ndi zimene adachita. Izi ndi zimene tiyenera kumachita. Tsopano tikhoza kuchita izi. Taphunzira zinthu zokhazikitsa chikhulupiriro cha mtima. Mphamvu ya kulenga mwa mzimu ndipo tsopano tiri okonzeka kugwiritsa ntchito mu madera onse a moyo wathu nthawi zonse.

g. Khala mwa pemphero nthawi zonse komanso kuchokera kuchepetsa zolephera zako.

h. Uwapemphe Ambuye kuti akupatse pulani yokuteteza mu nthawi imene zinthu sizikuyenda monga udakonzera. Mulungu adali ndi pulani pamene amalenga dziko lapansi ndipo pamene munthu adachimwa ku munda wa Edeni pulani yakeyo idagwira ntchito yake.

1. Osamangoganizira kuti moyo umangokhala chabe koma iwenso uyenera kudzipereka wekha ku moyo.

2. CHUMA - Chifukwa choti ulibe ndalama (chuma), sizikutanthauza kuti siungapeze zoti uyambire zomwe ukulingalira. Maganizo pamodzi ndi fundo zabwino zimabweretsa ndalama osati ndalama kubweretsa fundo zabwino.

a. Ubwereke ndalama zochitira bizinesi ngati nkhotheka komanso kofunikira.

b. Upeze ndalama kupyolera mu kugulitsa kenakake kamene ulinako.

c. Funafuna fundo yopezera ndalama.

d. Lowa ntchito pena pake - kuti upeze ndalama

3. KUKHALA OSAZINDIKIRA - Munthu aliyense amene amayamba osazindikira amadzazindikira pamodzi ndi kupambana koposa. Mkatikati mwa munthu muyenera kukhala kufunitsitsa kulakwitsa pamene akuphunzira. Munthu akhoza kuona zinthu zoonekera kunja kupyolera mu kuchita izi:

d. Ambuye, kodi pali kena kalikonse kamene mukufuna kuti ndichite pa nthawi ino koma sindikuchita?



e. Ambuye, kodi pali pulani iliyonse imene mukufuna kuti mundipatse? Ngati zili choncho kodi ndi pulani iti?

f. Ambuye, kodi makhalidwe pamodzi ndi machitidwe anga alibwino? Kodi ndimaganizira za kufunikira kwa moyo komanso kapena kodi ndili wokonzeka kudzipereka ndekha kwanthunthu monga wantchito kwa anthu ena?

6. CHUMA - Ambuye, kodi mukufuna kuti mundipatse ndalama pa ntchito iyi motani? Kodi mukufuna ndibwereke kapena ndilowe ntchito, kapena kodi mukufuna maganizo ena apadera a kulenga ndalama omwe muli nawo muwamasule pa ntchito iyi?

KUKHALA OSAZINDIKIRA KANTHU - Ambuye kodi pali madera ena amene ndikusowa kuwazindikira kuti ndikachite moyenera ntchito iyi? Ngati zili chomwecho, chonde ndidziwitseni.

a. Ambuye, kodi mukufuna ine kupambana kapena kulephera kukwanilitsa ichi?

b. Ambuye mufuna kuti ndidzipereke kwaulere kugwirira munthu wina kuti ndiphunzire madera ena omwe ali pamaso panga? Ngati zili chomwecho, ndi yani ndingamugwirire ntchito? Ndipo liti?

c. Ambuye, kodi ndikuonetsera chidwi chofunitsitsa kuphunzira kuti mzimu mwanu uwalire pa ine?

d. Ambuye, Kodi ndikuchita mwa chikhulupiriro kukhudzana ndi izo mawika mu mtima mwanga?

3. DONGOSOLO LOLAKWIKA; Kodi uli ndi chidziwitso cha umo zinthu zikuyendera komanso kudzipereka kwako ku ichi? Dongosolo labwino zitanthauza kusankha ntchito yabwino, kupangitsa maphunziro abwino zida zake zogwirira ntchito komanso kusanja zinthu mu njira imene idzakuthandiza kukhala womasuka komanso kukhala ndi mwayi wopeza zipangizo ukusowa.

4. KUONA KUTI WAKOMANA NDI VUTO LALIKULU; Umwanye ntchito zazikuru zikuru kuti zikhala zochepa ndipo uzichite mu nthawi yochepa

a. Ayenera kudzipereka yekha kwa ulele kuti akagwire ntchito pena pake kuti akaphunzire ndi kukhala ndi chidziwitso chozama pa icho akuphunzira.

b. Akhale ndi mtima wofunitsitsa kuzindikira zimene akuphunzira.

c. Zonse uyenera kuchita mwa chikhulupiriro ndipo uzitha kuzipenya mu uzimu mwake zisadaoneke mwa thupi pamaso pa anthu onse.

d. Makalata a umboni wa kupambana pa maphunziro ako amakhala ofunikira.

ZOYENERA KUCHITA

kumbukira - Kweza maso ako pa Yesu Khristu pamene ukupemphera ndi kuika mafunso awa pamaso pa Ambuye, Upenyerere chimene lye akulankhula ndi kuchita pokhudzana ndi mafunsowo.

1. KUSAPILIRA - Ambuye, kodi ndikuyembekezera zambiri mu nthawi yochepa? Lankhulani nane kukhudzana ndi umo mukuonera.



2. ZOLINGA - Ambuye chonde ndikumbutseni zolinga mwaika mu mtima mwanga. Kodi zili zambiri bwanji? Kodi panopa ndi zichite chiyani?
3. DONGOSOLO LOLAKWIKA - Ambuye, kodi ndili ndi malo abwino ogwirira ntchito, ochitira maphunziro a ntchito komanso zipangizo zogwirira ntchito imene mukundilangiza kuti ndichite? Kodi pali kena kalikonse mukufuna kuonjezera panopa?
4. KUONA KUTI WAKOMANA NDI VUTO LALIKURU - Ambuye kodi palibe njira yina yake imene ndingamwanyire ntchito iyi? Ndionetsereni umo mukufunira kuti ndichitire bwino pa nthawi ino?
5. KUCHITA ZINTHU MOGWIRIZANA NDI NTHAWI YA MULUNGU * - Ambuye kodi zimene ndikuchita panopa zili mu nthawi yanu?
b Kodi pali china chake chimene mukufuna kundionetsera chomwe ine ndikulephera kuona?
c. Kodi pali abwenzi atsopano amene mukufuna kuti mundilozere kwa iwo? Kodi ali ayani? Kodi ndingawapeze bwanji?

B. KUCHOTSA ZINTHU ZIMENE ZICHITIKA MU UZIMU

1. MPHAMVU YA MULUNGU - Kuti ukakhale ndi zolinga za Mulungu kuyenda mu moyo wako lingalirani fundo izi:

a. Chithu chilichonse chimakhala ndi nthawi yake....." (Agalatiya 4:4). Khala wokonzekera kuchita zonse mogwiizana ndi Ambuye.

b. Khala womasuka kwa Mulungu kukuonetsera zinthu "mwa dzidzidzi zimene siudali kuziyembekezera kapena kuzifunafuna.

c. Chita zinthu mwa kulenga kuti ukathandize mu kuzindikira zako.

d. Chita zinthu mwa kulenga kuti ukathandize mu kuzindikira zako.

e. Umvetsere mwa tchutchutchu ku kulankhula kwa mzimu mkati mwako.

f. Khalani ofunitsitsa kuchita zinthu mwa chikhulupiriro.

Kukhala ndi mpingo waukuru mu dziko lonse la Korea. Pamene adali kuyesetsa kuti masomphenya awa akwanilitsidwe idafika nthawi kuti adatopa kotero kuti pakanthawi ndithu adalephera kugwira ntchito zake monga m'busa. Apa mkuti adalowa mugawo ka "kufa kwa masomphenya ake" okhala ndi mpingo waukuru mu dziko lonse la Korea. Mulungu, pa nthawi yake adayamba kukonza chotengera chake, kuchotsa kunyada konse pamodzi ndi kumveka kudzichepetsa konse Mulugu adamuuza Dr. Cho kuti patenga zaka khumi kuti lake lichilitsidwe chifukwa Iye adazindikira kuti patenga zaka khumi kuti aumbe maonekedwe pamodzi di chikhalidwe choyenera kupyolera mu zowawa zomwe Dr. Cho adali kukomana nazo.

Mu nthawi ya zaka khumi izi, Mulungu adaumba dongosolo labwino mu mpingo wa Dr. Cho lomwe lidampangitsa iye kuchita zoposa masomphenya kapena maloto omwe adali nawo. Sikuti iye wangokhala ndi mpingo waukuru ku Korea komanso kuti uli mpingo waukuru pa dziko lonse lapansi.

Zinthunzi zoterezi zimachitika mu moyo wathu pamene tikumvetsa pamodzi ndi kukhala mu njira za Mulungu komanso kulowa muchiyanjano ndi Iye mokhulupirika kuchita chili chonse chimene Iye alilamulira.

ZOYENARA KULEMBA

Uwapemphe Ambuye kuti akuonetsere pamene iwe uli mu dongosolo lotere. Lembera zimene akuyankhe.
PEMPHERO.....Ambuye tithandizeni kuti tikhale ndi masomphenya a ulemelero wa mdzukiro....."

KUDUTSA MWA CHANGU KUPYOLERA MU CHIGWA CHA IMFA

Anthu ena amakhala nthawi zonse mu imfa. Nthawi zonse amakhala akumva zowawa chifukwa cha khristu Yesu. Nthawi zonse amakhala akudutsa mu zinthu zowawa. Amaoneka nthawi



zonse kuti sakupeza dziko lolonjezedwalo. Iwo amaganiza kuti izi ndi zimene Mulungu akufuna kuti iwo akhale otero. Ine ndili ndi uthenga kwa iwo. Tiyenera kudutsa chigwa chathu cha zovuta mwasangamsanga ndi kulowa mu dziko la lonjezano la Kanani!

Ana a Israeli akadakhoza kudutsa chipululu pa masiku khumi ndi mphambu ziwiri (12) koma zidawatengera zaka makumi anayi (40). Gulu lonse limene lidaturuka dziko la Aigputo adayenera kufa mu chipululu. Sitiyenera kumango yendayenda malo amodzi mu chipululu cha phiri la Sinai. Tikhoza kuphunzira kudutsa mwachangu komanso kukhala mu zofuna ndi zolinga za Mulungu ndi kuphunzira kukhala moyo wa dziko la malonjezani mmalo mokhala mu chigwa cha mthunzi wa imfa. Mwa ichi nkofunika kuti tiphunzire kumaona mwa tchutchutchu pamodzi ndi kumavetsa komanso kumagwira bwino zokhoma (zovuta) zonse zokomana nazo pa moyo wathu wa uzimu. Pansi apa pali zinthu zingapo zovuta zomwe timakhala nazo ndipo tsopano ulembere izo cholinga cha kulemebra ndi kuthandiza kuti uzindikire umo ungapyolere mu zinthu zina zovuta ndi kulowa mu dziko loyenda mkaka ndi uchi.

KUCHOTSA ZINTHU ZIMENE ZIMALETSA MAKWANILITSIDWE A MASOMPHENYA

A- Zinthuzi zili pansi apa zimaoneka ngati zinthu zoletsa kukwanilitsidwa kwa masomphenya koma sizili chomwecho ay.

1. KUSAPIRIRA: Onetsetsani kuti usayembekezere zinthu zambiri mu nthawi yochepa. Zinthu zambiri ukufuna kukhala nazo zimafunanso nthawi yambiri kuti zichitike.

2. KUTANTHAUZILIDWA KOLAKWIKA KWA ZINTHU; Kodi uli ndi zolinga zoyenerera zimene wakhala uku dzipemperera. Kodi Mulungu wakupatsa pulani yanji yomwe tsiku ndi tsiku uyenera kuionerera? Kodi zolinga izi zili za ntheredi zoyeseka komanso zotsogozedwa ndi madeti operekedwa? Kodi wakodwa mu msampha wa zochitikachitika?

adapemphera mopsyinjika mtima, atakweza maso ake pa cholinga pamodzi ndi mphamvu ya Mulungu. Iye adapambana chifukwa cha kupemphera kwa chipsyinjo mtima. Zolinga za Mulungu zidamera mizu mu mtima Yesu ndipo chisomo chidaperekedwa kuti akapirire zowawazo. Ifenso, tiyenera kupambana nkhondoyo kupyolera mu kupemphera kopsyinjika nako. Pamene tikulira kwa Ambuye kawiri ndi kawiri, timapeza mphamvu pamodzi ndi masomphenya zikukhazikitsidwanso mozama mu mtima yathu.

APA NDI PAMENE NKHONDO IMAPAMBANIDWA KAPENA KUGONJA. APA NDI PAMENE MUNTHU AMALOWA MU CHIKHRISTU CHENICHENI KAPENA KULEPHERA KULOWAMO.

Getsemani Yesu a matikonzekera ife ku mtanda wa kalivare. Mtanda wa kalivale umatikozekera ife ku ulemelero.

Ena akhoza kumatsutsa pomanena kuti adamva zowawa ndi cholinga kuti ifeyo tisamamve zowawa. Ayi, Khristu adamva zowawa ndi cholinga kuti kumva zowawa kwathu kulumikizana ndi zowawa zake ndipo zotsatira zake chisomo cha Mulungu chikagwire ntchito.

KUMVA ZOWAWA ZA IMFA MU THUPI PAMODZI NDI KUIMA OSACHIMWA.

Mbali imodzi imene imakwanilitsidwa mu imfa ya masomphenya ndi kufa kwa umunthu wako pamodzi ndi mphamvu ya uchimo mu thupi langa - zotsatira zake ndi kukhala ndi moyo mwa chilungamo cha Khristu Yesu. Pa 1 Petro 4:1, 13....."

Apa akutifotokozera mwa tchutchutchu kuti kumva zowawa ndi mbali imodzi yagawo lathu ndipo chithu chabwino chimaturuka mwa zowawa zo pamene taika maso athu pa Yesu pamene tikuyenda mu zowawazo. (1 Petro 4:12-19). Mwa ichi, ndi chofunikira kwambiri kwa ife kuzindikira zolinga za Mulungu. Tiyenera kukhala mu chiyanjano makamaka pamene tikudutsa



mu nthawi yakufa kwa masomphenya. Mu chiyanjano timapezamo mphamvu pamodzi ndi kumvetsa bwino zotithandizira ife kupirira. Ndi kumvetsa uku, pamafika mwayi wokhala limodzi ndi Mulungu mu machita chita ake a ulemelero. Mmalo wothawa kuchokera ku imfa, tikhoza kulandira ndi manja awiri pamodzi ndi kumvetsa umodzi, komanso mphamvu kusandulika kuchokera ku ulemelero kupita ku ulemelero - pamene tikupenyerera zinthu zosaoneka ndi maso osati zimene tikuziona ndi maso athu. Apa tsopano timalowa mu chikhristu chenicheni.

KUKWANILITSIDWA MWA UZIMU KWA MASOMPHENYA

Takamba kale pang'ono za ichi mu chaputala oyambirira. Genisesi 17 ndi 18 akufotokoza za maziko a kukwanilitsidwa kwa masophenya. Chiyanjano pakati pa Mulungu ndi Abraham chidabwezeretsedwanso patadutsa zaka khumi ndi mphambu zitatu (13). Uthenga woyamba wa Mulungu kwa Abraham udali woti akhale womvera kotheratu. Uthengawo udali wotere...."Yenda pamaso panga mukhale wangwiro ....."Genesis 17:1. Mulungu adali kufuna chiyero. Iye sadamukane Abraham chifukwa choti adalemphera pamaso pake. Iye adafuna chiyero pangano lisadakwanilitsidwe. Pa Genesis 17:23, tikuona kuti Abraham adamvera Mulungu "tsiku lomwelo." Ichi chidatsegula makomo kuti Abraham ayanjanenso ndi Mulungu (Genesis 18:1). Mu chiyanjano cha nthawi iyi, Mulungu adapereka nthawi yeniyeni mnene masomphenya aja akwanilitsidwe chaka chomwecho.

Inde ndaona kuti pemphero, masalo achakudya, chiyanjano pamodzi ndi kumvera zimakonzera njira kuti chozizwa cha Mulungu chikwanilitsidwe. Chigonjetsa chilichonse kumoyo wanga chakhala zotsatira za pemphero, masalo a chakudya, chiyanjano ndi kumvera.

UMBONI WOMWE NDAONA

Ndiloleni kuti ndiperekere umboni kuchokera ku moyo wa Dr. Cho. Dr. Cho adali ndi chikhumbo pa mtima pake-masomphenya ofuna

## CHIPHUNZITSO PAMODZI NDI CHITSANZO CHA YESU

Mwa pemphero pamodzi ndi kulingalira mozama lemba Yohane 12:23-25. Kodi mavesi awa akulanhkula chiyani kwa iwe? Chilamulo cha moyo ndi choti mdzukiro wa moyo ndi zotsatira za imfa. Mbeu imadzuka kukhala mtengo itayamba yafa kaye. Yesu adzadzuka ku ulemelero atayamba wafa kaye. Mawu a Mulungu (rhema) pamodzi ndi masomphenya amadzuka atayamba afa kaye kuthupi.

Yesu adawawuza kuti Iye adzakhazikitsa ufumu. Masomphenya awa pamodzi ndi mawu (rhema) adafa mu mtima mwao pamene Yesu adapachikidwa pa mtanda - ndipo patapita masiku ochepa tsiku la pentekositi pamene Mulungu adakwanilitsa maaomphenya pamodzi ndi mawu olankhulifwa (rhema) mu njira yadabwitsa koposa chiyembekezero chawo.

## MALEMBO ENA OPATULIKA OFOTOKOZA ZA IMFA YA MASOMPHENYA

Yosefe mu nthawi ya umwana wake adapatsidwa masomphenya kuti adzalamulira abale ake. Masomphenya awa adafa pamene Yosefe adatengedwa mu ukapolo kupita ku nyumba ya mndende - chowechidali cinthu chosonyeza kuti kudali kosatheka kuti masomphenya aja akwanilitsidwe. Kupyolera mu zokhoma ndi zovuta zotere, Mulungu adagwira ntchito yomukonza komanso kumpatsa kudzichepetsa ndi cholinga kuti mu nthawi yake ya kuikira Mulungu akwanilitse pamodzi ndi kubweretsa masomphenya aja ku moyo (mzukiro). Tsopano Mulungu adaika munthu wofatsa ndi wodzichepetsa uyo mu utsogoleri. Mulungu nthawi zonse amachita zofuna zake ndi zolinga zake kupyolera mu imfa ya masomphenya.

Mose adapatsidwa ulamuliro kukaombola ana a Israeki mu ukapolo waku Aiguputo. Tsono iye, mwa thupi adapita kukapha mu aigupto yemwe adachita nkhondo ndi munthu wa fuko la



Israeli. Mulungu adamutsogolera iye kukakhala ku chipululu pa zaka makumu anayi (40) kumene Iye adakamuzamitsa pamodzi ndi kumuphunzitsa mose njira zake za Mulungu. Pomaliza pake Mulungu adakwanilitsa masomphenya ake. Izi ndi zitsanzo zochepa za imfa yamasomphenya mu malembo opatulika. Upeze zina zoonjezera apa pamene ukusanthula malembo opatulika.

## UMO UNGAPAMBANIRE KUPYOLERA MU IMFA

Pamene tiganizira imfa, ndichithu chopweteka, chosankhulupirika. Akhristu ambiri satenga mtanda wao, osazindikira zolinga za Mulungu kapena kuona mdzukiro wa ulemelero umene Mulungu adzaonetsera patsogolo pake. Ichi ndi chifukwa chake akhristu ambiri sapyolera kufikira ku kuzama kwa chikhristu koma a mangokhala pakati kati pa kukwanilitsa kusenza mtanda wa Yesu ndi kukhala wofewa. Yesu adapirira kusenza mtanda. Lembani pa Aheberi 12:2, kuti muone umo adachitira, Yesu sadaike maso ake pa mtanda. Inde, Iye adayenera kuyenda nawo ndipo indedi, chidali chinthu chowawa. Koma palibe moyo pokungomamatira mtanda.

## MUNTHU AMAPEZA MPHAMVU ZOMWE AKUSOWA KUTI APAMBANE KUPYOLERA MU KUPENYERERA CHIMENE CHIDAIKIDWA PAMASO PAKE.

Maso anga ayenera kupenyerera pa zolinga za Mulungu zomwe zikwanilitsidwe pamene masomphenya aja adzuka. Yesu amapenyerera kupyolera pa mtanda wa kalivale ku kudzuka kwa ulemelero ndipo masomphenya pamodzi ndi chimwemwe zidampatsa Iye mphamvu kuti akapilire mtandawo.

....."Ndi kupenyerera woyambira ndi womaliza wa chikhulupiriro chathu Yesu,....."(Aheberi 12:2).

Munthu amayesedwa popenyerera maso ake kulemera kwa mtanda pamene akupyola kudzera mu imfa. Ngati munthu angachite izi alephera mosakaikira. Yesu anapita ku munda wa Getseman ndipo

Chitsanzo chathu changwiro. Iye amalankhula zokhazo zimene amamva kwa Atate ndi kumachita zokhazo zimene amaona Atate akuchita, ndipo pakutero adakhala ngati mulato waphamvu ya kulenga ndi kuchilitsa pamodzi ndi kuombola kupereka nzeru ya Umulungu pamalo pamene ikusoweka.Ine ndakopeka mtima kuti pamene tikutsatira chitsanzo chake cha moyo wake muchikhalidwe pamodzi ndi kalankhulidwe ka zokhazo zochokera kwa Atate, ifenso tidzakhala pamodzi ndi kuyenda monga Yesu adachitira.

KUFA KWA MASOMPHENYA - KUONETSEDWA MU MOYO WA ABRAHAM

Pali chinthu chimodzi chowawa chimene timakomana nacho izi zisadachitike u moyo wathu. Uko ndi kufa pamodzi ndi kuuka kwa masomphenya.

Tiyeni tione pa Abraham. Iye adalandira lonjezo la chikhulupiro chomwe iye adafungatira pa zaka makumi awiri ndi mphambu zisanu (25). Chonde lembeni Genesis 21:5.
Abraham adaona chimene tingachitche kuti "kufakwa masomphenya." Mu njira za Mulungu tikhoza kuona kuti Mulungu amatidutsitsa mu masitepe atatu (1) kubadwa kwa masomphenya (2) kufa kwa masomphenya (3) kukwanilitsidwa kwa masomphenya.

Mulungu amabereka masomphenya powapereka kwa ife. Ife tsopano timayesetsa kuwakwanilitsa mu mphavu zathu uko ndiko kugawana ndi ulemeleo wonse wake. Ulemelero wonse umakhala wa kwa Mulungu. Mulungu sadapatse ife chipembedzo chapadera cha thupi chimene tikhoza kukwanilitsa mwa mphamvu za ife tokha Chikhristu chimaposa malamulo a zipembedzo koma kuti chimaonetsera mphamvu ya Mulungu.

Taonani umo Abraham pamodzi ndi Sara adafuna kukwanilitsa masomphenya a Mulungu mu njira yao yathupi chifukwa cholephera ku kulirira pa kudikira pa ambuye - ndipo adabereka



Ishimaeli kupyolera mwa mdzakazi wa Sara - hagai (Genesis 16). Pataditsa zaka khumi ndi zitatu (13 Abraham amayembekezera kuti njira yake adachita idali yokhonzeka pamaso pa Mulungu (Genesis 17:18-19 monga akulankhula motere "Ha! Ishamaeli akhale ndi moyo pamaso panu/....."

Koma Mulungu anati "Ayi". Pa nthawi iyi, Abraham adali ndi zaka makumi asanu ndi anayi kuphatikizapo mphambu zisanu ndi zinayi. (99). Padalibe njira iliyonse malingana ndi chikhalidwe cha chilengedwe cha thupi kuti masomphenya awo akadakwanilitsidwa. Masophenya adafa ndipo Abraham adayeneranso kuti iye afe ku umunthu wake. Palibe chinachilichonse chimene iye akadachita koposa kungodikira pa Mulungu ndi kukhala womvera kwa Iye ndipo ichi Abraham adachita. Mulungu adalankhulanso kawiri kupereka malamulo amene Abraham adawatsatira msangamsanga zomwe zidamupangitsa Mulungu kulankhulanso kawiri -kumulonjeza iye kuti adzakhale ndi mwana mkati mwa chakacho (Genesis 17, 18).

Atatha kufa masomphenya, tsopano inafika nthawi ya kukwailitsidwa kwake ngati tikhalabe tikupitiriza kufuna Mulungu pamodzi ndi kuvera Iye mu nthawi ya kuyesedwa kotere.

Sikuti Abraham akadangofa kumasomphenya ake kamodzi kokha komanso Mulungu adamuitana kuti apereke masomphenyawo. Mulungu adampempha Abraham kuti apereke Isaki paguwa lansembe. Pa nthawi iyi, Abraham adali atakulanso nsinkhu mu chidziwitso cha njira za Mulungu. Iye adazindikira kuti monga masomphenya adafa mwa iye Mulungu akadakhozanso kukwanilitsa kwake kuchokera ku masophenyawo. Lemba maganizo a Abraham amene ali pa Ahebeeri 11:19).
Mulungu amatilola kuti masomphenya ake afe nthawi zambirir kuti tizindikire kuti ali osati kuti ali athu. Komanso kuti ali Iye osati ife kuti Iye akalemezedwe mu zonse.

CHAPUTALA 10

## KUFA PAMODZI NDI MDZUKIRO WA MASOPHENYA MAWU OYAMBA - KUBWEREZANSO KWA DONGOSOLO

Pomaliza tikubwera kuyandikira kwa kukhazikitsidwa kwa chikhulupiriro cha mtima. Tisadayambe kulandira lonjezano la Mulungu, timayamba kaye tapyola pa kuona kufa kwa masomphenya. Koma tisadafike apa tiyeni poyamba tibwezerenso kuona ndondomeko taona kale lija.

Tidayamba kuona za masomphenya aokhazikitsidwa mu mitima yathu ndi Mulungu. Zinthu izi timazifungatira mkati mwathu. Tidadzadza malingaliro a mkati chifuniro, machitachita pamodzi ndi mawu a Mulungu kuphatikizapo masomphenya. Tidalingalira mozama za izi, kudzilola kuti zikule kufikira zibadwa mu nthawi yake monga tichitira mwana wakhanda.

Monga Dotolo Cho akulankhula kuti kena kalikonse kamene kamafungatiridwa mu chigawo cha chinayi cha miyambi, kumalengedwa mu chigawo chachitatu cha miyamba. Kapena tikhoza mu njira yina, kulankhula motere, kuti pamene tafungatira masomphenya pamodzi ndi (rhema) mawu a Mulungu mu mizimu yathu, tidzaona kuti aberekedwa mu dziko limene tikukhala.

Izi zitanthauza kuti pamene tikufangatira mawu olenga pamodzi ndi masomphenya a Mulungu, ifenso timasanduka kukhala olenga. Timakhala ngati Yesu.



| | SENSI | KAGWIRITSIDWE NTCHITO UMO IMFA | CHITSANZO CHA M'BAIBOLO | SITEJI |
|---|---|---|---|---|
| 1. | MAKUTU AMKATI KHUTU LA MKATI | KULANDIRA MAWU A MULUNGU | GENESIS 12:1-3 | KATENGA PAKATI |
| 2. | MASO A MKATI 2 CHIVU LUTSO 4:1 | KULANDIRA MASO MPHENYA A MULUNGU | GENESIS 15:5-6 | |
| 3. | MALINGALIRO AMKATI LUKA 2:19 | KULINGALI MAGANIZO A MULUNGU | AROMA 4:20-21 | KUFUNGATIRA |
| | CHIFUNIRO CHA MKATI MACHITIDWE 19:21 | KULANKHULA MAWU AMULUGU | GENESIS 17:5 | |
| ZOTSATIRA ZAKE | | KUFA KWA MASOPHENYA | GENESIS 16:2<br>GENESIS 17:18-19 | KUBADWA |
| | | KUUKA KWA MASO MPHENYA | GENESIS 21:1-2<br>AGALATIYA 4:4 | |

4. Gwiritsa ntchito njira izi kuchepetsa anthu oyimba lamya (telefoni)

a. Gwiritsa ntchito lamya (telefoni) mmalo molemba makalata

b. Mauthenga onse omwe ukufuna kutumiza pa lamya (telefoni) uyenera kuwasonkhanitsa pamodzi - nthawi ya mmawa

c. Yesetsa kupeeka lamulo kuti lamya zonse zizitenga mphindi zitatu zokha basi

d. Ngati nkhoteka, ukhale ndi munthu wolandirira ma telefoni (lamya) kuti adziwafitikozera za iwe.

e. Ulembe fundo zonse ukufuna kulankhula usadachite lamya (telefoni)

5. kabisale malo ena ake pamene ukufuna kuti wina asakusokonezere nthawi yako. pita kuchipinda chapadera kusunga abuku, ofesi yapadera, chipinda cha mu hotelo, kapena magalimoto yako

6. Ntchito yonse idakhalira osachitika onetsetsa kuti wachita osachedwetsa.

D. KODI UKHOZA KUDULIZA CHILI CHONSE MWA IZI?

1. Nthawi imene uagwiritsa ntchito pogona?

2. Nthawi imene umagwiritsa ntchito poonera televivyoni

ZOYENERA KUTI ULEMBE

1. Ambuye, Kodi ndikungokhala wotangwanika chabe koma wosapindula? Kodi zinthu zina zimene mukufuna kukonza mwa ine kuti ndisangokhala wotangwanika komanso wopindula?



2. Ambuye, Kodi pali njira iliyonse yapadera imene ndikhoza kugwiritsa ntchito imene ndikugwira yogwirizana ndi nthawi imene ndimakhala nayo pa tsiku?
3. Ambuye kodi ndimakhala ndi nthawi yokwanira yopumitsa ubongo nkumacheza ndi banja langa?
4. Ambuye Kodi matsogoleredwe ku chinthu chofunikira kapena chokukhala kuti chikufuna changu?
5. Ambuye, Kodi ndimasiya osachita zimene sindikadayenera kuchita?
6. Ambuye, Kodi ndi kutha kuletsa anthu omangofuna kundiyendera basi opanda zifukwa zenizeni ku ofesi yanga kapena kumayimba lamya (telefoni) moyenera?
7. Ambuye, Kodi ndikutha kugwiritsa ntchito nthawi yogona ndi yoonera televivyoni moyenera?

SITEJIYACHITATU - KUBADWA KWA CHOZIZWITSA

DIAGRAM

".....Koma pokwaniridwa nthawi Mulungu adatumiza mwana wake" (Agalatiya 4:4)

2. Ukhale ndi nthawi yapadera ya chete tsiku ndi tsiku imene udzimvetsera kuchimene Mulungu akukulankhula kukhudzana ndi moyo wako komanso zimene ukuchita.

3. Ulembe zolinga zako zofunikira zokhazokha tsikulo monga zoyambirira kuzikonza zonse ukuchita mu dongosolo. Mu njira yotere, ngati zonse sizichitika komabe zofunikira zokhazo wazikwanilitsa.

4. Ntxchito iliyonse uonetsetse kuti ikugwirizana ndi nthawi pa tsikulo pamene upindule kwambiri pokwanilitsa ntchito yotere.

5. Uyesetse kuti mapulogalamu ako akhale osathina kwambiri ndi cholinga choti Mulungu, anthu, kapena zovuta zina, zikhoza kusuntha mapulogalamuwo.

6.Ukhale ndi nthawi yomacheza - kupumitsa bongo ndi cholinga kuti mtima wako ukhoza kufungatira zinthu za Mulungu zimene waika mwa iwe.

7. Ufunefune njira kuti ukagwiritsire ntchito nthawi imene simuli siikugwiritsidwa ntchito kwambiri.

C - KUCHEPETSA ZINTHU ZOSOKONEZA PAMODZI NDI ZOTSEKEREZA

1. Ufunse: "Kodi ichi ndi choti chichitike mwa changu kapena ndi chofunikira, kapena chili zonse ziwiri?" Zindikira kuti nthawi zonse zinthu za changu sizikhala zabwino.

2. Kena kuti "Ayi" ku zinthu zomwe ukuona kuti Mulungu sakufuna kuti uchite pa nthawi imeneyo pa moyo wako. Zinthu onga izi nkoyenera kuzisiya osachita:



a. zinthu zonse zazing'onozing'ono

b. Ntchito yina iliyonse imene mphindu lake ndi lochepa

c. Chimene ukhoza kupereka kwa munthu wina kuti achite.

d. Zimene umachita pofungofuna kusangalatsa anthu ena chifukwa cha mantha kuti akuweruza.

e. Zinthu zosakhala pa pulogalamu kapena zopemphedwa zosayenera zomwe zingadye nthawi yako chabe.

f. Chilichonse chimene ena mwa iwoakhoza kuchita mwa iwo okha.

3. Ngati ukugwira ntchito mu ofesi, gwiritsa ntchito njira zotsekereza anthu odzakuona chabe monga izi:

a. Tseka chitseko pamene ukugwira ntchito yofunika kuti ukhale wekha.

b. Uchotse mipando yapadera mu ofesi yako kapena pamene ukugwira ntchito.

c. Ngati wina akufuna kuti akuone, pita kumene ali ndipo ukalankhule naye.

d. Ngati ukusokonezedwa ndi anthu ofuna kuti athandizidwee ku mavuto awo, uwauze kuti azilemba mavuto awo pa pepala

e. Gwiritsa ntchito mawu a ulamuliro.

f. tebulo lako al mu ofesi liyang'ane kolowera anthu

g. Ukhale ndi mlembi yemwe adziwafotokozera alendo onse za iwe

h. Gwiritsa ntchito nthawi ya chakudya cha mmawa kapena chamasana kulankhulana ndi alendo okhawo ofunikira kwambiri.

Ukhoza kulemba pa pepala lapadera kugwiritsa ntchito kupyolera mu masitepe a pa chinthunzi ichi ntchito iliyonse imene Mulungu wakupatsa pasiteji iliyonse, uyenera kulemba zonse zochitika. Mu njira yotere, udzakhala ndi malingaliro a Mulungu mmalo mwa ako.

DONGOSOLO LA PULANI






KUGWIRITSA NTCHITO NTHAWI MOYENERA

Kupindula kumatengeranso kagwiritsidwe ntchito kabwino kanthawi imene Mulungu watipatsa. Kagwiritsidwe ntchito kabwino ka nthawi kamatipatsa ufulu wochuluka mmalo mwa wamalire. Tidzaona kuti tikugwirizana ndipo tikugwira ntchito moyenera osati movuta.

TIYENERA KUKHALA OPINDULA OSATI KUTANGWANIKA CHABE

Kupindula kumatengeranso kagwiritsidwe ntchito kabwino kanthawi imene Mulungu watipatsa. Kagwiritsidwe ntchito kabwino ka nthawi kamatipatsa ufulu wochuluka mmalo mwa wamalire. Tidzaona kuti tikugwirizana ndipo tikugwira ntchito moyenera osati movuta.

TIYENERA KUKHALA OPINDULA OSATI KUTANGWANIKA CHABE

1. Usasokoneze pakati pa kutangwanika ndikukhala waphindu.

2. Kukhala waphindu ndi mbali ya zotsatira za ntchito yabwino pa nthawi yake yoyenera, kugwiritsa ntchito maganizo abwino, ndikukhala ndi zinthu zokuyenereza (chuma)-apa ukwanilitsa zofuna zako.

3. Kukhala waphindu ndi wamphamvu kutanthauza kugwiritsa ntchito nthawi yako ku zomwe zili zofunikira dongosolo la Mulungu kukhudzana ndi lako ndipo uzipeze zinthuzo.

4. Yesu sadali munthu wothamanga (changu) pochita zinthu kapena wa chidodo koma kuti adali kupindula pa zimene amachita komanso zonse zimene Mulungu amafuna pa moyo wake.

B - ZIDA ZOGWIRITSIRA NTCHITO POONJEZERA PHINDU POGWIITSA NTCHITO NTHAWI

1. Pa chaka chonse udzipatula sabata  imodzi yosanthula umo ukugwiritsira ntchito nthawi.

Kenako masomphenya adoneka ndipo ndidaona mzimu woyera atamufungatira iye koma siudalowe chifukwa choti padali zovuta zina zomwe zimachitika mu mtima mwake. Ndidadabwitsidwa kwambiri ndipo ndidafuna kuwakama masomphenya chifukwa ndimaona kuti sizingakhale zoona.

Ndidatsimikiza mtima kuti munthuyo wangopulumuka kumene. Nchifukwa chiyani mzimu woyera ukukhala kunja kwa iye osalowa mkati mwa moyo wake?

Ndidatsegula maso anga ndipo ndidafunsa ngati kena kalikonse kadamuchitikira chifukwa ndimakhulupirira kuti pamene munthu wapulumutsidwa, mzimu woyera ammachitira umboni ndi mzimu wake kuti ali tsopano mwana wa Mulungu. Ngati mzimu woyera sakuchiitira umboni mkati mwake ndine yani kuti ndimuuza kuti mzimu woyera ali pakati pathu? Mwa ichi ndimakhulupirira kuti munthu wapulumutsidwa kumene ayenera kuona kanthu kena kake osati mu moyo koma mu mzimu mwake. Munthuyo adakweza nkhope nati, "palibe chimene ndachiona." Apa ndidakhala chete kusowa cholankhula. Ichi chidapasula chidziwitso changa pa za uzimu.

Malingana ndi zonse ndidaphunzira, munthuyo adayenera kupulumutsidwa ndipo adayenera kuona kanthu kena kake ka chilendo mu mzimu wake Komabe kuvomereza kwake kudagwirizana ndi masomphenya amene ndidaona. Mwa ichi ndidalankhula kwa iye motere, "Inenso sindinaone kena kalilonse." Keneko Ambuye adavumbulutsa kuti munthuyo adali pa chikondi ndi msungwana wina ndipo amakoza dongosolo kuti asiyane ndi mkazi wake kuti atenge msungwanayo. Ndidamuuza kuti iye wasankha kuti Yesu akhalembuye pamodzi ndi mpulumutsi wake, ayenera kuthetsa chibwenzicho ndipo akhale ndi mkazi wake woyamba basi. Iye adanena kuti sangathe kuchita zimenezo. Ine ndidamuyankha kuti Ambuye sangamulandire kuti akhale mpulumutsi wake.



Masomphenya a Mulungu aja adapherezedwa apa. Nkofunika kutsatira chilichonse chomwe masomphenya aonetsa pamodzi ndi kuchikwanilitsa ndipo pakutero Mulungu adzavumbulutsa choonadi chake chobisika.

## ZOYENERA KUWERENGA - AHEBERI 11 CHAPUTALA CHOYAMBA ZA CHIKHULUPIRIRO

Werengani Aheberi 11 - chaputala choyamba za chikhulupiriro pafupifupi kanayi konse pang'ono, komanso mwa pemphero ndipo ulembe izi.

1. Mukuwerenga kwako poyambirirra lembera ntchito zomwe chikhulupiriro chidachita.
2. Mu kuwerenga kwako kwachiwiri, lembera chokhudzana ndi kumwalira mwa chikhulupiriro opanda kulandira malonjezano a Mulungu.
3. Mu kuwerenga kwako kwachitatu, lembera kuona kwa anthu a dziko lapansi kukhudzana anthu asakuona kwa ulungu kukhudzana ndi anthu awa.
4. Mu kuwerenga kwako kwa chinayi, lembera chidziwitso chilichonse chimene Mulungu wakupatsa ukuwerenga mwa pemphero uku ukudikira vumbulutso. Kodi Mulungu akulankhula chiyani lero kwa iwe pamene ukulawa mu uzimu wakuchita chikhulupiriro?

PEMPHERO....."Ambuye takhala anthu opusa padziko lapansi pa nthawi yaitali. tsopano tiloleni kukhala opusa chifukwa cha inu....."

Pa tsamba lotsatirali, mupeza chinthunzi cha umo ungachitire ndi loto kapena masomphenya kuyambira pa "kukhala ndi pakati nawo" mpaka nthawi ya "kubereka" aloto kapena masomphenya. Ichi chidakozedwa ndi gulu la anthu (bungwe) lotchedwa "THE LEADER'S GROUP, INC ndipo chidaonjezeredwa ndi cholinga chakupatsa chinthunzi chabwino cha njira yake yokonzera dongosolo la kubadwa kwa masomphenya ochokera kwa Mulungu.

kutipangitsa kuti tichitepo kanthu kena kake. Koma pamene mkati mwa mitima yathu muyamba kukhudzidwa ndi chifundo, kukhudzana ndi vutolo, tidzaona kuti tokha timayamba kuchitapo kanthu kena kake pa vutolo. Machitachita awa ali ntchito zotsatira za kukhudzidwa kwa mkati.

Fundo yina yomaliza. Sikuti ntchito zathu zimangochokera ku kukhudzidwa kwa mzimu wathu komanso kuti machitachita awa amatsitsimutsidwa ndi masomphenya. Zithunzi mutu mwathu zimatikangamiza ife kupambana ndi mawu olankhula chabe. Chinthunzi chimakhuza machitachita amtima kwambiri kuposa maganizo chabe. Ndikhozanso kulankhula motere kuti mlaliki aliyense amene amakhudza mtima wako komanso kutakasa ine ndi yekhayo amene amalankhula mwa mafanizo ndi kukujambula zinthunzi kukulowetsa iwe mu izo.

Machitachita athu amayendera limodzi ndi masomphenya mwa ichi pamene uli ndi masomphenya a Mulungu mu mtima mwako, machitachita a mtima wako amamasuka pa zimene ukuona ndipo kenako zimakutsogolera kuchitapo kanthu.

## NTCHITO ZIMACHOKERA KU MACHITACHITA PAMODZI NDI MASOMPHENYA A MULUNGU

Tsopano tiyeni tibwere kwa Abraham. Mulungu adaonekera kwa Abraham ali ndi zaka 99 za kubadwa. Mau (rhema) amene Iye adalankhula adasungika mu masomphenya. Mulungu adapereka langizo lapadera kukhudzana ndi mdulidwe. Ngati Abraham sakadafungatira malonjezano pamodzi ndi masomphenya a Mulungu, sindikukhulupirira kuti akadachita zimene Iye adachita. Ine ndikukhulupirira kuti akadachita zimene Iye adachita. Ine ndikukhulupirira kuti kuonekera kwa Mulungu pamodzi ndi kulankhula kwa mawu ake kudatakasa mtima wa Abraham kumpangitsa kuti achite kathu kake. Machitachita achikhulupiriro awa adapangitsa Mulungu kuti abwererenso kawiri ndipo pa ulendo uwu ndi lonjezano kuti iye (Abraham) adzakhala ndi mwana mkati mwa chaka chomwecho.



Chikhulupiriro nthawi zonse chiyenera kukutsogolera kuchita kanthu kena kake. Chikhulupiriro cha Pettro chidampangitsa kutii ayende pa madzi. Anthu akhate khummi adauzidwa kupita ndipo ali mkati mopita adachilitsidwa. Rahabi mkazi wadamayo adabisa anthu awiri omwe adabwera kudzazonda. Yakobo akulankhula kuti chikhulupiriro chopanda ntchito chili chakufa (Yakobo 2:22, 26).

Nthawi zambiri za chikhulupiriro zimakhala zosamveka ku umunthu wa munthu. Zitsanzo za izi ndi monga; kulowa kwa ana a Israeli ku zungulira Yeriko, Namani adapita kukasamba kasanu ndi kawiri mu mtsinje wa Yordano ndipo khate lake lidachilitsidwa, munthu wankhungu kuuzidwa kuti akasambe ku Siolamu, ndipo akhate khumi amene adauzidwa kuti akazionetse okha ansembe pa nthawiyo mmene adali ndi nkhate. Ntchito za chikhulupiriro zidapangitsa kuti zodabwitsa za Mulungu zionekera.

Kalikonse kamene Mulungu akukuuza kuti uchite monga mwa chikhulupiriro uyenera kukwanilitsa kuti chodabwitsa cha Mulungu chichitike.

## CHITSANZO CHANGA

Ndiloleni kugawana nanu mawu nthawi yina yake pamene ndinaoneka wopusa pochita masomphenya amene Mulungu adandionetsera. Ndidali nditangotsiriza kumutsogolera munthu wina wake kwa Ambuye. Ndidamulankhula mwa tchutchutchu kufunikira kolapa mozama ndi cholinga kuti asangozinyenga chabe kuti ali wopulumutsidwa ndi uthenga wozizira omwe akulalikidwa masiku ano. Ndidamuuza kuti aonetsetse kuti wapereka moyo wake pamaso pa Ambuye Yesu - komanso kupyolera mu kutaya moyo mwake adzaupeza. Iye adapemphera pemphero la kulapa pamodzi ndi kupereka moyo wake kwa Ambuye Yesu. Pamene tidakhala pansi kusanthula malembo, ndi damva kukoma kwambiri mu moyo wanga. Ndidazindikira mu moyo wanga kuti munthuyo adalapadi ndipo adatembenukadi. Adakali mkati mogwetsa nkhope yake pansi, ndidayesera kubweza maso a mkati mwanga kwa Ambuye kuti ndione ngati pali kena kake kamene Iye amafuna kuti andionetsere.

Chaputala 9

KUDZADZA SENSI YAKO YACHISANU YA MZIMU WA MUNTHU POCHITA MWA CHIKHULUPIRIRO

Mzimu wa munthu uli ndi machitachita!
- tsopano tafika kusensi ya chisanu ya mzimu wa munthu - mphamvu yozindikira machitachita. Ndidali wodabwitsidwa kuona kuti mzimu wa munthu udali ndi mphamvu ya kuzindikira machitachita. Ndimadziwa kuti munthu akhoza kuona mmachitachita ndi moyo wake koma sindidali kuzindikira kuti machitachita onse amene amakhudza chikhalidwe changa pamodzi ndi ntchito zanga amachokera ku mzimu wanga. Tiyeni tisanthule ndi kuona zimene baibulo likulankhula kukhudzana ndi machitachita ochokera ku mtima wako kapena mzimu wako.
.....Mzimu wa Ahabu udachita msunamu chifukwa sadapeze chimene iye amafuna (1 mafumu 21:5).
.....Pamene adamva Yesu akuvumbulutsa malembo, mitima yao idatentha mkati mwa (luka 24:32).
.....Mulungu adaumitsa Ezekieli kumtumiza ndi mzimu wowawidwa, wonyuka mtima..... (Ezekieli 3:8, 14)

| | SENSI | KAGWIRITSIDWE NTCHITO UMO IMFA | CHITSANZO CHA M'BAIBOLO | SITEJI |
|---|---|---|---|---|
| 1. | MAKUTU AMKATI KHUTU LA MKATI | KULANDIRA MAWU A MULUNGU | GENESIS 12:1-3 | KATENGA PAKATI |
| 2. | MASO A MKATI 2 CHIVU LUTSO 4:1 | KULANDIRA MASO MPHENYA A MULUNGU | GENESIS 15:5-6 | |
| 3. | MALINGALIRO AMKATI LUKA 2:19 | KULINGALI MAGANIZO A MULUNGU | AROMA 4:20-21 | KUFUNGATIRA |
| | CHIFUNIRO CHA MKATI MACHITIDWE 19:21 | KULANKHULA MAWU AMULUGU | GENESIS 17:5 | |
| ZOTSATIRA ZAKE | | KUFA KWA MASOPHENYA | GENESIS 16:2<br>GENESIS 17:18-19 | KUBADWA |
| | | KUUKA KWA MASO MPHENYA | GENESIS 21:1-2<br>AGALATIYA 4:4 | |



Mu fundo zonse izi ili yonse payokha, tikutha kuona machitachita mu mzimu wa munthu koposa mu moyo wake. Pali mavesi ena ambiri amene amafotokoza za machitachita a mtima wa munthu kapena mzimu wake. Apa tiri ndi ena mwa iwo kuti uwerenge (Genesis 41:8, Masalimo 142:3, Danieli 7:15, Ekisodo 6:9, Miyambo 15:13, Yohane 11:33, 1 Samueli 1:15, Mlaliki 10:4, Machitidwe 17:16, Yobu 21:4, Yesaya 19:3, Genesis 45:26, Masalimo 34:18, Yesaya 54:6)

Kuchokera lu malembo opatulika awa titha kuona machitachita ochokera ku mzimu wa munthu. Mneneri Nee akulankhula motere, "machitachita awa ali mipata cha mzimu." Tikhozanso kulankhula motere kuti machitachita ozama ali njira kapena malo kupyolera mmene mzimu woyera umayenda mwa ife. Fundo iyi idanditsegulanso maso mwapadera komanso kuzamitsa kumvetsa kwanga pa mawu a Mulungu. Poyamba penipeni ndidali osalabadira machitachita anga poganizira kuti ndi zofuna za moyo chabe ndipo zosafunika pa moyo wachikhristu. Panopa ndiku kuona kuti machitachita amzimu ali ofunikira komanso oyenera kukhala nawo pa moyo wa chikhristu.

Njira yolekanitsa pakati pa moyo ndi mzimu ndi iyi: "chimene chimachokera mu moyo chili chakunja chokhoza kusinthika koma icho chimachokera mu mzimu chili chogwirika komanso chozama ndi chosinthika." Ndikhulupirira kuti Paulo adagawa machita chita a moyo amzimu pa 2 Akorinto 4:8 pamene adalankhula motere,....."ndife osautska, monsemo, koma osapsyinjika koma osakhala kakasi....." Moyo wa Paulo udali kuzuzuka koma mzimu wake siudali wopsyinjika. Onse awa ali machitachita Paulo akulankhula pa vesi 6 kuti chiwalitsiro cha yesu Khristu mkati mwa mtima wake sichikadakhoza kulola koma mtima wake udali wozuzika di zinthu zomwe zimachitikira.

Miyoyo yathu pamodzi ndi mizimu yathu yakhala ndi machitachita ozama. Mizimu yathu ndi imene amatitsogolera ife kuchita kanthu kena kake. Mwa chitsanzo, tikhoza kudziwa kuti pali ana penapake akuzuzika pa dziko lino lapansi koma chidziwitso ichi sichingathe

kudziwika kwa ziwalo zonse za gululi kwa ine?

KUKHAZIKITSA ANTHU OKUTHANDIZA

1. Ulingalire munthu amene akuona kuti akhoza kukuthandiza

2. Ukambilane ndi amzako fundo zako. Kenako uone zimene iwo akhoza kukuthandiza

3.Yamba tsopano kumafunafuna anthu kapena mabungwe amene akhoza kugwirtsa ntchito fundo zako.

4. Ulankhulane ndi anthu a chilendo amene ungathe kukomana nawo

5. Pita kumene ukuona kuti zikatheka zimene ukulingalira.

ZOYENERA KULEMBA

Ambuye, Kodi ndi anthu ati amene ndikuwadziwa amene akhoza kundithandiza?

Ambuye, ndi ndani mwa anzanga amene ndingakambilane nawo fundo iyi kapena masomphenya awa?

Ambuye, Ndi bungwe liti likhoza kundithandiza kukwanilitsa fundo kapena masomphenya awa?

Lembera fundo zonse pamodzi ndi anthu amene wakamba nawo kuphatikizapo alendo amene wakamba nawo. Kenako, uwafunse Ambuye kuti akuonetsere anthu amene ukhoza kugwira nawo ntchito.

Ambuye, malo ake abwino (kumidzi mu mzinda) ndi ati kumene nditha kakwanilitse izi?



KUPEREKA ZOPEZA ZAKO ZONSE KUTI ZIONEDWENSO

Tisadafike kuchaputala 9 chomwe chili "kuchita monga mwa mawu (rhema) ndi masomphenya," tsopano ndi nthawi kuti tilembe mwa chidule pamodzi ripoti la masomphenya, cholinga pamodzi ndi masitepe amene uyenera kuyendamo.

Tsono utenge ripoti ili ndipo upereke kwa munthu amene watsimikizirika kukhala waluntha ndi wodziwa bwino kumadera otere kuti asanthule pamodzi ndikuikira umboni kuti zilibwino. Onetsetsa kuti munthuyo ali woyenera ndipo wa luntha lake. Ngati mu dera lako muli anthu ambiri ozama, upereke ripotilo kwa aliyense wa awa malingana ndi dera lomwe iye akuzindikira bwino.

Kuti anthu awa uwapeze, uyambe waganizira iwo amene ukuwadziwa kuti ali ozama mu madera onse amene ukudziwa. Uwapemphe kuti akomane nawe kuti akomane kuti akupatse ndemanga zao pa ripoti lakolo. Ngati ali ndi maganizo apadera, yensetsa monga ungathere kusanthulanso dongosolo lako kukwanilitsa masomphenya ako posakaniza ndi maganizo awo.

Nkoyeneranso kuti utenge ripoti lako kwa munthu amene amakutsutsa kwambiri.

Umpatse iye ndipo umpemphe iye kuti akuonetse madera onse ofooka amene iye akuwaona mu ripotilo. Funafuna kusanthulanso zolemba zako mu madera onse amene iye wapeza ofooka.

Nchachidziwikire apa akupemphedwa kugwira ntchito yaikuru. Tiyenera kuzindikira kuti kupambana kumafunika kugwira ntchito kwambiri. Ngati ungatsatire njira izi mpaka kumapeto, kutsatira sitepe ili yonse mu chidzalo chake pamodzi ndi pemphero mu chitsogozo cha Ambuye Yesu komanso kusanthula osatopa ayi - kufikira ukabereka maganizo enieni omwe ali yankho ku mavuto ukakomana nawo. Sikuti udzangopindula iwe wekha komanso dziko limene ukutumikira ndi mphamvu zako lidzadalitsikanso.

3. Kuwavomereza anthu kupereka fundo zawo komanso kuwapatsa mpata kuti akhale nawo pa zinthu zokhudza chitukuko.

4. Ngati nkotheka, tambasula fundo zokhudzana pang'ono

5. Kukonza fundo zina zosintha, muziyese kwa kanthawi kuti muone ngati zikhale bwino.

6. Zindikiritsa anthu kuti kusintha pamodzi ndi imfa ndi zinthu ziwiri zokomana nazo mu moyo wa munthu.

KULEMBA MAYANKHO KUKHUDZANA NDI FUNDO ZOTHANDIZIRA ANTHU

Ambuye, ndionetsereni ngati ndakhala womasuka komanso woona mtima pokomana ndi kulimbana kwa mkati mwanga pokana kusintha.

Ambuye, kodi ine mungandithandize bwanji kuti ndikope anthu ena kuti akhale nane mu zokambilana kukhudzana chitukuko? Kodi ndakhala ndikumvetsera kufundo za anzanga?

Ambuye, kodi pali masitepe ena okhazikitsa masomphenya awa amene mukufuna kuti ndingagawane ndi anthu?

Ambuye, Kodi ngakhalepo ngati Danieli, mu njira yoti ndapereka kusintha mmalo mwa kupereka chabe malamulo oti iwo achite? (Danieli 1, 2)

KUPANGA GULU LA ANTHU LOPAMBANA

1. Uzisonkhanitsire wekha anthu amene ali achikhulupiriro komanso okhala ndi masomphenya amene ali ndi maziko enieni



pa mawu a Mulungu

2. Usonkhanitse anthu amene angapezeke pa nthawiyo.

3. Uonetsetse kuti anthu amene wawasonkhanitsa ali ndi ufulu wogwiritsantchito mphatso zawo.

4, Upereke kwa anthuwo fundo zokhwima komanso za tanthauzo ku moyo wao.

5. Upereke ufulu kwa anthu woti akhoza kutsutsa

6. Ukhale nawo mu matamando komanso kuwazindikira ziwalo za gululo.

ZOYENERA KULEMBA KUKHUDZANA NDI KUPANGA GULU LA ANTHUWO

Ambuye, Kodi anthu a chikhulupiriro ndi ati, anthu a masomphenya ndi ati amene azika mizu pa mawu amene akhoza kugwira ntchito pamodzi ndi ine?

Ambuye, Kodi pali anthu enanso ali ndi zowayenereza zabwino mu madera awa amene ali pamaso panga amene mukufuna kuti ndiwasonkhanitse pamodzi kuti agwire ntchito ndi ine?

Ambuye, Kodi ndikutha kuwamasula kuti agwiritse ntchito mphamvu zao zomwe mwaika mwa iwo?

Ambuye, Ndionetsereni umo ndingaperekere ku ziwalo za gulu ili fundo zokhwima koma za tanthauzo?

Ambuye, Kodi ndikuwapatsa anthu ufulu wotsutsana nane?

Ambuye, Kodi ndikuchita bwino popereka matamando pamodzi ndi

Tiyenera kukhala osamalitsa kwambiri kumvetsera kwa Mulungu mu nthawi ya kufungatira kwathu kuti tisalakwe pochita mosayenera.

ZOYENERA KUCHITA MU ZOLEMBA ZAKO

Ambuye, kodi pali kena kalikonse kamene mukufuna kulankhula kwa ine kukhudzana ndi kulankhula za masomphenya amene mwaika mu mtima wanga? Lemba pansi apa zimene akulankhula.

KULANKHULA KUMATHANDIZA KUTI ANTHU AKHALE MU MAGANIZO A MULUNGU

Chifukwa china cholankhulira ndi pakamwa pako (kuvomereza mawu (rhema) pamodzi ndi masomphenya a Mulungu ndi kulimbikitsa chikhulupiriro mwa ena ndi kuwapanga iwo kuti akhale ndi iwe pokhazikitsa zolinga za Mulungu. Pamene tikuphunzira kugawana ndi anthu masomphenya mwa chikhulupiriro, anthu amayamba nawo kudzodzedwa komanso kutenga mbali mu chili chonse. Mulungu angawatsogolere.

Koma sichinthu chophweka kugawana ndi anthu masomphenya mu chikhulupiriro ndi kuwatengera anthu mu icho. izi ndi zina mwa zovuta zomwe ungakomane nazo, komanso njira zomwe ungakomane nazo, komanso njira zina zokuthandiza kukutsogolera kuti ukachite mwanzeru ndi mopindula.

ZOVUTA ZINA ZA UMUNTHU

1. Anthu ambiri amakana kuti asinthe. Usayesere kumusintha munthu aliyense pa zachuma chake, chinthunzi chake, zikhulupiriro zake mu njira yosayenera.

2. Pakhoza kukhala mayesero ambiri pa kusinthapo. Khala wamphamvu!



3. Matsutsano akhoza kufika. Uyenera kuti uwapime ndipo uyankhe okhawo amene ali matsutsano omangirira ndi a phindu.

4. Anthu ena akhoza kuyankha ndi ukali komanso mkwiyo. Iwe usagwedezeke koma pita patsogolo ndi mawu (rhema) pamodzi ndi masomphenya a Mulungu)

KUSANKHULA ZOLEMBA ZAKO

Tsopano usanthule zolemba zako zomwe udalemba kale. Kodi Ambuye adapempha kuti uvomereze ndi pakamwa pako masomphenya ena alionse omwe Iye adaika mkati mwa mtima wako? Ngati zili choncho, lembera izi:-

Ambuye, ndionetsereni mu njira yina iliyonse imene ndatsutsana ndi mbali ya za chuma yao, kapena chinthunzi chao, kapena zikhulupiriro zawo za uzimu? Ngati zili choncho kodi izi zingakonzedwe bwanji?

Ambuye, kodi ndili wofooka, ndili woukira? Ngati ndili wotero, kodi njira yokonzekera ingakhale yotani?

Ambuye, ndilankhuleni kukhudzana zomwe zokhoza kukhala mkati mwa matsutsano. Kodi inu mukufuna kuti ndinene kwa iwo zotani? Kodi mukufuna kuti ndiyankhe motani?

KUKONZA NJIRA ZOTHANDIZIRA ANTHU

1. Kulenga mmaganizo mwa anthu kufunikira kosintha pochita izi;
(a) kuwazindikiritsa anthu mavuto amene alipo pa nthawi ino.
(b) kuchenjeza anthu zotsatira zokana kusintha
(c) kuwatsimikizira zotsatira zake zabwino akasintha

2. Kukomana nawo anthu okana awa moona mtima pamodzi ndi momasuka

AHEBERI CHAPUTALA 4 CHAPEREKEDWA CHITSANZO PAMODZI NDI KULEMBEDWA MWA CHIDULE

Ine ndalengedwa kukhala mu mpumulo wosatha polumikiza chikhulupiriro changa ku mawu a moyo a Mulungu. Ndiyenera kuwalankhula ndipakamwa panga - nditawasunga mu mitima mwanga kumupempha Mulungu kuti andipatse chikhulupiriro kuti ndikakhulupirire pamene ndayamba kukaikira ndi kukumbukira kuti Yesu naye adayesedwa ndi chikaikiro ndipo ndikumvetsa bwino kuti andichotsera kukaikira kwanga pamene ndikuitana pa Iye.

CHIKHULUPIRIRO PAMODZI NDI CHIPIRIRO ZIMALANDIRITSA MALONJEZANO

Pamene tikulankhula ndi pakamwa pathu malonjezano, Mulungu akufuna ife kudikira mwa chipiriro pa Iye kuti akwanilitse izo. Chonde lemba Aheberi 6:11-15 mwa pemphero. Cholinga cholembera chaputala ichi ndi choti cholembera chathu ndi diso lako lenileni. Pamene tikulembera chaputala mwa pemphero komanso molingalira mozama, Mulungu amavumbulutsa zinthu kwa ife kuchokera ku zolembedwazo zomwe sitidazionepo. Mwa ichi ndimaona kuti kulemba malembo opatulika ndinjira imodzi mwa zina yofunikira kumoyo wanga wa uzimu. Pansi apa pali malo osalembedwa kuti ulembe mavesi awa.

Kodi zopherezera zako zili zotani pa mavesi awa?
KULIMBIKITSIDWA KUGWIRITSA NTCHITO CHIVOMEREZO CHATHU

....."Ngati tigwiritsa kulimbika mtima ndi kudzitamandira kwa chiyembekezocho....."(Aheberi 3:6, 3:6, 4:14)
....."Tigwiritse chivomerezo chosagwedera chiyembekezo chathu pakuti wolonjezayo ali wokhulupirika....." (Aheberi 10:23).



Mulungu sadataya nthawi yake kumatiuza ife kuti tigwiritsebe chivomerezo chathu kukadakhala kuti sichili vuto kwa ife. Tidzakhala tikuyesedwa kusiya chivomenezo chathu poleka kulankhula mawu (rhema) pamodzi ndi masomphenya a Mulungu pamene tikudikira lonjezano lake la Mulungu kuti likwanilitsidwe mu nthawi yakudikira. Ichi, pamafunika chipiriro chapadera ndipo chipiriro ichi chimaumba umulungu mwa ife. Iye amaswa zofuna zathu, kuyeretsa mitima yathu ndi zina zotere mu nthawi yakudikira kotere. Pamene tikupita kwa Iye mu chiyanjano, Iye adzatiuza zimene Iye akuchita ndi zimene tiyenera kuchita - komanso izi zidzatithandiza kuimabe mu chipiriro pamodzi ndi mu chikhulupiriro.

UBWINO WOZINDIKIRA NTHAWI

Dziwani kuti kudali patadutsa zaka makumi awiri ndi mphambu zinayi Mulungu atapereka kale lonjezano kwa Abraham, pamene Iye adamuuza Abraham kuti azilankhula ichi kwa anthu poyera. Ndikukhulupirirra kuti ichi ndi cinthu chovuta kuchichita. Sitimangoyamba kulankhula zimene Mulungu watilankhula mu nthawi yathu komanso mu njira yathu yathu. Mulungu ali ndi nthawi yake Yangwiro komanso njira yake yokwanilitsira zinthu. Tisamachite zinthu mwa ife tokha. Timalankhula pamene Iye watiuza kuti tilankhule komanso mu njira imene Iye akufunira.

Pamene Mulungu waika mbeu ya uzimu mwa ife mwa mawu (rhema) kapena mwa masophenya, apa yangokhala mbewu chabe. Iyenera kukhala ndi mizu, ikule, ikhale, mtengo waukuru ndi wamphamvu wopereka moyo kwa iwo okhudza. Ngati tilankhula nthawi isadakwane, ndipo anthu ena anyoza zimene Mulungu watiuza Iye adzakwanilitsa kupyolera mwa ife, - mtengo ukhoza kuthyoka usadamere komanso usadakule. Mwa ichi Mulungu amafuna kuti tizidikira tisadayambe kulankhula mawu (rhema) ake pamodzi ndi masomphenya ake. Iye amafuna kuti mbeuyo imere mwa ife ndi cholinga kuti tikhoza kuima ndi anthu otsutsa koma ife osagwedezeka konse. Iye amafuna ife kudikira pokhazikitsa muyeso wake weniweni kuti mphamvu yake ikayende. Kenako, Iye amalola kuti tikhoze tsopano kulankhula ndi pakamwa pathu kwa anthu.

ndikupereka zosowa zanga kwa iye, Iye amalankhula kwa ine kukhudzana ndi izo. Iye amandiuza cholinga chake pa izo.

Pemphero langa pamodzi ndi pembedzero langa zamizidwa mu chiyamiko changa chifukwa choti Mulungu wavumbulutsa zolinga zake kukhudzana ndi zinthunzo. Umo ndimo pemphero langa limasanduka chiyamiko. Ndimayamba tsopano kulankhula kwa ine. Kuvomereza ndi pakamwa kukutanthauza "kulankhula chinthu chimodzi modzi chomwecho." Mwa ichi ndi mayamba kulankhula zinthu zomwe Mulungu walankhula kwa ine mu pemphero. (Buku la chiyanjano ndi Mulungu lolembedwa ndi mkozi yemwe yilikuthandiza umo ungapempherere mu njira yotere).

## KUKHAZIKIKA MU CHIKHULUPIRIRO MU NTHAWI YA PAKATI PA KULANKHULA NDI KULANDIRA

Pamakhala kanthawi ka kudikira pakati pa nthawi ya kulankhula kwa Mulungu ndi nthawi ya kukwanilitsidwa kwa izo walankhula. Abraham adali kulankhula za dzina lake pamodzi ndi kulankhula izo Mulungu adamuuza zisadakwanilitsidwe. Pa Mariko 11:23 akulonjeza kuti "koma adzakhulupirira zisadakwanilitsidwe. Pa Mariko 11:23 akulonjeza kuti "koma adzakhulupirira kuti chimene chichitidwa, adzakhala nacho."

Pa Aheberi 3 ndi 4 tili ndi chiphunzitso chabwino mu baibulo zakulumikizana kwa chikhulupiriro ndi mawu (rhema) mu nthawi yakudikira dipo uko ndiko kukhazikika mu chikhulupiriro pamene ukudikira makwanilitsidwe a malonjezano a Mulungu kwa iwe. Tiyeni tilingalire ichi. Chonde werengani Aheberi 3 ndi 4 mwa pemphero ndipo ulembe zonse zimene wapeza kukhudzana ndi kulumikizana pakati pa chikhulupiriro ndi mawu (rhema).



## CHIPHUNZITSO CHA PA AHEBERI 3




FUNDO IJAMBULIDWA (3:18-19)
- Mawu kuphatikiza ndi chikhulupiro = Mpumulo
- Mawu opanda chikhulupiriro = Mpumulo palibe

Ndikukhulupirira kuti kulowa mu mpumulo wa Mulungu munthu ayenera kuphatikiza mawu olankhulidwa a Mulungu pamodzi ndi chikhulupirirrocho mu mtima chopereka kwa munthu ndi Mulungu. Mawu a Mulungu kuphatikiza ndi chikhulupiriro cha Mulungu zimapanga mpumulo wa Mulungu. Izi zimatipangitsa ife kukhala anthu opatulika mu dziko lino lapansi lodzala ndi anthu omwe alibe zinthu izi mu miyoyo yao. Timakhala anthu omwe anthu amaikapo chikhulupiriro mu nthawi ya mavuto awo.

Lingalirani ichi:

## KUKHAZIKITSA ZOLANKHULA ZAKO KUPYOLERA MU CHIFUNIRO CHA MZIMU WAKO

Ndidali wodabwa kuona kuti mzimu wanga udali ndi "chifuniro." Ndimadziwa za maganizo, zifuniro pamodzi ndi zochitachita zili mbali imodzi ya moyo koma sindidazindikire kuti zidalinso mbali imodzi ya mzimu. Taona mavesi otsatirawa umo akuti phunzitsira kuti tikhoza kuchita zisankho zomwe zili ntchito ya chifuniro mkati mwa mitima yathu kapena mizimu yathu.

....."Ndipo taonani ndipita ku Yerusalemu womangidwa mu mzimu
....."(Machitidwe 20:22)....."Yense achite monga anatsimikizira mtima....." (II Akorinto 9:7)

....."Paulo anatsimikiza mu mzimu wake kunka ku Yerusalemu" (Machitidwe 19:21)

Pamene tatsimikiza mu mizimu yathu, limakhala lingaliro lozama komanso logwirika. Silisinthika wamba. Pamene "talingalira ndikutsimikiza" mu moyo wathu limakhala lofewerako kotero kuti ukhoza kusintha nthawi ili yonse. Kumbukirani: timalankhula zinthu zimene zili mu mtima mwathu (Mateyu 12:34). Choncho pamene tikufungatira mu mizimu yathu kuti tidzitsatire zotsatira zake kudzakhala kuzikankhula kuti zionekere komanso tidzalankhula ndi mtima wonse. Timalankhula zimene talingalira pamodzi ndi kukhazikitsa mu mitima yathu. Chinthu chimmodzi mwa zonse zopemphedwa kwa anthu ku chipangano chatsopano ndikulankhula mawu okha a chisomo pamodzi ndi omangirira osati oipa (Aefeso 4:29). Ngati talingalira pamodzi ndi kutsimikiza mu mizimu yathu kuchita ichi, tidzaona moyo watsopano mkati mwa ife pamene tikulola mitima yathu kufungatira ndi pakamwa pathu kulankhula zokhazo zomangirira osati mawu oononga a satana.



## KUKHAZIKITSA CHIFUNIRO CHA MZIMU WAKO KU KULANKHULA MASOMPHENYA PAMODZI NDI MAWU A MULUNGU (RHEMA)

Mulungu atatha kumpatsa Abrahamu mawu (rhema) pamodzi ndi masomphenya ndipo Abrahamu adadzadzitsa mtima wake ndi izo. Mulungu tsopano adamuitana kukhazikitsa chifuniro chake ndikuyamba kuchilankhula Adamusintha dzina kuchokera ku Abram kukhala Abraham kutanthauza "tate wa mafumu ambiri). Mwa ichi nthawi iliyonse Abraham amatchulidwa dzina lake, adali kulankhula mwa chikhulupiriro malonje zano a Mulungu. Lemba zomwe zili pa Genesis 17:5....."
Tsopano m'lembenso mosamala ndi mwapemphero Mariko 11:22-24

Mwapemphero, usanthule zimene walemba kale ndipo tsopano ulembe zomwe waphunzira kuchokera pa izo walemba. Chikhulupiriro cha mtima chimakhudzana ndi kulankhula kwanga kwa mawu (rhema) pamodzi ndi masompenya a Mulungu zomwe ndafungatira mkati mwa mtima wanga pozindikira kuti pofika mu makwanilidwe a nthawi, Mulungu adzadzikwanilitsa yekha.
Pa Yoswa 6, tikuona ana a Israeli akuthokoza Mulungu khoma la Yeriko lisadagwe. Pa Yohane 11:41-43, adathokoza Lazaro asadauke mmanda.

Pa Afilipo 4:6-8 tikuuzidwa kuti mu mapemphero athu tidziphatikizanso mayamiko. Pakuchita izi pemphero lathu timapanga likhale lenileni lamphamvu. Ndiloleni ndichite chitsanzo chotere; Ngati ndipita kwa Mulungu ndi zosowa zanga ndipo mu pemphero pamodzi ndi pembedzero ndi ziika pa mapazi a Yesu Khristu kenako nkunyamuka, Kodi apa ndiye kuti ndapemphera? Sindikukhukupirira choncho! chifukwa choti ndipemphero pemphero liyenera kukhala chiyanjano ndi Mulungu mmene ine ndizilankhula kwa Mulungu ndipo lye azilankhula ndi ine kupyolera mu chiyanjano cha uzimu pamene

Chaputala 8

## KUDZADZA SENSI YACHINAYI YA MZIMU WA MUNTHU POLANKHULA MAWU (RHEMA) NDI MASOMPHENYA

### KULANKHULA KUCHOKERA MU MTIMA

....."Akubabwa inu anjoka mungathe bwanji kulankhula zabwino, inu akukhala oipa? Pakuti mkamwa mungolankhula mwa kusefukwa kwake kwa mtima. Munthu wabwino aturutsa zabwino mchuma chake chabwino ndi munthu woipa aturutsa zoipa m'chuma chake choipa....." (Mateyu 12:34-35)

Timalankhula zimene zili mkati mwa mitima yathu. Ngati mkati mwa mitima takhala tikufungatira zoipa, timalankhulanso zoipa. Ngati tafungatira matsutsano, timadzalankhula za matsutsano. Ngati tafungatira kulankhula kwa Mulungu (mawu) pamodzi ndi masomphenya a Mulungu wamphamvu yonse timayamba kulankhula mawu pamodzi ndi masomphenya a Mulungu. Ichi ndi chifukwa chache kulankhula kuli chinthu chofunikira ku kulenga. Pamene Mulungu amalenga zakumwamba Mulungu, "anaitana zinthu zoti kulibe monga ngati ziripo....." (Aroma 4:17). Tiyenera kufunitsitsa kulankhula pamene Mulungu watilangiza ife kutero .

| | SENSI | KAGWIRITSIDWE NTCHITO UMO IMFA | CHITSANZO CHA M'BAIBOLO | SITEJI |
|---|---|---|---|---|
| 1. | MAKUTU AMKATI KHUTU LA MKATI | KULANDIRA MAWU A MULUNGU | GENESIS 12:1-3 | KATENGA PAKATI |
| 2. | MASO A MKATI 2 CHIVU LUTSO 4:1 | KULANDIRA MASO MPHENYA A MULUNGU | GENESIS 15:5-6 | |
| 3. | MALINGALIRO AMKATI LUKA 2:19 | KULINGALI MAGANIZO A MULUNGU | AROMA 4:20-21 | KUFUNGATIRA |
| | CHIFUNIRO CHA MKATI MACHITIDWE 19:21 | KULANKHULA MAWU AMULUGU | GENESIS 17:5 | |
| ZOTSATIRA ZAKE | | KUFA KWA MASOPHENYA | GENESIS 16:2<br>GENESIS 17:18-19 | KUBADWA |
| | | KUUKA KWA MASO MPHENYA | GENESIS 21:1-2<br>AGALATIYA 4:4 | |



Komanso mu njira yomwe watilangizira. Ngati sitingatero, apa timaletsa mphamvu ya kulenga kuti ikhale ya mphamvu. Mphamvu imene yakhala ikukula mkati mwa mizimu yathu imasowa kumasuludwa. Mawu athuolankhulidwa amapereka njira yotere yomasula. Pamene mphamvu kuchokera ku mizimu yathu yamasulidwa, imapanga chimene mumafuna ndi mawu a pakamwa panu. Mwa chitsanzo, monga Yesu amalamulira thupi la munthu kuti lichiritsidwe, apa adali kumasula mphamvu ya mzimu woyera mkati mwake kuti ichite zimenezo ndipo zimachitika.

### UMBONI WANGA

Kalelo, kulankhula ndi pakamwa panga sichidali chophweka kwa ine. Pa zaka zambiri sindidali wotsimmikizika ndi kulankhula kwa mphamvu kwa Mulungu mkati mwa ine ndipo kudali kovuta kuti ndidzuke ndi kulankhula mwa chikhulupiriro kuitana pa dzina la Mulungu. Koma pamene ndidapitirira kulemba pamodzi ndi kukhala wokhulupirira kulankhula kwa Mulungu, izi zapangitsa kuti ndikhale ndi chikhulupiriro pa kulankhula zolinga za Mulungu zisadayambe kuchitika.

Chitsanzo chimodzi cha izi chidachitika tsiku la Mulungu mmawa pamene ndidali kudikira pa Ambuye pa chitsogozo chake. Pa tsiku ili pokonza uthenga. Iye adalankhula kupyolera mu kulemba kuti Iye akachilitsa mkulu wa mpingo wanga usikuwo. Iye adali kudwala msana umene udavulala mu nthawi ya ulimi wake. Izi ndidagawana naye nthawi ya mmawa ndipo adalandira uthengawo. Mu mapemphero a nthawi ya kumadzulo nditatha kulalikira kwa anthu onse, ndidaitana mkulu wa mpingo wina kubwera kutsogolo ndipo tonse tidaika manja pa iye. Pamene tidali kupemphera adachilitsidwa nthawi yomweyo ndipo kupweteka konse kudatheretu ndipo tsopano adakhala wamphamvu ndiwanthanzi pa moyo wake wa thupi.

Nthawi yochepa yakudikira iyi idatengera kuti ine ndilankhule ndi pakamwa panga mwa chikhulupirire zolinga za Mulungu zisadayambe kuonekera. Kenako Mulungu adamasula mphamvu yake.

Chaputala 8

## KUDZADZA SENSI YACHINAYI YA MZIMU WA MUNTHU POLANKHULA MAWU (RHEMA) NDI MASOMPHENYA

### KULANKHULA KUCHOKERA MU MTIMA

....."Akubabwa inu anjoka mungathe bwanji kulankhula zabwino, inu akukhala oipa? Pakuti mkamwa mungolankhula mwa kusefukwa kwake kwa mtima. Munthu wabwino aturutsa zabwino mchuma chake chabwino ndi munthu woipa aturutsa zoipa m'chuma chake choipa....." (Mateyu 12:34-35)

### CHITSANZO CHANGA

Akhristu ambiri lero lino ali ndi maganizo chabe a tsiku la chionongeko cha la Amerika. Alibe choti akambe kukhudzana ndi dziko labwino ndi lalikuru la Amerika limene lili lathu. Pali chikhulupiriro, masomphenya chiyembekenzo kapena pemphero lwa Mulungu kuti achite zodabwitsa pakati pathu. lwo amvetsera nkhani zolembedwa mu manyuzi ndipo keneko masunga zinthu zoipa zokhudzana ndi dziko la Ameriza mu mitima yao. Ambiri akhala akulankhula motere...."Tilionera dziko la Amerika likapasuka...."

Umo sindimo Yesu amachitira pamene adali kuyenda mu Galileya. Ngakhale kuti chopia chidali ponseponse muufumu wonse wa Romammene lye amakhala, lye amakonda kukhala payekha kupemphera zonse zochitika komansi lye kukhala chitsanzo kumadera amene lye amakhala.

Ifenso sitiyenera kumangolingalira zoipa mu mitia yathu. Tiyenera kukhala ndi Atate wathu wakumwamba kuti mawu ake akhalee mwa ife ndi kukhala chitsanzo chabwino.



Pa zaka zitatu zadutsanzo ndakhala ndikupemphera paodai ndi kusala kudya kamodzi mwezi uli wonse kupemphera dziko lathu. Ndachita izi pamodzi ndi amnanga zikwizikwi owe ali mu utumiki wopembedzera dziko la Amerika.

Takhala tikupempha kuti Ambuye akhululukire zolakwa za dziko lathu, kupempha Mulungu kuti abwezeretse utsogoleri wa uzimu woyenerera kuti mchitidwe wochotsa pakati pa azimayi uthe, komanso kuti mphamvu ya mzimu woyera iyende mu dziko lathu. Mulungu wandipatsa (rhema) uthenga pamodzi ndi masomphenya kukhudzana ndi zinthu zoterezi pamene ndakhala ndkupemphera pamodzi ndi kusala chakudya. Ndakhala ndikudzisunga zoterozo mu mtima mwanga ndipo kenako ndakhala ndikuona Mulungu akuyankha mapemphero athu komanso kundipanga ine kukhala chitsanzo pakati apa anthu amene amakhala pafupi ndi ine. Tsono tiyenera kukhala tonse moyo woteri. Tiyenera kukhala padera ndi Atate wathu amene ali wopereka moyo ndi kusunga mawu ake mu mtia mwathu kotere kuti mawu onse aturuka mkamwa azikhala mkamwa mwathu ndi amoyo kwa onse akumvera - osati mawu a imfa.

Tilole kuti kena kalikonse, kamatsutsano, kosakhulupirika kamezedwe ndi zinthu za bwino zotonthoza, zolangiza pamodzi ndi zopereka moyo. Tisafungatire naganizo a satana mu mitima yathu koma tifungatire mzimu woyera mkati mwa mitima yathu.

### ZOYENERA KUTI ULEMBE

....."Ambuye, kodi pali mbali yina yake mu moyo wanga mmene muli zosayenera zosagwirizana ndi mawu amene mukufuna kuti mulankhule nane? Ngati zili concho, chonde ndivumbulutsireni ichi ine ndipo mumdionetsere umonso munga chilitsire umonso munga chilitsire ichi....."ulembe yankho lake pansi apa.

PEMPHERO - Mulungu, yeretsani mitima yathu ndi maloto pamodzi ndi masomphenya.

CHITSANZO CHANGA

Akhristu ambiri lero lino ali ndi maganizo chabe a tsiku la chionongeko cha la Amerika. Alibe choti akambe kukhudzana ndi dziko labwino ndi lalikuru la Amerika limene lili lathu. Palibe chikhulupiriro, masomphenya a chiyembekenzo kapena pemphero kwa Mulungu kuti achite zodabwitsa pakati pathu. Iwo amvetsera nkhani zolembedwa mu manyuzi ndipo kenako ku masunga zinthu zoipa zokhudzana ndi dziko la Ameriza mu mitima yao. Ambiri akhala akulankhula motere...."Tilionera dziko la Amerika likapasuka...."

Umo sindimo Yesu amachitira pamene adali kuyenda mu Galileya. Ngakhale kuti choipa chidali ponseponse muufumu wonse wa Romammene Iye amakhala, Iye amakonda kukhala payekha kupemphera zonse zochitika komanso Iye kukhala chitsanzo kumadera amene Iye amakhala.

Ifenso sitiyenera kumangolingalira zoipa mu mitima yathu. Tiyenera kukhala ndi Atate wathu wakumwamba kuti mawu ake akhale mwa ife ndi kukhala chitsanzo chabwino.

Pa zaka zitatu zadutsanzo ndakhala ndikupemphera paodai ndi kusala kudya kamodzi mwezi uli wonse kupemphera dziko lathu. Ndachita izi pamodzi ndi amnanga zikwizkwi owe ali mu utumiki wopembedzera dziko la Amerika.

Takhala tikupempha kuti Ambuye akhululukire zolakwa za dziko lathu, kupempha Mulungu kuti abwezeretse utsogoleri wa uzimu woyenerera kuti mchitidwe wochotsa pakati pa azimayi uthe, komanso kuti mphamvu ya mzimu woyera iyende mu dziko lathu. Mulungu wandipatsa (rhema) uthenga pamodzi ndi masomphenya kukhudzana ndi zinthu zoterezi pamene ndakhala ndkupemphera pamodzi ndi kusala chakudya. Ndakhala ndikudzisunga zoterozo mu mtima mwanga ndipo kenako ndakhala ndikuona Mulungu akuyankha mapemphero athu komanso kundipanga ine kukhala wotere.



Chitsanzo pakati pa anthu amene amakhala pafupi ndi ine. Tsono tiyenera kukhala tonse moyo wotere. Tiyenera kukhala padera ndi Atate wathu amene ali wopereka moyo ndi kusunga mawu ake mu mtima mwathu kotere kuti mawu onse aturuka mkamwa azikhala amoyo kwa onse akumvera - osati mawu a imfa.

Tilole kuti kena kalikonse, kamatsutsano, kosakhulupirika kamezedwe ndi zinthu za bwino zotonthoza, zolangiza pamodzi ndi zopereka moyo. Tisafungatire naganizo a satana mu mitima yathu koma tifungatire mzimu woyera mkati mwa mitima yathu.

ZOYENERA KUTI ULEMBE

....."Ambuye, kodi pali mbali yina yake mu moyo wanga mmene muli zosayenera zosagwirizana ndi mawu amene mukufuna kuti mulankhule nane? Ngati zili concho, chonde ndivumbulutsireni ichi ine ndipo mumdionetsere umonso munga chilitsire umonso munga chilitsire ichi....."ulembe yankho lake pansi apa.

PEMPHERO - Mulungu, yeretsani mitima yathu ndi maloto pamodzi ndi masomphenya.

Chitsanzo china chomaliza chikutionetsa umo njira yofungatira imagwirira ntchito mwa njira yinanso. Werengani chitsanzo cha Eliya pa 1 mafumu 18 mpaka 19.

Eliya atatha kugonjetsa aneneri 450 a Baala mu njira ya mphamvu yodabwitsa, kenako mantha adamugwira ndipo adayamba kuopa atamva mawu a Yezebeli. Yezebeli adamuopsyeza kuti amupha Eliya (19:1-3). Mmalo moti akhale pansi kulingalira kuti apeze zolinga za Mulungu, iye adalola mawu a chionongeko kulowa mu mtima mwake ndi kukhazikika ndipo zotsatira zake adathawa chifukwa cha mantha mmalo moti aime ndi mphamvu ya Mulungu yoperekedwa kwa iye. Pa kuchita zoterezi adafungatira choipa mumtima mwake mmalo mwa chilungamo, mantha mmalo mwa chikhulupiriro. Zidamutengera Mulungu masiku ambiri kubwezeretsanso mtima wake pomwe udalili poyamba wokhutitsidwa ndi wopatsidwa mphamvu ndi mawu a Mulungu (rhema). Mulungu adamutumikira iye kupyolera mwa angelo. Eliya adasala chakudya pa masiku makumi anayi ku phiri (19:8) asadalandire mawu (rhema) a Mulungu uperekanso mphamvu ku mtima wake. Pamene adalowa mu chiyanjano ndi Mulungu adalankhula mawu (rhema) mu mtima mwake kubwezeretsanso mziu wake komanso kumutumanso kuti akagwire ntchito ya Ambuye (1 mafumu 19:13-18).

Chitsanzo chabwino bwanji ku moyo wathu! ndikudziwa umo izi zikuchitikira kwa ine. Ndakhala ndikufungatira choipa mmalo mwa kuumangirira mu chikhulupiriro. Kenako tsopano ndimayamba ulendo wautali wobwerera kwa Mulungu mwa chikhulupiriro ndi kukonzedwanso kwa mtima wanga pogwiritsa ntchito mawu (rhema) a khristu.

Kumvetsa bwino kwanga pa zinthu izi kumandithandiza kukhala mu chikondi cha khristu komanso kubwerera kumene ndidagwerapo. Ndipemphera kuti izi zichitike ndi moyo wako. Kuti tifike pa chikhulupiriro cha mtima, tiyenera kusandulika kuchokera ku ufumu wa mdima kulowa mu ufumu wa kuunika.



Tiyenera kuzindikira pamodzi ndi kuononga ntchito za satana pamene tikuzindikira ntchito za mzimu woyera.




ABRAHAM - TATE WA CHIKHULUPIRIRO
1. ADAMVA KULANKHULA KWA ABUYE
2. ADAONA NDI MASO A CHIKHULUPIRIRO
3. ADAGANIZA NDI MTIMA WA CHIKHULUPIRIRO
4. ADALANKHULA MAWU A CHIKHULUPIRIRO
5. ADACHITA MWA CHIKHULUPIRIRO
6. ADALANDIRA MALONJEZANO A CHIKHULUPIRIRO

Zinthu zitatu izi kuonetsera kuti zili zionetsero za mzimu, kudzisiyanitsa ndi za moyo komanso kuonetsera umo tingagwiritsire ntchito chilichonse pachokha pakufungatira maloto pamodzi ndi masomphenya komanso mawu (rhema). Komanso tidzakhala tikuona Abrahamu, monga "Tate wa chikhulupiriro "adalola maloto pamodzi ndi mawu (rhema) a Mulungu kudzadza zinthu zonse zitatu izi (maganizo, zofuna pamodzi ndi zochitachita kuti iye AKULE MU CHIKHULUPIRIRO (Aroma 4:20).

KUZINDIKIRA ZOLINGARIRA ZA MZIMU

Ndidali wodabwa pamene ndidazindikira kuti mtima wanga kapena kuti zimu wanga uli ndi zolingarira. Ndimazindikira kuti moyo wanga udali ndi zolingalira koma sindidali kuzindikira kuti mzimu wanga udalinso ndi mphamvu yoganiza mozama. Tiyeni tisanthuleni mubaibulo machaputala amene akufotokoza za izi:

....."Mariya amasunga mawu awa onse nawalingalira mu mtima mwake.....' (Luka 2:19)

....."Koma amakhalpo ena alembi akuganizira mumtima mwao....." (Mariko 2:6)

Mavesi awa akuonetseratu kuti tili ndi mphamvu ya kulingalira ndi kusanthula mu mitima yathu komanso mizimu yathu. Lamulo lotitsogolera kusiyanitsa pakati pa mzimu wa munthu ndi moyo wa munthu ndi ili: chimene chimaturuka kuchokera mu miyoyo chili chakunja, chosinthika nthawi iliyonse koma chimene chimachokera ku mzimu chili chinthu chapadera chozama. (kulingalira kusiyana ndi kusanthula).

KUDZADZA ZOLINGALIRA ZA MZIMU

Mulungu akufuna ife kufungatira maloto, masomphenya, pamodzi ndi mawu ake mu mitima yathu. Iye akufuna malingaliro a mkati mwathu kuti adzadziwe ndi vumbulutso lake basi. Ngati tikhala mwa Iye ndipo mawu (rhema) ake akhala mwa ife, tikhoza



kupempha chilichonse tikufuna (Yohane 15:7)

Mulungu akufuna ife kuti tizikhala nthawi zonse mwa Iye ndipo mawu ake olankhulidwa azikhala mwa ife kuti zokhumba za moyo wathu zizikwanilitsidwa.

Abrahamu adalimbika mu chikhulupiriro pololа malingaliro a mtima mwake kuzama pa Mulungu pamodzi ndi malonjezano ake kwa iye. (Ulembe Aroma 4:17-24 ndipo uwerenge mofatsa ndi modekha komanso mwa pemphero).

Tsono mwa pemphero, onaninso zimene walemba ndipo tsopano lembera zimene Mulungu akupereka kwa iwe. Abrahamu sadafooke mu chikhulupiriro (vesi 19). Iye adali kuzindikira za choonadi chake chenicheni cha thupi zomwe akomane nazo kuti alandire malonjezano a Mulungu. Iye sadalole kuti kufooka kwake kw thupi kuzamitse chikhulupiriro chake. Mmalo mwake,iye adapenyerera mphamvu ya Mulungu pamodzi ndi lonjezano la Mulungu ndipo ndi maganizo ake adafungatira chikhulupiriro osakhala ndi chikaiko chilichonse. iye adatsimikiza mtima kuti zimene Mulungu adalonjeza, adali nayo mphamvu ya kukwanilitsa. Izi sikuti zidangolembedwa kwa Abrahamu yekha komanso kwa ife kuti tichitepo kanthu.

Tiyeni tione chitsanzo china cha mu baibulo cha Mariya pa Luka 2:8-20 chonde muwerenge panopa.

Pa vesi ya 10-14 angelo akulankhula uthenga wapadera (rhema) kwa abusa. Pa vesi 17 abusa adamuuza Mariya ndi Yosefe "mawu" (rhema) okamba za mwanayo. Pa vesi 19....."Mariya adasunga mawu (rhema) nawalingalira mu mtima mwake.....". Apa tikuona Mariya akufungatira mawu (rhema) a Mulungu mu mtima mwake - mozama kawiri ndi kawiri. Ichi ndi chitsanzo chabwino ndi chagwiro cha umotizifungatira mawu a chikhulupiriro mu tima wa chikhulupiriro.

SITEJI YACHIWIRI - KUFUNGATIRA

chithunzi



Chaputala 7

# KUDZADZA SENSI YACHITATU YA MZIMU WA MUNTHU POLINGALIRA KULANKHULA KWA MULUNGU PAMODZI NDI MASOMPHENYA

## Mawu oyambirira - kufungatira

Pmene munthu walandira zolinga za Mulungu mu mtima mwake kupyolera mu mawu (rhema) pamodzi ndi masomphenya, ayenera kuyamba kufungatira zimene iye waziona pamodzi ndi kumva - kuzilola kuti zidzadze chigawo chilichonse cha mtima wake. Mitima yathu ili ndi maganizo, zofna pamodzi ndi zochitachita zimene ziyenera kudyeretseredwa pamodzi ndi kuzamitsidwa ndi maloto pamodzi ndi masomphenya a Mulungu. Mulungu watilenga ife kuti mizimu yathu (mitima) pamodzi ndi miyoyo yathu, zikhale ndi malingaliro, zofuna pamodzi ndi zochitachita pamodzi ndizauzimu zili zozama ndipo zili zamphamvu yapadera kuposa maganizo, zofuna, pamodzi ndi zochitachita za moyo.

| | SENSI | KAGWIRITSIDWE NTCHITO UMO IMFA | CHITSANZO CHA M'BAIBOLO | SITEJI |
|---|---|---|---|---|
| 1. | MAKUTU AMKATI KHUTU LA MKATI | KULANDIRA MAWU A MULUNGU | GENESIS 12:1-3 | KATENGA PAKATI |
| 2. | MASO A MKATI 2 CHIVU LUTSO 4:1 | KULANDIRA MASO MPHENYA A MULUNGU | GENESIS 15:5-6 | |
| 3. | MALINGALIRO AMKATI LUKA 2:19 | KULINGALI MAGANIZO A MULUNGU | AROMA 4:20-21 | KUFUNGATIRA |
| | CHIFUNIRO CHA MKATI MACHITIDWE 19:21 | KULANKHULA MAWU AMULUGU | GENESIS 17:5 | |
| ZOTSATIRA ZAKE | | KUFA KWA MASOPHENYA | GENESIS 16:2 GENESIS 17:18-19 | KUBADWA |
| | | KUUKA KWA MASO MPHENYA | GENESIS 21:1-2 AGALATIYA 4:4 | |

1. Kodi ndingagwire ntchito izi motani pa ntchito zina? Njira zina zatsopano zogwiritsira monga izi? Pali zinanso zogwiritsira ntchito ngati zingakonzedwe?

2. Kukopera? Pali yinanso ngati iyi? Kodi fundo zina ndi ziti? Kodi zakale zija ndi zosiyana ndi izi? Kodi apa ndionere kapena kukopera chiyani? ndani amene ndimukopere?

3.Kodi ingakonzedwenso bwanji? Njira yatsopano? Posintha tanthauzo mtundu, maonekeedwe? Pali kusintha kwinanso.

4. Kodi ichi chingakulitsidwe bwanji? Ndionjere chiyani? Nthawi yambiri? Kulilitsa kwamphamvu? Kulimba? Kukwera? Kutalika? Kukandapala? Maonekedwe apadera? Kukopera? Kuontchetsa/ kusinjirira?

5. Kuchepetsa? - kodi ndichotsere chiyani kapena ndifanize? chochepera? Chokhutala? Chotsikira? Chopepuka?

6. Cholowa mmalo? Mmalo mwake mukhale chiyani? ndani alowe mmalo mwake, chida china? Njira zina? Mphamvu zina? Malo ena? Kafikiridwe kena? Kalankhulidwe kena?

7. Kuchitanso dongosolo? - ndisinthenso? Ndithithikanitse? Ndiyalenso kawiri? Ndisinthe matalikidwe wina kwa mnzake?

8. Kubwezera mbuyo? - Kodi ndibweze mmbuyo? Ndi chitembenuze dodolido? ndibweze m'mbuyo machitidwe ake? Ndisithe nsapato?

Kuphatikiza? - Ndiphatikiza bwanji? Ndizitolera zonse pamodzi motani? Ndiphatikiza motani fundo izi?



KUONJEZERA TCHUTCHUTCHU WA UZIMU KUPYOLERA MU ZOLEMBERA ZAKO

Ambuye, ndilankhuleni kukhudzana ndi fundo izi zonse izi. Ndi ziti zonse izi. Ndi ziti mwa izi mukufuna ine kuti ndizitsatira pamodzi ndi kuchita nazo? ndi ziti zimene simukufuna kuti ine ndikhale wotchera khutu ku zimenezo pa nthawi ino? Kodi mukufuna ine kuti ndipitirire motani? (Lembera zimene ukuona kuti Ambuye akukulankhula).

CHIKONZERO PA ZOKAMBILANA MU KALASI

Ukonzekere kusonkhanitsa mafunso kapena fundo zimene ulinazo masomphenya ake. Uzilembe izo.

2. Konzekera kukambilana nonse pamodzi masomphenya aliwonse amene Mulungu waika mu mtima mwako. Nthawi zonse kukambilana kotere kumawalitsira chikhulupiriro mu mitima ya iwo amene akuvera ndipo zimabweretsa ulemelero kwa Mulungu.

3. Padzakhala kukambilana kwa padera za kugonjetsa kapena kuti kulalikira pa zotsekereza kuti munthu asalandire masomphenya. Ngati pali kulimbana kwapadera kuti ulandire masomphenya, bwera ndipo ukonzekere kukambilana kuti zovuta zako zikonzedwe ndipo mayankho apezeke. Ulembe zovuta zako zimene ukufuna kuti anthu

kupambana koyenera? Kupambana koposa? Chonde ndionetsereni mwa tchutchutchu.

5. Ambuye, ndionetsereni chokhumba chanu kupambana kwanga.
6. Ambuye, ndionetsereni umo kufikira cholinga kungatsegulire makomo kuzinthu zambiri zomwe muli nazo pa moyo wanga
7. Ndionetsereni mtengo wake ndingalipire kuti ndpeze ichi
8. Ambuye, ndionetsereni chimene chidzachitike ngati sindipambana.
9. Ambuye, ndionetsereni mapazi akulu enieni mmene ndiyendemo kuti ndipambane. Kodi pali deti yake yapadera pa phazi (sitepe) lili lonse?
10. Ndionetsereni zoletsa zomwe ndingakumane nazo pakati pa ine ndi kupambana kwanga kwa ntchito iyi. Ndionetsereni umo ndingazigonjetsere
11. Ndionetsereni zimene ukufuna kuti ndi chite lero zimene zidzayambitsa njira kupambana kwanga.

ZOYENERA KUCHITA - UFUNSE MAFUNSO AMENE AWALITSIRE ZOLINGALIRA ZAKO

Nthawi zina timaoneka ngati kuti tasokonezeka ndipo tikusowa chochita zimaoneka ngati kuti palibenso mavumbulutso atsopano kapena nasomphenya. Mu nthawi zonga zoterezi, ukhoza kugwiritsa ntchito mafunso awa ku vuto kapena zolinga zimene ukuzikonza kuti zikhale zabwino. Apa pali mafunso amene akonzedwa kukuthandiza kukonza vuto lako. Ndandanda wa mafunso wachiwiri waperekedwa womwe cholinga chake ndi kukhudzana ndi maganizo pa malonda, zinthu zina, komanso ntchito zina. Usankhe ndandanda wabwino wa mafunso ukufuna.

Mafunso onse awa ndi omakambilana pagulu osati wekha. Awa akukhudza ndandanda wa malingaliro pamodzi ndi kutambasula mphamvu yakuganiza kwako. Adzakuthandiza kumasula mphamvu ya kulenga yako komanso yapa gulu pa anthu komabe sikuti uku ndi kulenga kwa Mulungu. Udzayenera kutenga ndandanda wa mafunso awa ndi kuwapereka pamaso pa Mulungu mu pemphero uku ukupenyera pa Mulungu osati pa zimene



walembazo - kumufunsa zimene lye akufuna kuti alankhule ndi moyo wako kukhudzana ndi izo. Malo oti uchitire izi aperekedwa kumapeto kwa chaputala ichi.

A. MAFUNSO OGWIRITSA NTCHITO PAMENE UKUKONZA ZINTHU OSATI NTCHITO

(Mwa chitsanzo njira zochilitsira kupasuka kwa chibale pakati pa wina, ndi mnzake, fundo zolimbikitsa mgwirizano mu banja, fundo zoyanjanitsa anthu amene akutsutsana pa ziphunzitso, fundo zofufuza pokonza uthenga womangirira anthu.

1. Utchule mwa tchutchutchu vuto limene ukufuna kulingalira mozama
2. Kodi ndi njira ziti zimene anthu akhala akutsatira pokonza vuto lotere?
3. Kodi ndi njira ziti zoyenera zimene wazimva kapena ukuganizira zokonzera vuto limeneli?
4. Ujambule mmutu mwako chinthunzi cha Ambuye Yesu pokhudzana ndi vutolo. Kodi iwo akalikonza bwanji?
5. Ulembe njira zambiri zopezeka mu baibulo zimene zikhoza kuthandiza kuthetsa vutoli.
6. Kodi ndi njira ziti za mu baibulo zimene ukuona kuti zikhoza kusemphana ndi izo walemba kale?
7. Kodi nkuchokera ku njira ziti ukhoza kuonerera vutolo? Ndi fundo ziti zatsopano zomwe ukhoza kuonerera vutolo?

B. MAFUNSO OKONZEDWA KUKHUDZANA NDI FUNDO ZA MALONDA

Pamene ukufunafuna fundo za kulenga za kukhazikitsa pamodzi ndi zochitika za malonda a kanthu kena kake, mafunso otsatirawa ali aphindu kuti uwalingalire.

za kubadwa.

Masomphenya a Mulungu amapereka ku mtima luntha, pamodzi ndi mphamvu, kukachita mwa chikhulupriro komanso kuona zotsatira zake zodabwitsa zikuchitika.

Mkazi wanga pamodzi ndi ine takhala ndi masomphenya ambirimbiri amene takhala tikufungatira pa miyezi yambiri komanso ngakhale zaka za mbiri. Ena a iwo akwanilitsidwa koma ena adakalibe ofungatiridwa. Amodzi mwa masomphenya a mkazi wanga adali kukhala nyumba yaikuru ndi yokongola. Ndimadziwa kuti monga m'busa wampingo wochepa wokhala ku midzi izo zidali zosatheka. Mavuto azachuma sakadalola kuti izo zitheke. Koma pamene mpingo wathu udagula malo poti timange, padamangidwa nyumba yaikuru ndi yokongola. Awo adali makwanilitsidwe a maloto onse tidali nawo komanso apyolera kwathu. Masomphenya a Mulungu ofungatiridwa pa nthawi yaitali adabereka chozizwa ku miyoyo yathu kulolera zokhumba za mtima za mkazi wanga.

ZOYENERA KUCHITA - KUKHAZIKITSA ZOLINGA KU PYOLERA KU KULEMBERA MASOMPHENYA A MULUNGU

Mu chaputala chomaliza, mudayankha mafunso otsatirawa kumupempha Mulugu kuti akulankhule kukhudzana ndi funso lililonse pa lokha. Tsopano bwerera kumafunso awa ndipo pa nthawi ino upemphe Mulungu Kuti akupatse masophenya pa cholinga chake chilichonse pa chokha pokhudzana ndi moyo wako. Pamene ukupempha masomphenya ufunefune masomphenyawo. Udzaona kuti izo zidzachitika.

Ulembe chidule cha masomphenya aliwonse pamene ukuwaona. Ufunefune masomphenya pa funso lililonse mwa otsatirrawa. Ukhoza mwina kufuna kubwereza yankho ku funso lililonse lomwe Mulungu adakupatsa mu chaputala chomaliza usadayambe kufunafuna masomphenya ake. Kenako ndi mtima wako wonse wodzadzidwa ndi mawu, funafuna kuti uone masomphenya.



Okondedwa Ambuye, chonde ndionetseni masomphenya a zolinga zanu zomwe inu mukufuna kuti ndipenyerepo pa nthawi ino. Udikire kaye pang'onoo uku ukufunafuna chithunzi m'maganizo mwako (Daniel 7). Ndipo kenako lembera mwa chidule zimenezo kapena kuti uzifotokoze.

Mu moyo wanga wa m'banja.....

Mu kuyenda kwanga ndi Mulungu.....

Pa ntchito yanga.....

Posamalira umoyo wa thupi langa.....

Mu chibale ndi amzanga.....

Pa chuma changa.....

Mu utumiki wanga.....

PEPALA LOLEMBERA MASOMPHENYA

Pa pepala ili udzafunsa Mulungu za vuto lapadera kapena cholinga chimene Mulungu akufuna kuti ulingalirepo mozama. Ukatha kulandira yankho lake kufunso loyamba, kenako udzalemba mafunso onse otsala - amene adzakupatsa chidziwitso, cha yakho lako. Ufunenso masomphenya amene atsagana ndi mawu (rhema) kuchokera ku chaputala chomaliza yamba mwa kubwerezanso kulingalira mawu (rhema) kuchokera pa chaputala chomaliza.

1. Ambuye, mungathe kundionetsa mwa tchutchutchu cholinga chimene mukufuna kupindula mwa ine pa miyezi isanu ndi unodzi kutsogoloko?
2. Ambuye, ndiloleni ndione nchifukwa chiyani mukufuna kuti ndifikire chinthu ichi?
3. Ambuye, ngati ndingapambane, chonde ndionetseni zotsatira zake zidzakhala zotani?
4. Ambuye, kodi nchiyani chimene mudzawerengere kuti ndi

3. Kodi umatenga masitepe otetezera kapena kutsogolera zinthunzi zomwe zimayenda mu maganizo ako?

4. Kodi udazolowera ku kuyenda kwa masomhenya mu mtima pamodzi ndi mu maganizo ako?

5. Kodi zinthunzi zili za mphamvu bwanji mu aganizo ako ndipo umadzamva bwanji?

MABUKU OTI UWERENGE POGWIRITSA MPHAMVUYAKO YA KUONA MASOMPHENYA MU CHIYANJANO NDI MULUNGU

1. Pa kusanthula njira za thupi za mphamvu yakuona masomphenya Dr. Paul Yonggi yemwe ali chitsanzo amakhala ndi pakati pa maloto ndi masophenya adalemba buku lake ndipo uwerenge-limatchedwa "Miyambo yachinayi" (Fouth Dimensions).

2. Buku labwino lofotokoza kagwiritsidwe ka malingaliro mu utumiki wakuchira kwa munthu werengani buku lotchedwa "kuchilitsa zopweteka za mkati mwa moyo....." (Healing life Hurts) Lolembedwa ndi M'busa Dennis pamodzi ndi Matt Linn.

KUYESA MALOTO NDI MASOMPHENYA

Popeza maloto pamodzi ndi masomphenya akhoza kuchokera ku mzimu wako, mzimu woyera kapena satana nkoyenera kukhala wosamalitsa ndipo aziyesedwa ndi mawu a Mulungu. Maloto pamodzi ndi masomphenya okhwima adziperekedwa kwa mtsogoleri wa moyo wako wa uzimu. Chithunzi chotsatirachi ngakhale chili ngati chofanana ndi cha pa chaputala choyamba, chaperekedwanso kwa ine kuti uchisanthulenso komanso chikutsogolere pamodzi ndi kukuthandiza kuyesera maloto pamodzi ndi masomphenya.



KUYESA NGATI CHITHUNZI CHACHOKERA MU MTIMA MWAKO, KWA SATANA KAPENA KWA MULUNGU

DIAGRAM

UMBONI WANGA WA MASOMPHENYA A MULUNGU KUDZADZA MASO A MTIMA

Pamane timafuna kutumikira machilitso kwa mayi wosowa kwambiri mu mpingo wathu, mnzanga wogwira naye ntchito limodzi-mkuluwa mpingo pamodzi ndi ine tidapeza tasekerezedwa ndipotimalephera kupitirira kutero. Pamene ndidapemphera uku ndikudabwa kuti tsopano tichita chiyani, ndidapereka maso anga amtima wanga kwa Mulungu ndi kupemphera ngati pangakhale masomphenya amene amafuna kuti andionetsere. Mwa msangamsanga masomphenya a msungwana wocheperansinkhu wovutika wa zaka zakubadwa pafupifupi zisanu. Zaka zochepa mmbuyomo kudali kosatheka kulandira masomphenya otero chifukwa choti sindidali kupereka maso amtima wanga kwa Mulungu kuti awadzadze.

Ndidapenyerere ndipo kenako ndidagawana masomphenya ndi mayi wa zaka makumi atatu ndi mphambu zisanu pamaso panga ndipo ndidamufunsa iye ngati masomphenya adali ndi tanthauzo lililonse kwa iye. Zidaonetsa kuti adali mafungulo omukumbutsa kuchilitsidwa kwake pamene Mulungu adamubwezeretsa ku umwana wake kukachilitsa mavuto adali nawo omwe adayamba ali ndi zaka zisanu

chivumbulutso 4:1 Yohane adali kupereka maso ake a mkati kwa mzimu aone chimene Mulungu adzanena naye. Pavesi yachinayi tikuona kuti adatengedwa ndi "Mzimu" kukaona masomphenya a mpando wa chifumu. Nchosangalatsa kuona kuti sadatengedwe mwa mzimu kufikira pavesi yachiwiri- ndipo apa munthu akhoza kudabwa kuti kodi Yohane adali kuti pa vesi yoyamba asadatengedwe mu uzimu pa vesi yachiwiri? Ndipo nanga Yohane amachita chiyani kumene adali pa vesi yoyambayo?

Apa tikhoza kuona kuti cinthu chofunikira ndi kuzindikira kuti tikhoza kupenyerera zinthu mwa mzimu. Pa zaka zambiri sindidali kulabadira za maso a mkati ndipo ndimaona ngati zopanda pake basi. Sindidalandirepo masomphenya kuchokera kwa Mulungu. Tsopano pamene ndipereka maso anga amkati kwa Mulungu kuti awadzadze. Iye, ndimaona masomphenya pafupipafupi akuyenda mwa ine. Izi zikhoza kuchitika kwa wina aliyense ndipo pamene zikuchitika tidzayamba kuphunzira mozama za uzimu.

Fundo zotsatira izi zikuthandiza kuti uyambe kukhala omasukira Mulungu kumulola kuti adzadze maso a mtima wako ndi maloto pamodzi ndi masomphenya.

1. Uyenera kukhala chete mkati mwa moyo wako kuti mzimu woyera akhoza kupereka masomphenya pamodzi ndi kupereka zinthunzi.

2. Ona nkhani iliyonse ya mu baibulo pogwiritsa ntchito masomphenya. iyi ndi njira yodziwika ndi yogwiritsidwa ntchito ndi anthu ambiri. Uzilole wekha kupenya zimene ukuwerenga. Apa ukhoza tsopano kuwapempha Ambuye kukuonetsa zomwe iwo akufuna kuti akuonetse ndipo keneko kuyenda kwa mzimu kumayamba mwa iwe ndipo umayamba kuona motsogozedwa ndi Mulungu.

3. Utsegule maso a mtima wako mu nthawi ya kukhala chete kwako kumulola Mulungu kuti akuonetse zinthu. Ndaona kuti kupenyerera pa Yesu kufika Iye ayamba kuyenda kapena



kulankhula kumapangitsa zinthunzi za mzimu kukhala mwa ine (Aheberi 12:1-2).

4. Kupembedzera anthu ena (Kumuona munthuyo pamene ukumupembedzera komanso kuona Yesu ali naye munthuyo. Kenako upenyerere zimene Yesu akuchita naye ndipo pomaliza upemphere kuti zikwanilitsidwe.

5. Kumvetsera ku maloto ako amene ali chabe chionetsero cha zinthu za kudziko la uzimu. Pempha Ambuye kuti akulankhule mu nthawi ya usiku (Masalimo 127:2). Pamene wadzuka ku tulo tako, lembera msangamsanga maloto ako ndipo upemphe Mulungu kuti akuthandize kukutanthauzira. Iye adzachita.

6. Kupemphera mwa mzimu kumatsegula chiyanjano ndi mzimu woyera kupereka mwayi kuti zinthunzi za mzimu zifike makamaka pa nthawi imene ukupereka maso a mtima wako kwa Mulungu.

7. Pemphero la kachetechete limangoonetsa chikondi chako pa Yesu komanso chikondi chake pa iwe ndipo zotsatira zake zinthunzi za uzimu zimaumbika.

8. Mu nthawi ya kuyamika ndi kuthokoza uyenera kuona chimene ukuyimba ndipo ulole mzimu woyera kunyamula masomphenya komwe Iye akufuna.

KUPENYERERA MASOMPHENYA - ZOYENERA KUCHITA

Chonde, yankhani mafunso awa mwa chidule. (Ngati mphamvu yako ya kuona masomphenya inatsekerezeka pena pake pazifukwa zina, chonde onani ku mapeto a bukuli....."Kulolera Mulungu kubwezeretsa mphamvu yako yoona masomphenya.

2. Kodi ukuzindikira za zinthunzi zomwe zikuyenda mu maganizo ako?

KUSINTHA KWA KULENGA KUMACHITIKA POPENYERERA ZOSAONEKA NDI MASO

Baibulo limatiuza ife umo tingalengere zinthu mu miyoyo yathu komanso mu dziko mmene tiri (II Akorinto 3:18). Munthu amasandulika ponyerera pa zinthu za uzimu zosaoneka ndi maso a thupi. Ngati tingapenyere pa zinthu zooneka ndi maso, sitingathe kulenga kanthu. Ngati tipenyerera ndi diso lathu la mkati pa zinthu zosaoneka ndi maso a thupi, ndipo kenako tifungatira mwa mzimu mu mtima wathu, Mulungu adzadzikwanilitsa izo mu nthawi yake kuti tsopano zionekere poyera ( Miyambo ya dziko lachitatu).

Talingalirani chozizwitsa cha Petro pamene amayenda pa madzi monga ngati chitsanzo. Nkhaniyi ikupezeka pa mateyu 14:28-32). Yesu adalankhula mawu (rhema) pomuuza Petro kuti abwere kwa Iye pamadzi. Petro adachita mwa chikhulupiriro-kuturuka mu bwato.....Petro....."adaona masomphenya...." popenyerera maso ake pa zimene Mulungu adaziika wa Yesu. Chozizwa chidachitika. Mphamvu za kulenga zidamasulidwa mu moyo wa Petro ndipo adayenda pa madzi. Chozizwa ichi chidadulidwa chifukwa choti mmalo moyang'ana pa zimene Mulungu adaika wa Yesu, Petro adayamba kupenyerera zooneka ndi maso. Nthawi yomweyo mphamvu ya uzimu idachika ndipo Petro adayamba kumira. Umu ndimo mphamvu zakulenga zimamasulidwa pamene tikupenyerera pa zinthu zosaoneka ndi maso.

Mulungu amatipatsa masomphenya a uzimu ndi cholinga kuti tidzapenyerere pa iwo ndipo pakutero mphamvu zake za kulenganso zimasulidwa mu mtima yathu....."pakuti tiyendayenda wa chikhulupiriro simwamaonekedwe....." (II Akorinto 5:7....."

....."MMALO AMENE UMAPENYERERA MASO AKO PAMODZI NDI MALO AMENE UMATCHERERA KHUTU LAKO AMAFOTOKOZA NGATI NDI CHIKHULUPIRIRO CHA MTIMA KAPENA AYI....."



....."Ndi kupenyerera woyambirira ndi womaliza wa chikhulupiriro chathu.....Yesu" (Aheberi 12:1-2)

KUPHUNZIRA KUPEREKA MASO A MTIMA WATHU KWA MULUNGU

Mawu a mu chiheberi a mneneri ndi "mulosi." Mneneri ali mulosi - munthu amene amaona masomphenya pamodzi ndi zolinga za Mulungu.

Pa II Mafumu 6:8-20, tikuwerenga nkhani ya Elisa ndi maimidwe ake potsutsana ndi a Aaramu. Pamene adazinga pa malo pokhala Elisa nyamata wake adachita mantha popeza adali kupenyerera zooneka ndi maso koma Elisa adali kuona zinthu za uzimu ndi diso lake la uzimu. Pamene adapemphera kuti Ambuye atsegule maso a mnyamata adaona kuti pa phiri padadzadza ndi kavalo ndi magareta a moto akumzinga Elisa.

Tiyenera kuphunzira kumaona zinthu mwa mzimu osati mwa thupi mokha ayi. Tiyenera kuphunzitsidwa kuti tizindikire izi kuti ifenso tiziona zinthu mwa uzimu. Poyamba tiyenera kuphunzira kuzitonthoza tokha pamaso pa Mulungu. Mmalo monganizira kuti maso athu a mkati ali bwino pa zolingalira zokha za moyo wa thupi, tiyenera kumaona kuti tikhoza kuwapereka pamaso pa Mulungu ndipo pakutero amadzadziwa ndi maloto pamodzi ndi masomphenya a uzimu.

Habakuku adapita pa malo a yekha ndikukaziika palinga kuti aone Mulungu adzanenanji kwa iye ndipo Mulungu adamupatsa masomphenya kuti awalembe (Habakuku 2:1-2). Habakuku "mneneri adaphunzira kupereka maso ake a mkati kwa Mulungu pamene amapemphera kuti alandire maloto pamodzi ndi masophenya a Mulungu.

Mtumwi Yohane adaperekanso maso a mkati mwake kwa Mulungu pamene adali kudikira kulandira kulankhula kwa Mulungu. Lembani Chivumbulutso 4:1-2 pansi apa. Ndifotokoze motere kuti pa

Mulungu adazindikira kutichithunzi kapena kuti masomphenya adzazamitsa pamodzi ndi kulimbikitsa mawu olankhulidwa (rhema) ndipo pakutero adaonjezarapo ku mawu olakhulidwa masomphenya a lonjezolokwanilitsidwa. Mulungu adampatsa Abraham masomphenya a thupi: Nyenyezi za kumwamba pamodzi ndi mchenga wa mnyanja. Monga mtumwi Yohane adalemba buku la Chivumbulutso, Mulungu adampatsa iye masomphenya. Zitsanzo ziwiri izi zifotokoza momveka bwino kuti Mulungu amakhonza kupereka masomphenya a kunja komanso mkati.

Ndikukhulupirira kuti kulandira masomphenya kumakhazikitsa chikhulupiriro cha mtima. Ndi kukhulupirira kuti pamodzi ndi mawu olakhulidwa ndi Mulungu (rhema), Mulungu amapereka malonjezano, maloto pamodzi mdi masomphenya omwe adzakhala pamodzi ndi kulimbikitsa chikhulupiriro.

Pamene munthu wojambula pa pepala akufuna kujambula nyumba yatsopano, poyamba amayamba ndi kulingalira mmutu mwake-(rhema). Kenako aijambula nyumba ija mmutu mwake. Kenako tsopano a mayamba kuilenga (kulemba).

Palibe chinthu chimene chimakhala chisadayambe chaganiziridwa mu maganizo a munthu. Kuona chinthu ndi zotsatira za kukonzedwa kwa chinthucho mu maganizo a mutu mwa munthu. Kuona chithu ndi zotsatira za kukonzedwa kwa chithucho mu maganizo chabe a munthuyo. Anthu ozindikira za kafukufuku wa zinthu (scientists) apeza kuti magulu awiri a anthu amagwiritsa ntchito zofanizira ndipo magulu awa ali akuruakuru pamodzi ndi ana ndipo onse awiri awa ali ndi mphamvu ya kulenga. Albert Einstein adalakhula motere, ...."kuganizira kuli kofunika kuposa chidziwitso....." Shakespear adalankhula motere ....."kuganizira kumapangitsa munthu kukhala wotsogolera nyama ....." Disrael adalakhula kuti ....." kuganizira kumalamulira dziko lapansi....."Aristole yemwe adapeza chinsinsi chakuganiza komanso kagwiritsidwe ntchito ka zinthu adalemba



motere....."Nkosatheka kuganizira popanda chithunzi cha zoganizazo kuumbika mu bongo la munthu ....."

MIYAMBA YACHINAYI IDALENGA MIYAMBA YACHITATU

..... "Ndi chikhulupiriro, tizindikira kuti maiko ndi a mmwamba omwe anakozedwa ndi mawu a Mulungu kotero kuti zinthu zopenyeka sizinapangidwa zochokera mwa zooonekazo...(Aheberi 11:3).

Ndikukhulupirira kuti Mulungu adaona dziko looneka ndi maso mkati mwa mzimu wake ndipo kenako adalenga miyamba itatu ya dziko kuchokera mu masomphenya a mu mtima wake. Kena kalikonse kamene kali mu miyamba yachinayi lomwe ndi dziko la uzimu ndi kukonzedwa mu miyamba ya chitatu.

Yesu, chitsanzo CHANTHU, ADAKHALA NTHAWI ZONSE WOTCHERA KUMASOMPHENYA

Ambuye Yesu, adakhala moyo wa dziko lapansi mwa mawu pamodzi ndi masomphenya ....."Ndipo zimene ndazimva kwa Iye, zomwezo ndilankhula kwa dziko laapansi....."(Yohane 8:26)

....."Zimene ndinaona Ine kwa Atate, ndilankhula ndipo inunso muchita chimene mudamwa kwa atate wanu....." (Yohane 8:38)

....."Ndipo sindichita kanthu kwa ndekha koma monga anandiphunsitsa Atate....." (Yohane 8:28)

Ifenso tiyenera kukhala mwa mawundi masophenya nthawi zonse. Mu njira yotere, tidzakhala mu chifuniro cha Atate komanso tidzayenda monga Yesu Khristu adayendera.

aliyense adakalingalira mwa iye yekha payekha.

- Tidakomananso tonse pamodzi ndi kusankha fundo yeniyeni.
- Sitidatsutsane
- Pamene tidayamba kukambilana kwanthu mwa gulu pofotokoza malamulo anayi awa otsatira. Tidawalemba pa bolodi (kuweruzana pamodzi ndi matsutsano zidaletsedwa). Aliyense adali womasuka. Tonse timafuna kutchuka kwa zinthu, fundo zonse zikhale za phindu.
- Tidafuna phata la vuto
- Mavuto omwe tidasankha kuti tikambilane adali oti timangiriraneosati kuweruzana.
- Gulu lathu lidali la anthu khumi ndi awiri ndipo tidakakambirana
  mphindi makumi atatu ( 30 minutes)
- Tidalewa mzimu wodziyeretsa tokha.
- Tidalimbitsa fundo zimene zidali za phindu.
- Padalibe munthu wolembera zokambilanazo.

MALAMULO OTSATIRA NJIRA YOKAMBIRANA MWAGULU

1. KUWERUZANA PAMODZI NDI KUTSUTSANA NKOLETSEDWA
2. KUMASUKA KWA MUNTHU KUPEREKA MAGANIZO AKE KULI KUVOMEREZEKA.
3. KUMAFUNAFUNA KUCHULUKA KWA ZINTHU.
4. FUNAFUNANI KUPHATIKIZANA PAMODZI NDI KUZUMITSA MAGANIZO A ANTHU ONSE.



Chaputala 6

KUDZADZA SENSI YACHIWITI YA UZIMU WA MUNTHU POPENYERA MASOMPHENYA A MULUNGU

"Kuphatikiza kulankhula kwa mulungu ndi masomphenya ochokera kwa Mulungu."
Chigawo chachiwiri cha mtima wathu chimene chimagwira ntchito yolandira mavumbulutso a Mulungu ndi "maso a mitima yathu"(Aefeso 1:18). Monga maso athu a thupi ali chiwalo choyambirira kulandira pamodzi ndikupenya zochotika mu dziko la thupi ili, chomwecho maso athu a uzimu ali sensi yoyambirira kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kutipatsa ife vumbulutso kuchokera ku dziko la uzimu. Kuchokera ku Genesis mpaka ku Chibumbulutso, Mulungu amapereka maloto pamodzi ndi masomphenya iwo amene adali kumufunafuna lye. Maloto pamodzi ndi masomphenya awa ali ofunika pokhazikitsa chikhulupiriro cha mtima.

| | SENSI | KAGWIRITSIDWE NTCHITO UMO IMFA | CHITSANZO CHA M'BAIBOLO | SITEJI |
|---|---|---|---|---|
| 1. | MAKUTU AMKATI KHUTU LA MKATI | KULANDIRA MAWU A MULUNGU | GENESIS 12:1-3 | KATENGA PAKATI |
| 2. | MASO A MKATI 2 CHIVU LUTSO 4:1 | KULANDIRA MASO MPHENYA A MULUNGU | GENESIS 15:5-6 | |
| 3. | MALINGALIRO AMKATI LUKA 2:19 | KULINGALI MAGANIZO A MULUNGU | AROMA 4:20-21 | KUFUNGATIRA |
| | CHIFUNIRO CHA MKATI MACHITIDWE 19:21 | KULANKHULA MAWU AMULUGU | GENESIS 17:5 | |
| ZOTSATIRA ZAKE | | KUFA KWA MASOPHENYA | GENESIS 16:2 GENESIS 17:18-19 | KUBADWA |
| | | KUUKA KWA MASO MPHENYA | GENESIS 21:1-2 AGALATIYA 4:4 | |

yokambilana zinthu mwa gulu, maganizo onse a anthu amalembedwa pa khadi (mmutu kapena chilichonse) ndipo tsopano amaikidwa papepala yolembera monga tikuonera.

Pamene njira yokambilana zinthu mwa gulu yatha, ganizo lililonse palonkha limachongedwa malingana ndi kufunikira kwake, ndondomeko yake malo ake. Maganizo amene apezeka kuti ali opanda pake achotsedwa nthawi yomweyo. Malo ena aja amasinthidwa malingana iwo ali oyenera kuti akahale.

ZOKAMBILANA ZINA MUKALASI MASABATA AKUSATIRAWO

Monga nkalasi, mukhoza kugwiritsaa ntchito njira izi mwakusankha mutuwa nkhani kuti mukambilane ndipo mukhadzikitse fundo zomwe muzilembe pa bolodi kapena papepala. Kumbukirani kuti ndi kwabwino kusankha mutu umene uli wosangalatsa kwa anthu onse. Fundo ngat izi ..... "umo mungakhalire ndi ana osamvera"...."umo ungaonjezerekudzipereka kwa mwana wako kwa Ambuye ..."kapena kwa abwezi ako ...."Umo ungakhazikire chikondi cha muyaya ..." Chonde, khalani omasuka kuonjezera mitu yina yosangalatsa mu nthawi ya kukambirana kwanu mukalasi.

ZOMWE NDAZIONA PA MOYO WANGA

Popeza chaputala ichi ndi chofunika kudzadzitsa kwa sensi yoyamba ya mzimu wa munthu mwa kumva kulankhula kwa Mulungu, ndiloleni kugawana nanu chitsanzo changa umo mawu olankhulidwa ndi Mulungu andipatsira chikhulupiriro cha mtima wanga pa mavuto.

Kagulu ka anthu kochokera ku mpingo womwe ndidali kutsogolera monga m'busa kadandipeza atatenga kalata yondiuza kuti ndisiye kugwira ntchito yaubusa pa masabata asanu ndi limodzi pamene mpingo uzikonza zavuto lina pakati pathu. Pamene ndidafunafuna Ambuye kukhudzana ndi ichi, Iye adalakhula ndi ine kuti sandichotsa pa mpando wa udindo woyang'anira mpingo.



Nditatha kulandira chilimbikitso kuchokera kwa "onditsogolera pa moyo wa uzimu, " ndidayamba kuyenda mwa chikhulupiriro potsatira zomwe adandiuza.

Pamene mphepo izi zimandiomba ndidapezeka kuti masabata asanu ndi imodzi otsatira adali opambana kwa ine ndipo ndidazama mu mawu a Mulungu zomwe zidali zisadachitikepo ndi kale lomwe. Mulungu adatsegula maso anga kuti ndizindikire malembo opatulika modabwitsa ndipo uko kudali kuyala kwa maziko a choonadi omwe ndidzagwiritsa ntchito pa moyo wanga wonse. Choonadi ichi chikuwakhuza anthu ena amene ndikugawana nawo. China mwa choonadi ichi ndi chimene chikugawidwa mu buku ili.

Masabata asanu ndi limodzi atatha, Mulungu adapitirira kulankhula ndi ine kuti ndipitilizebe kutsogolera anthu monga m'busa ngakhale kuti ndidali kufuna kusiya malingana ndi maganizo a umunthu wanga. Patapita miyezi iwiri pamene kuchira pamodzi ndi kubwezeretsedwa kwa zinthu kudali kuchitika, Mulungu adandiuza kuti ndileke.

Nditatha kulandira malangizo kuchokera kwa "onditsogolera pa moyo wanga wa uzimu" ndida lekadi kutsogolera mpingo monga m'busa popanda ntchito iliyonse yoti ndizichita ndidangopezeka mmanja mwa Mulungu. Mulungu adalankhula nane kuti Iye adzayambitsa mwa ine pa miyezi yammbiri. Ndidakhala ndikuyembekezera ndi kuzizwa pamene Mulungu adachita chimene munthu sangachite mwa iye yekha. Iye adandipatsa chokhumba cha mtima wanga mu utumiki wa kuphunzitsa mawu. Zoonadi kulankhula kwa Mulungu kudandipatsa luntha pamodzi ndi chisomo kunditsogolera ine mwa phindu pa nthawi yovuta ya kusintha kwa moyo wanga.

ZOYENERA KUTI UCHITE

MALAMULO OKAMBILANA MWA GULU : (uyankhe kuti "Inde" kapena "Ayi")

- Timaika nthawi padera yolingalira mozama
- Titatha kulingalira tonse pamodzi ndidabweranso ndipo

## 2. YOLEMBA PA BOLODI

Iyi ndi njira yina imene ili yosiyana kwambiri ndi njira yokambilana pa gulu. Iyi imathandiza kuona madera ena a pulani pamene ikukonzedwa. Idayamba kugwiritsidwa ntchito ku ma fakitore pothandiza kukoza ma filimu. Padakali pano imagwiritsidwa mu mahotela, mabungwe a za maphunziro, komanso aza zipembedzo. Njira iyi imathandiza motere:

- Imathandiza mu nthawi ya zokambilana pagulu

- Imathandiza kuti fundo imene mukukambilana pa gulu imveke bwino.

- Imathandiza kukonza dongosolo la zinthu zoti zichitike kuti ziyende mwa tchutchutchu.

- Imapereka mphamvu ya kutsitsimutsa yakulenga.

Iyi ili ngati chimodzimodzi ndi njira yomwe amakonzera pamodzi ndi kufalitsa nkhani mu wailesi. Mulingo wake wa kadi yopangira chida chogwiritsira njira iyi ndi (81/2 x 11 - pepala yotaipidwa). Iyi ndi yoika pamwamba. Yotsatira ikhale ya muyeso wa (pafupifupi 5 x 7). Iyi ndi pepala logwiritsidwa ntchito polemera mitu yaikuluikulu yoti ikambidwe yomwe yakonzedwa. Koma yochepera ikhale (3 x 5) ndipo iyi imagwiritsidwa ntchito kulembera mutu uliwonse wa zokambilana pawokhapawokha (onani chinthunzi chotsatira).






Apa zikuonetsera makhadi oonetsa fundo yokambidwa.

Pogwiritsa ntchito malamulo afotokozeredwa kale okhudzana njira yokambilana pagulu zinthu, munthu aliyense payekha kapena timagulu tayamba kutumiza makhadi wo mmalo oyenerera pa bolodi. Kumbukirani kuti tikulimbira zambiri osati zochepa. Maonekedwe abwino adzafufuzidwa pomaliza pa zonse. Mu nthawi ya njira

chikhulupiriro cha Abrahamu ndipo utero. Ukhoza kulembera fundo zina zofunikira.

KUBWERERANSO KU KULEMBERA MUTATHA ZOKAMBIRANA

Njira yokambilana zinthu mwa pagulu ikuthandiza kukonza zinthu zambiri. Kupyolera mu kulembera fundo zonse zokambilana pa gulu, umakhoza kuona zinthu zomwe umalakwitsa. tsono ukhoza kuzibweretsa pamaso pa Ambuye kuti uone chimene angakuyankhe. Adzakuonetsa fundo zoyenera kutenga komanso zoyenera kusiya. Chenjezo: Onetsetsa kuti maso ako asakhale pa zimene ukupenyazo pamene wabwera nazo pamaso pa Ambuye. Maso ako ukweze kwa Ambuye. Apa udzalandira yankho lenileni lochokera kwa Ambuye.

Komanso ngati wakhala ndi zokambilana za pagulu mukalasi kukhudzana ndi umo ungapititsire patsogolo njira yolumikizana kunyumba kwako ukhoza kulembera pamodzi ndi kugwirira ntchito limodzi ndi fundo zonse zomwe zidaperekedwa mkalasi muja.

NJIRA ZIWIRI ZOSIYANA ZOKHUDZANA NDI KUKAMBILANA KWA PAGULU

Pali njira zosiyanasiyana zomwe tikhoza kuziona panjira ya kukambilana mwa gulu. Panopa titangogawana ziwiri zokha. Yoyamba tiyitcha kuti "Ya nthambi ndipo yachiwiri tiyitcha kuti, "Yolemba pa bolodi"

YA NTHAMBI
Apa tiona kuti ndi njira yosiyana zedi osati kungosonkhanitsa maganizo ako pamodzi ndi mutu waphuziro lako patsogolo pa tsamba kapena pa bolodi mwa kagulu kochepa ka anthu. Pamene waona fundo yina yake yomwe wina wapereka, koma yothandiza, ulembere ndipo uchite maki. Ngati fundo yina yaperekedwa, uchite maki - chonga chimodzichimodzi ndipo kena. Ubwerenso kufundo yoyamba ija yomwe ili mutu wa nkhani yonse. Pamene uzikatsiliza zonse pepala lako lidzaoneka motere:






Mwina ukhoza kufuna kukhazikitsa maganizo ako achiwiri pa pepala lapadera apa palibe vuto. Ukhoza kutero. Pa nthawi imene muli pa gulu kukambilana, ukhoza kulembera kena kalikonse kobwera mu maganizo ako. Pali ubwino uwiri wopezeka mu njira yoyamba yotere. Poyamba zimakuthandiza kuti maganizo ako akhale omwazikana osati amodzi okha. Kachiwiri, ukhoza kosonkhanitsa pamodzi paganizo onse ofanana.

Pamene njira yokambilana pagulu yatha apa tsopano udzafuna kusankha maganizo, malembo opatulika, zitsanzo ndi zina zotere zomwe ukuona kuti zikuchitira umboni mkati mwa mtima wako ndipo kenako uyambe kugwira ntchito ndi zimenezo.

Timayang'ana pa vuto kupyolera mbali imodzi ndipo pakutero timakhala ndi masomphenya ochepera ndipo izi zimalepheretsa Mulungu kuti achite zomwe akufuna kupyolera mwa ife masomphenya atchutchutchu ndipo zoterezi Mulungu satichitira pafupifupi ayi.

Mulungu watipatsa ife njira yoti tidzitsegulana maso tokhatokha ndipo njira iyi wotere imatchedwa kuti "kukonzanso bongo."

FUNDO ZA KUOMBA BONGO (KUKOZA)

1. Iyi ndi misonkhano imene cholinga chake ndi kukunza fundo zimene patsogolo pake zikhoza kugwiritsidwa ntchito kukonza mavuto.
2. Ubwino wina ndi woti imapereka fundo zabwino mu nthawi yochepa.

MALAMULO AKE

1. Kuweruzana pamodzi ndi matsutsano sali ovomerezeka
2. Kumasuka nkofunikira
3. Uzifunafuna kuluka kwa zinthu
4. Uziyesetsa kugwiritsa ntchito fundo zonse zafotokozedwa pamwambapa.

FUNDO ZINA ZOONJEZERA

1. Ukhale ndi tchutchutchu wa vuto lomwe uli nalo
2. Gwiritsa ntchito njira yoitana mnzako kukukambilana osati kutsutsana kokha
3. Chiwerengero cha anthu ofunika pa zokambilana pothetsa vuto chizikhala khumi ndi awiri (12). Ukukambilana pa mphindi makumi atatu 30 basi.

4. Muyambe zokambilanazo pogwiritsa ntchito fundo zinayi zomwe zili pamwambapa. Izi muzilembe pa borodi.
5. Thawani mzimu wodziyeretsa nokha



6. Mulimbikitse maganizo okhawo amene mudamanga poyamba amene aliyense payekha amakhala womasuka kumaganizo a mnzake
7. Pakhale wina wolembera ganizo lililonse lokambidwa.

NCHIFUKWA CHIYANI NJIRA YOKAMBIRANA IYI IMAGWIRA NTCHITO

1. Kupyolera mu kukambilana, aliyense amaonetsa mphamvu ya kulenga yake
2. Anthu amaganiza mozama akakhala pagulu
3. Pamene mukupikitsana pa maganizo kuzama kwanu polingalira kumaonjezeka ndi 50%
4. Kuvomereza maganizo onse a anthu kumapindulitsa aliyense payekha kuchikhalidwe chake

ZOYENERA KUTI MUCHITE MU KALASI

Mupange malamulo ndipo mukambilane ndipo kenako muwayese. musankhe phunziro limene lili losangalatsa kwa onse osati loweruzana komanso osati lovuta. Wina akhoza kumalembera njira zosiyanasiyana zoperekedwa ndi anthu pa gulupo. Gulu lina lomwe ndidachita nalolidabwera ndi maganizo 100 pa mphindu makumi atatu (30). Sabata yotsatirayo tidapereka kwa aliyense kope la maganizowo.

Mukhoza kumva bwino komanso kusangalala pa nthawi ya kukumbilana kwanu. Mugwiritse ntchito pepala ya mageredi yomwe uli pa chaputala chotsatira ndipo uzipatse mageredi wekha.

ZOYENERA KUTI UCHITE KUNYUMBA

Ngati siudamalize ntchito idaperekedwa mwa kulembera, bwereranso ndipo umalize monga mbali imodzi ya zochita zako za pa sabata. Ukhoza kufuna zomwe udalembera, apa ukhale pansi pamodzi ndi anzako ndipo mukambilane ndipo uone zotsatira zake. Ulembere pansi apa zonse zimene wapeza ku mafunso muchaputala ichi. Uwerengenso Genesis 22:19. Uzipangitse wekha ngati kuti uli mu

KUKHAZIKITSA ZOLINGA ZA MOYO KUPYOLERA MU KULEMBERA

Okondedwa Ambuye, kodi zolinga zanu pa moyo wanga zimene mukufuna kuti ndipenyerere izo ndi ziti pa nthawi ino? Pa moyo wanga wa m'banja?.....

Pa moyo wanga wauzimu .....

Ku ntchito kwanga.....

Pa chisamaliro cha umoyo wanga wa thupi.....

Pa chibale ndi amnzanga.....

Pa moyo wanga wa uzimu.....

Ku ntchito kwanga.....

Pa chisamaliro cha umoyo wanga wa thupi.....

Pa chibale ndi anzanga.....

Pa chuma.....

Pa utumiki.....

KULEMBERA MWAKATHITHI

Pa pepala ili udzafunsa MUlungu pa vuto lililonse lapadera kapena cholinga kuchimene lye ayenera kutchera khutu pa nthawiyi. Utatha kulandira yankho lake ku funso loyamba, kenako udzalembera mafunso otsalirawo amene adzakupatsanso chidziwitsa mu kuyankha kwake.



1. Ambuye mungathe kundifotokozera cholinga chapadera chimene mukufuna kupeza mwa ine pa miyezi isanu ndi umodzi ikubwerayo (kapena madera amene mukufuna kuti ndigwire tchito)?
2. Ambuye, nchifukwa chiyani mukufuna kuti ndikhale ndi izi?
3. Ambuye ngati ndingapambane, kodi zotsatira zake zidzakhala zotani?
4. Ambuye, kodi mungaganizire chiyani kukhala chokhonzeka? Kupambana kwabwino kupambana kopyola?
5. Ambuye, ndilankhuleni kukhudzana ndi chokhumba chanu pakupeza kwanga zinthu izi?
6. Ambuye, kodi kupeza chinthu ichi kudzanthandiza bwanji kuzolinga zambiri za moyo wanga?
7. Kodi ndidzalipira mtengo wotani kuti ndipeze ichi?
8. Ambuye, chidzachitike nchiyani ngati sindidzakhoza?
9. Ambuye, kodi ndi masitepe angati akuluakulu kuti ndipeze ichi? Kodi pali tsiku lake pa sitepe iliyonse.
10. Ndi zokoma zotani zomwe zilipo pakati pa ine ndi kupambana kwa kumaliza kwa ntchito iyi? Nanga zidzagonjetsedwa bwanji?
11. Kodi mukufuna ine kuti ndichite chiyani lero chimene chikhale sitepe yoyamba yopezera zolinga zanga?
12. Ambye, chonde ndipatseni masomphenya a tchutchutchu a chinthu ichi (Lembera masompenya amene Mulungu wakupatsa)

KUTAMBASULIDWA NDI MUNTHU: KUKONZANSO BONGO NDI NJIRA YAKE

Sikuti tizingololera Mulungu ku tambasulira ife komanso tidzilolera munthu kutitambasulira. Mu kuchuluka kwa uphungu pali chipulumutso. Tikufuna khristu pamodzi ndi thupi lake komanso osatenga malo a munthu wina.

Ukhoza kufunsa motere, "nchifukwa chiyani Mulungu salankhula ndi ine mwa tchutchutchu? Nchifukwa chiyani ndiyenera kupita kwamunthu yemwe sali wangwiro? "mafunso abwino. Ndikukhulupirira kuti mbali imodzi ya yankho ikupezeka mu fundo yoti nthawi zambiri timakhala ndi kupenya kwa malire.

pa moyo wathu wa uzimu amatiteteza pamodzi ndi kutiphimba kuti tisakondwe mu chisokonezo kapena mu njira za satana.

Baibulo limafotokozera ife kuti tiyenera kumverana wina ndi mnzake mkuopa khristu (Aefeso 5:21), makamaka iwo amene akuyang'anirana miyoyo yathu (Aheberi 13:17) pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatu maneno onse ayenera kutsimikizilika. Ndimaona kuti ndi choyenera kudzipereka kwa anthu atatu nthawi zonse. Ngati pali china chake chapadera mu moyo wanga, ndimachipereka pamaso pa atsogoleri anga - kuwapempha kuti achipepherere ndipo ndione chimene Mulungu alankhule kukhudzana ndi zimenezo. Ndimadikira kufikira ndaona kuti pali umodzi pakati ife anthu anayi ndisadachite chilichonse. izi zandipatsa chitetezo chokwanira pa moyo wanga zaka zadutsazo.

KUKHAZIKITSA OKUFUNGATIRA PA MOYO WAKO WA UZIMU

Pamene ukukhazikitsa okuyang'anira pa moyo wa uzimu uyenera kuzindikira poyamba kuti Mulungu waika anthu otere kale mmalo ake, mwa chitsanzo, mamuna wako, m'busa wako, m'bwana wako. Poonjezera pa awa, ukhoza kukhazikitsa ena okuyang'anira motsogozedwa ndi awo kale amene uli nawo kale amene uli nawo pa nthawiyi. Ngati zili chomwecho, udzafua kupemphera kwa Mulungu kuti akuvumbutsire munthu woyenerayo. Ayenera kukhala munthu amene
(a) akuzindikira baibulo
(b) amatha kumva kulankhula kwa Mulungu
(c) ndi mnzako
(d) ndi wodzipereka kwa ena
(e) ndi wofuna kukhala pa chiyanjano ndi iwe

KUPENYERERA MASOMPHENYA AKO - ZINTHU ZITATU ZOPENYERERA

Pamene ukutchera khutu lako lauzimu, poyamba uyenera kuona kumene wakweza maso ako kupenyerera. Ngati udzayang'anira



mwa wekha apa ndiye kuti zonse zizichokera mwa iwe wekha mu mtima mwako. Ngati udzipenyerera pa zonse pa chinthu ukufunacho zonse zikhale zochokera pa icho. Ngati uzipenyerera pa Yesu, zonse zidzachokera kwa Yesu. Fundo ndi yoti zinthu zimabwera kwa iwe mogwirizana ndi pamene umapenyerera mu nthawi ya kupemphera kwako. Ichi ndi chifukwa chake kuli kofunika kuti tidzipenyerera pa Yesu pamene tikupemphera. Ngati uli ndi vuto loti upereke kwa Iye uzimuona Iye akukuona nalo vutolo komanso akuthana nalo. Uwonetsetse chimene akuchita komanso chimene akulankhula ndipo ukatero udzakhala ndi yankho loona lochokera ku mpando wa chisomo wa Mulungu.

KUONANSO MASITEJI A KULENGA

Munthu wakusonga pa kulenga adzakhala iye amene sadayambe waonapo mphamvu ya kulengayo ikuyenda mwa iye. Iye akukhalabe mu malingaliro a mmutu mwake monga munthu. Munthu amene angalenge ndi yekhayo amene adaonapo mphamvu ya kulenga mwa iye. Amene maso ake amakhala pa Yesu nthawi zonse (Aheberi 12:2), pamene akutchera khutu ku mzimu. Munthu wotereyi adzakhala ndi mphamvu ya kulenga ya Mulungu wamphamvu yonse.

Musangokhala okhutitsidwa ndi kukhala ndi mphamvu yakulenga mtima wa munthu. Landirani mphamvu ya kulenga ya mtima wa Mulungu.

KUTAMBASULIDWA NDI MULUNGU
Mulungu akulankhula kuti njira zanthu sizili zake ndi maganizo athu sali maganizo ake. Mwa ichi pamene tifika kulankhula kwake, nthawi zonse timapeza kuti mwatiuza kuti tichite zinthu zimene zili zosiyana ndi zimene timaganizira. Iye amatichilitsa kuti tikhale tcheru ku zinthu zimene timaganiza kuti tiziona mokwanira. Nthawi zina, Iye amatiuza ife kuchita zinthu zimene zimaoneka ngati zopanda pake. Nkoyerera kwa ife kumangochita zonse watilangiza komanso zolinga zake pa moyo wathu. Pansi apa, chonde mulembe malangizo amene mukufuna kuti Yesu akupatseni pa madera onse a moyo wanu.

Zonse zokhudza za uzimu ziyenera kuyamba zaperekedwa kwa wotsogolera wa moyo wako zisadayambe kutsatidwa. Nkoyenera kuti zonse zili pamwambapa zisadayambe kutsatidwa, munthu yemwe akuwerenga bukuli ayenera kuwerenga buku lotchedwa "kulankhulana" la Marck Virkler. Ndipo pempho langa kuti zonse zimene Habakuku amaziona pa moyo wake wa uzimu iwenso uzione pa moyo wako. Palinso zolemba zina zomwe akhristu akhoza kuitanitsa kuti athandizike.

KULANKHULA KWA MULUNGU KUMABEREKA MPHAMVU YA KULENGA MWA MUNTHU

Mphamvu ya kulenga ya Mulungu imayamba ndi kulankhula kwake kumene nthawi zambiri kumabwera ngati mwa maganizo mutu mwathu. Ganizo ili nthawi zonse limafika modzidzimutsa. Ichi ndi chifukwa chake kumakhala kofunikira kuti tidzikhala otchera khutu pamene mphamvu ya kulenga ikuyenda mwa ife. Pamene ganizo lafika mutu mwathu ndi chinthu cha nzeru kupereka nthawi chifukwa choti ganizolo likhoza kukhala la phindu kuposa umo timaganizira.

KUYESA KULANKHULA KWA MKATI MWA MOYO

Kufuna kuti tikhale ndi chikhulupiriro kuti kulankhula kwa mzimu ndi koyenera komanso, kwangwiro, tiyenera kukweza maso athu pa Yesu pamene tikutchera khutu lathu kuchimene mzimu akufuna kutilankhula. Chithunzi chomwe chili pansi apa chithandiza pofuna kuyesa kuyenda kwa mzimu kotere kuti ukhale ndi chitsimikizo kuti kukuchokera kwa Mulungu.

Popeza kulankhula kwa Mulungu nthawi zonse kumabwera modzidzimutsa, nkoyenera kuti kuziyesedwa. Poyamba tiyenera kukayesa pogwiritsa ntchito malembo opatulika. Tiyenera kuyesa chiyambi chake chenicheni, uthenga wake, pamodzi ndi chipatso chake chinthuzi chotsara ichi chikuthandiza poyesa ganizo lotero kuti ukhale ndi chitsimikizo kuti ukumvetsera kwa Mulungu.



| IWEYO | SATANA | MULUNGU |
|---|---|---|
| | Upeze chiyambi chake (kuyesa mzimu 1 Yhane 4:1) | |
| - Kuyamba kulingalira mawu a Mulungu mozama<br>- Kuzama mu maganizo | ganizo lofika modzidzimutsa. Kodi padali kalikonse mmaganizo ako? Kodi ganizolo likuonetsa lowononga? | Lochokera mkati mwa moyo kenako kulengako mmutu Kodi maganizo ako adali pa Yesu |
| | Kosanthula uyese mawu fundo zake 1 Yohane 4:5) | |
| Kulingalira zinthu zimene ndaphunzira | zosakhala bwino, zoononga zotsutsana ndi chikhakidwe cha Mulungu, zotsutsana ndi mawu. Ganizo lokanidwa kuyesedwa | omangirira, otonthoza, ganizo lovomera kuyesedwa |
| | Kuonanso chipatso (uyese chipatso chako Mateyu 7:15-16) | |
| Zofunikira | Mantha, ukapolo, chisokonezo, kukhumudwa | Kupatsa moyo kuchikhulupiriro kubweretsa mtendere, chipatso chabwino, chidziwitsa |

Chipatso cha moyo wamkati chiyenera kukhala chodzadza ndi chikondi, chiyanjanitso, machilitso, komanso umphumphu.

Mavumbulutso onse operekedwa kwa iwe ayenera kuperekedwa ku thupi la Yesu Khristu makamaka kwa woyang'anira mu uzimu (mtsogoleri wako) kuti akutsimikizire ngati zili zoona kapena ayi. Ichi ndi chitetezo chimene Mulungu adatipatsa. Mtsogoleri wathu

masomphenya. Iye adachita chimenecho kuchokera ku Genesis mpaka ku chibvumbulutso kulankhula popeza mzimu woyera adaperekedwa pa machitidwe 2. Tiyenera kuyembekezera kulandira maloto pamodzi ndi masomphenya (Machitidwe 2:1-4). Yesu amene ali chitsanzo chathu changwiro adaonetsera mphamvu iyi pokhala mu chiyanjano ndi Atate (Mzimu). Iye adalankhula kuti sadali kuchita kanthu mwayekha koma zonse zimene amaona Atate komanso akulankhula (Yohane 5:19, 20, 30). Moyo wodabwitsa wotani kuukhala!

Kodi nkotheka kwa ife kukhala moyo wa uzimu monga Yesu amakhalira? Ndikukhulupirirra choncho. Cholinga chenicheni cha imfa ya Yesu pamodzi ndi mdzukiro wake chidali choti nsalu ya chophimba idang'ambika kuchokera pamwamba mpaka pansi ndipo tsopano tonse tili ndi mwayi wofika pamaso pa Mulungu ndipo tili okakamizidwa kutero (Aheberi 10:10-22). Mwa ichi ngakhale kuti zimene ndikufotokoza zikuoneka zodabwitsa kwa akhristu m'mado uno, zili zooketseredwa pamodzi ndi kufotokoza monga ngati chiphunzitso choona cha mu baibulo. Ndi nthawi yobwezeretsa ku mpingo zonse zimene zili za mpingo wa Mulungu.

Ena, chifukwa chikhalitsa muchipembedzo cha miyambo adzisowa chithandizo cha kumvetsa choonadi ichi asadayambe kugwiritsa ntchito. Adzapeza nthandizo ili mu buku lotchedwa kulankhulana ndi Mulungu" lolemedwa ndi - Mark Virkler.

FUNGULO LA CHINAYI - KULEMBERA MAPEMPHERO PAMODZI NDI MAYANKHO A MULUNGU KUMABWERETSA UFULU WA KUMVA KWA KULANKHULA KWA MULUNGU

Mulungu adamuuza Habakuku "lembera masomphenya nuwachenutsa pa magome....." (Habakuku 2:2). zidali zisadachitikepo kwa ine kulembera pemphero pamodzi ndi mayankho a Mulungu monga Habakuku adachitira. Adali Mulungu amene adamulamulira. Ngati ungayambe kusanthula malembo opatulika mapeto ake uona machaputala mazanamazana



owonetsera ichi kuyambira pa (Masalimo aneneri ambiri komanso buku la chivumbulutso. Nchifukwa chiyani sindidali kuganizira ichi ndi kale lonse? Chifukwa chiyani sindidambepo ndi uthenga umodzi wokha wolalikira za ichi?

Ndidaganiza zoyamba kulembera ndipo ndidayamba kuchita kafukufuku wa ichi Ndidapeza kuti izi zabisika mu kuzindikira kuyenda kwa Mulungu chifukwa choti ndidayamba kulemba mwa chikhulupiriro pa nthawi yaitali chifukwa choti adali Mulungu amene amatsogolera. Sindidakhale ndi nthawi yoyesanso pamene ndidali kulandira ichi chifukwa ndimazindikira kuti pamene kuyenda kwa Mulungu kwatsilizika ndikhala ndi nthawi ya kuyesa izo mwa tchutchutchu pa nthawi imeneyo kuonetsetsa kuti zikugwirizana ndi malembo opatulika.

Ukhoza kukhala wodala pamene ukuyeserakulembera. Chikaikiro chikhoza kukuletsa iwe poyamba koma uyenera kukana ndipo uzilimbikitse wekha kuti izo ukuchita zikugwirizana ndi malembo opatulika komanso kuti Mulungu akulankhula kwa ana ake. Usadzitengere mokaikitsa. Uzitenge mwa chifatso. Pamene wazitenga wekha mokayikitsa umachita mosemphana ndi mzimu woyera. Ndipokhapokha pamene tapumula kuti ntchito zanthu zolemetsa kulowa mu mpumulo wake pamene Mulungu amakhala womasuka kuyenda mwa ife (Aheberi 4:10). Mwa ichi uyenera kumwetulira pa nkhope yako, kukhala womasuka kutenga cholembera chako pamodzi ndi pepala yako ndipo kenako ulowe mukupembedza ndi kulambira ndi kufunafuna nkhope ya Mulungu . Pamene ukulemba funso lako kwa Mulungu utakhala motakasuka ndi motonthola (chete apa kuti utakweza maso pa Yesu amene ali pomwepo ndi iwe ndipo pa nthawi yotere udzatha kumva yankho loperekedwa kwa iwe. Usalikaikire konse koma ungolemba basi. Kenako udzakhale ndi nthawi yoonanso ndipo udzaona kuti uli pamaso pa Mulungu.

Zolemba zomaliza. Aliyense aseyerekeze izi amene sadwerenge mokwanira chipangano chatsopano chonse. Poonjezera apo, munthu ayenera kudzipereka kwa munthu amene ali Tate wao mu uzimu.

Pamene ndakweza maso anga pa Yesu (Aheberi 12:2) kukhala chete pamaso pake pamodzi ndi kugawana ndi Iye zomwe zili pa mtima panga ndimadzaona kuti kukambilana kumayamba kuchitika. Maganizo amayamba kubwera ku mpando wachifumu wa Mulungu ndipo kenako ndimaona kuti ndilikulankhulana ndi mfumu ya mafumu.

Nkofunika kwambiri kuti munthu azikhala chete ndi kupenyerera kwa Mulungu ngati akufuna kulandira mawu a Mulungu. Ngati sangakhale chete, adzingolandira maganizo ake basi. Ngati sapenyetsetsa pa Yesu mwa tchutchutchu akhoza kulandira uthenga wabodza chifukwa sadakweze maso ake pa Yesu.

Mwa ichi ngati ukweza maso ako pa Yesu, maganizo onse amakhalaochokera kwa Yesu. Ngati wakweza maso ako pa zokhumba zako za mtima wako, zotsatira zake umalandira maganizo ochokera mu mtima mwako. Kuti ulandire mawu angwiro, poyamba uyenera kuzitontholetsa wekha kukhala chete chachiwiri ukweze maso ako kwa Yesu.

Ndilankhulanso motere kuti, izi zimachitika mosavuta polambira mfumu yamafumu komanso kulandira mawu abwino.

FUNGULO LACHITATU - PAMENE NDIKUPEMPHERA NDIMAKWEZA MASO ANGA A MTIMA MWANGA PA YESU, KUMAPENYA MU UZIMU WA MALOTO NDI MASOMPHENYA A MULUNGU WAMPHAMVU YONSE.

Taona kale fundo iyi mu ndime zina kale. Apa tikungofuna kuzamitsa pa fundoyo. Habakuku adalankhula motere, "ndidzayang'ana ndione..." Ndipo Mulungu adati, "Lembera masomphenyawo....Habakuku 2:1-2". Ndi chinthu chosangalatsa kuti Habakuku adali kudikira kuti aone masomphenya pamene adali kupemphera. Iye adali kutsegula maso amtima wake ndi kuyang'ana mu dziko la uzimu kuti aone zimene Mulungu amafuna kuti amounetse iye. Ili ndi ganizo lodala kwambiri.



Ndidali ndisadatsegulepo maso anga a mtima wanga ndi kupenyerera masomphenya. Koma pamene ndidali kulingalira mozama, ndidazindikira kuti ndi zimene Mulungu amafuna kuti ndichite. Iye adandipatsa maso mu mtima mwanga. Sali oti azigwiritsa ntchito potsilira kapena kuonera zinthu zolephereka. iwo amagwiritsidwa ntchito kuonera zinthu za dziko lauzimu komanso kuyenda kwa Mulungu.

Mwa maphunziro ndikukhulupira kuti pali mzimu wa machitachita kugwira nchito ndi ine. Uli ndi angelo, ziwanda, mzimu woyera mphamvu ya Mulungu ndi zina zotero. Palibe chifukwa kwa ine choti ndisaone izi ngakhale kuti anthu chipembedzo amandiuza kuti ndisamakhulupirire zoterozo.

Chinthu chofunika komanso chodziwika bwino ndi choti tiyenera kuona kuti tipenyerere. Danieli adali kuona masomphenya mu mtima mwake ndipo adalankhula motere, "anaona...ndinapenyerera....ndinaona..... Danieli 7:1), 9, 13). Tsopano pamene ndikupemphera ndimafunafuna Yesu kukhala pamodzi ndi ine ndipo ndimamupenyerera Iye akulankhula kwa Ine kuchita pamodzi ndi kulankhula zinthu zimene zili pa mtima pake. Akhristu ambiri akhoza kuziona izi ngati iwo atangokhala ndi kuyang'ana - akhoza kuonanso chimodzimodzi. Yesu ali Emmanueli - Mulungu ali nafe. Zili zophweka chomwecho. Udzatha kuona masomphenya a mtima wako chimodzimodzi monga umo umalandirira maganizo. Ukhoza kuona Yesu ali pamodzi ndi iwe chifukwa choti Yesu amakhala ndi iwe nthawi zonse motere. Ukhoza kuona kuti masomphenya otere amafika mosavuta kotero kuti ukhoza nthawi zina kuwakana kuganiza kuti ndi maganizo chabe....(Kukaikira ndi mzimu wa satana wochita khondo ndi mpingo wa Mulungu) Koma ngati upitirizabe kulembera masomphenya otere, kukaikira konse kudzagonjetsedwa ndi chikhulupiriro pamene tsopano ukhala ndi chidziwitso kuti izi zonse zabadwa kuchokera wa Mulungu.

Mulungu adapitiriza kudzivumbulutsa yekha kwa anthu amene adachita nawo pangano pogwiritsa ntchito maloto pamodzi ndi

iwenso pamene ukufunafuna Mulungu pogwiritsa ntchito mafungulo anayi awa. Awa akupezeka pa Habakuku 2:1-2. Ndikukupempha kuti uwerenge apa usadapitirire.

FUNGULO LOYAMBA - MAWU A MULUGU MU MTIMA YATHU AMAKHALA NGATI MAGANIZO MWA ICHI NDIMAKHALA TCHERU KWA MULUNGU

Baibulo limafotokoza motere "ndipo Yehova anandiyankha nati....." (Habakuku 2:2). Habakuku amazindikira kulankhula kwa Mulungu. Baibulo limafotokoza kulankhula kwa Mulungu ngati mawu a kachetechete". Nthawi zonse ndimamvetsera kulankhula kwa mkati ndipo ndi zoonadi Mulungu amalankhula mu njira yotere. Koma ndaona kuti ambiri a ife, nthawi zambiri kulankhula kwa Mulungu kumadza kwa ife ngati maganizo, masomphenya kumverera. Mwa chitsanzo palibe aliyense wa ife wakhala akuyenda ndipo mwa dzidzidzi ganizo kufika kuti umupempherere munthu wina wake? Timazindikira kuti uko ndi kulankhula kwa Mulungu kulankhula kwa ife kuti tidzipempherera anthu aliyense pa yekha. Funso langa kwa iwe ndi lotere....."Kodi kulankhula kwa Mulungu kumaveka motani pamene udali kuyendetsa galimoto lako?" Kodi kudali kochitika mkati mawu omveka kapena lidali ganizo lowe lidafika mmutu mwako? Anthu ambiri amanena kuti kulankhula kwa Mulungu kudawafikira mwa ganizo.

Tsono ndidaganiza kwa ine...ndekha.....mwina mwake pamene ndimamvetsera ku kulankhula kwa Mulungu chomwe ndidayenera kumvetsera kudali kuyenda kwa maganizo. Mwina mwake m'gwirizano wa mu uzimu umachitika kupyolera mu kuyesa komanso zolankhula za anthu zikwizikwi tsopano ndili wokhazikika mtima kuti izi zili choncho basi.

Baibulo likuchitira umboni ichi mu njira zambiri. Thanthauzo la "paga" mawu a chiheberi kutanthauza "kupembedzera" ndi loyenera. Pamene Mulungu waika anthu pa mtima pathu kuti tiwapembedzere, lye amachita ichi kupyolera mwa "paga" - ganizo lofika mwadzidzidzi.



Mwa ichi pamene ndakhala cheru kwa Mulungu, ndimakhala ndili tcheru kumaganizo za uzimu. Ngati ndili mu pemphero pamaso pa Mulungu ndi mapeza kuti kuyenda kwa maganizo kumabwera kwa ine kumachokera kwa Mulungu.

FUNGULO LACHIWIRI-NDIYENERA KUPHUNZIRA KUTONTHOLETSA MAGANIZO ANGA, NDI MACHITACHITA ANGA, KUTI NDIKATHE KUONA KUYENDA KWA MAGANIZO A MULUNGU NDI MACHITACHITA AKE MWA INE

Haakuku adalankhula motere "Ndidzaima pa dindiro langa ndi kudziika palinga.....(Habakuku 2:1). Habakuku adazindikira kuti iye amve kulankhula kwa Mulungu kwa kachete chete ngati maganizo adayenera poyamba kupita pa malo ayekha a chete komanso kutontholetsa maganizo ake pa Masakimo 46:10 akuti limbikitse polankhula motere. "Khalani chate ndipo dziwani kuti Ine ndine Mulungu.....".

Pali kuzindikira kozama kozindikira kuyenda kwa mzimu mu mzimu wathu aliyense wa ife pamene tikutholetsa matupi athu pamodzi ndi machitachita athu pamaso pa Mulungu.

Ndapeza njira zambiri zophweka zakuzitontholetsa ndekha ndi cholinga kuti ndikhoza kuona ulemelero wa Mulungu komanso kuona kuyenda kwa mzimu wake mwa ine. Kukunda Mulungu kopyolera mu kupembedza mu nyimbo mwa kachetechete ndi njira yamphamvu kwa anthu ambiri. (Onani pa II Mafumu 3:15 ndi pamene ndakhala chete-mototholetsa thupi langa ndi kuima pamaso pa Mulungu pamene ndimatha kuona kuyenda kwa maganizo a Mulungu mwa ine. Mwa ichi, ndikatha kupembedza mwa kachetechete motontholetsa thupi langa, ndimazitsegula ndekha kuti maganizo a Mulungu ayende mwa ine. Ngati maganizo afika kwa ine azinthu ndaiwala kuchita, ndimawalemba ndiponso kukambilana ndi anzanga. Ngati maganizo a kutsutsika afika mu maganizo anga, ndimawalapa nthawi yomweyo mwa tchutchutchu ndi kulandira chiyeretso mu mwazi wa mwanawankhosa ndi kuvala chovala chake cha chilungamo kuoneka pamaso pa Mulungu wopanda chilema.

Chaputala chachisanu

## KUDZADZA SENSI YOYAMBA YA MZIMU WA MUNTHU PAKUMVA KULANKHULA KWA MULUNGU

Mawu oyambirira-

Mphamvu ya kulenga mwa mzimu imayamba komanso kutha kudzera mu mphamvu ya kuyenda ya Mulungu. Mulungu amakhazikitsa chikhulupiriro cha mu mtima potumiza mzimu wake woyera kuti ulankhule mu mitima yathu ndipo keneko Mulungu amabweretsa mawu ake olankhulidwa kupyolera mwa mzimu. Mwa ichi titha kuona kuti mphamvu ya kulenga komanso kutheka mwa Mulungu yemweyo komade pali njira zambiri mmenene ife tikhoza kutenga mbali. Choyambirira mwa zonse ndi choti tiyenera kukhala otothola pamodzi ndi kumvetsera monga takamba kale mu chaputala choyamba. Pamene tikumvetsera mawu ake, timafungatira mawu ake mu mitima yathu ndi kudikira pa Iye kuti akwanilitse.

Mu chaputala ichi, tidzakhala tikuona umo tingamasulire mphamvu ya kulenga mwa mzimu kuonanso ntchito ya Mulungu komanso zimene munthu angachite ndi cholinga kuti aliyense wa ife akhoza kuchitira limodzi ndi Mulungu mu miyoyo yathu komanso mu dziko lapansi mmene tili.

| | SENSI | KAGWIRITSIDWE NTCHITO UMO IMFA | CHITSANZO CHA M'BAIBOLO | SITEJI |
|---|---|---|---|---|
| 1. | MAKUTU AMKATI KHUTU LA MKATI | KULANDIRA MAWU A MULUNGU | GENESIS 12:1-3 | KATENGA PAKATI |
| 2. | MASO A MKATI 2 CHIVU LUTSO 4:1 | KULANDIRA MASO MPHENYA A MULUNGU | GENESIS 15:5-6 | |
| 3. | MALINGALIRO AMKATI LUKA 2:19 | KULINGALI MAGANIZO A MULUNGU | AROMA 4:20-21 | KUFUNGATIRA |
| | CHIFUNIRO CHA MKATI MACHITIDWE 19:21 | KULANKHULA MAWU AMULUGU | GENESIS 17:5 | |
| ZOTSATIRA ZAKE | | KUFA KWA MASOPHENYA | GENESIS 16:2 GENESIS 17:18-19 | KUBADWA |
| | | KUUKA KWA MASO MPHENYA | GENESIS 21:1-2 AGALATIYA 4:4 | |



ABRAHAMU - CHITSANZO

Abrahamu ndi chitsanzo cha munthu amene amakhulupirira ndipo chikhulupiriro chake chidali cholenga - chomangidwa pa mawu olankhulidwa a Mulungu mu mtima mwake. Chikhulupiriro cha Abrahamu chidamasula mphamvu ya kulenga ya Mulungu mu moyo wake ndipo chikhulupiriro ichi chafalikira ku mibado ndi mibado. Chikhulupiriro ichi mwa Abrahamu chidayamba pamene Mulungu adayamba kulankhula nayemu mtima mwake. Lembera pamalo osalembedwa pa mawu amene Mulugu adalankhula kwa Abrahamu ulembe mau apa Genesis 12:1-3

## IWENSO UKHOZA KUMVA KULANKHULA KWA MULUNGU

M'bado uno mmene tikukhala uli wolumikizana kotheratu ndi kusankhulupirirana kotero kuti zimapangitsa anthu kuseka pamene tikumva wina akulankhula kuti amatha kumva kulankhula kwa Mulungu. Apa sitiseka pa zifukwa zambiri. Poyamba azibambo ndi azimayi lero lino amene amaonetsera kuti amamva kulankhula kwa Mulungu. Pomaliza, pali njala mu mitima yathu yofuna kukhala pa chiyanjano ndi Mulungu komanso kumva kulankhula kwake mu mitima yathu. Ndidalimba nako pa zaka zambiri monga ndili wokhulupirira Baibulo wobadwa mwatsopano kuyesetsa kumva kulankhula kwa Mulungu koma osankhoza kutero. Ndidapemphera, kusala kudya, kusanthula mkati mwanga koma palibe kalikonse ndidapindulapo. Palibe kulankhula mkati mwanga koma palibe kalikonse ndidapindulapo, padalibe kulankhula kwina kulikonse kwa mkati mwanga komwe ndidakumva! kenako Mulungu adandipatsa chaka china chimodzi kusanthula kuwerenga pamodzi ndi kuyesera, kumvetsera ku kulankhula kwa Mulungu. Mu nthawi imeneyo, Mulungu adandiphunzitsa ine mafunguro anayi omwe adatsegula khomo. Ku njira ziwiri za pemphero. Ndapeza kuti sikuti zimangothandiza ine komanso zagwira ntchito kwa zikwi za akhristu omwe ndawaphunzitsa. Pafupifupi 99% ya anthu amene ndawaphunzitsa akhala tsopano akukhala pa chiyanjano ndi Mulungu komanso miyoyo yao yakhala ikusintha. Izi zikhoza kuchitika kwa

. Pamene ndalephera, ndimazindikira kuti sindinachite izi mothandizana ndi Iye wokhala mwa ine

. Ndimachita zinthu osati ndi mphamvu zanga

KUYENDA KWA MPHAMVU YA MZIMU

. Ndimakhala tcheru kuyenda kwa mzimu

. Ndimazindikira kwa mzimu woyera pamene ukuyenda mwa ine (Yohane 7:37-39)

. Ndimafunitsitsa kukhala mwa mzimu woyenda mwa ine

. Sindiona bwino kukhala mwa chilamulo opanda mzimu

. Ndimakhala womasuka

. Ndimatha kuona mphamvu pamene mzimu ukuyenda mwa ine

. Ndimakhala ndikouna mphamvu ya kulenga ikuyenda mwa ine

. Ndimakhala womasuka pamene ndikugwira ntchito ndipo pakutero ndimalowa mu uzimu

. Ndimazitontholetsa ndekha kuti mzimu uyende mwa ine

. Pamene mzimu ukuyenda mwa ine, ndimakhalabe momasuka kufikira zonse ndimachita zitatha

. Sindiyamba kugwira ntchito kufikira nditayamba kuona kuyenda kwa mzimu

. Ndimayamba kuchita zinthu pamene ndaona mzimu akuyenda mwa ine



. Pamene ndikudzizoloweretsa kukhala mwa mzimu, ndimaona mphamvuyo ikuchulukirabe kugwira ntchito mu moyo wanga

. Ndimazindikira kuti zinthu zonse zimachokera mukudzodza kwa mzimu

PEMPHERO LOTSEKA:

Ambuye lolani kuti kulingalira kwanga pa mawu a Mulungu ikhale njira ya moyo wanga.

CHIGAWO CHOYAMBA

- KUKHALA NDI PAKATI

SITEJI YOYAMBA - KUTENGA PAKATI



...."Mzimu woyera udzafika pa iwe ndimphamvu ya wamkurukuku idzakumphimba iwe.....ndipo udzakhala ndi pakati.....
(Luka 1:35, 31)

. Maganizo ali ngati kalirole kuonetseratu zinthu zonse za dziko la thupi ndi la uzimu popanda chosokonezeka.

MUKHALA MODZIMASULA

. Zofuna pamodzi ndi zokhumba zanga sizinditsogolera ine

. Sindikhala wokakala mwa ine mwini ngakhale ndili ndi zinthu zina zosakonzeka pa moyo wanga

. Sindiona ngati kuti ndiyenera kuchita zinthu mothamanga

. Ndikhoza kulolera zinthu zimene zomwe sizingachitike kapena kumveka bwino

. Ndimaika zinthu zofunikira pa dongosolo lake

. Ndimakhala wopirira

. Pamene ndagwira ntchito kwambiri, ndimakhoza kupumula

. Sindikhoza kudandaula za mauto a dzulo kapena mmawa

. Ndimaona kuti ndikhoza kuvomereza pamodzi ndi kulandira mavuto anga mwanzeru

. Sindiona kuti chili chonse chidzichitika nthawi imodzi

. Ndimaona kuti zinthu sizili zoipa ngakhale kuti sizigwirizana ndi momwe ndimafunira

. Sindilimbana ndi zinthu zimene ndikudziwa kuti nkovuta komanso nkosatheka kukhala nazo

. Sindiona kuti ndiyenera kuvomereza zili zonse zomwe munthu anganene



KUKHALA OMASUKA KULANDIRA

. Ndikudziwa Mulungu akugwira ntchito mwa ine

. Ndimadalira pa mzimu woyera

. Ndimazindikira mphamvu ya mzimu woyera

. Sindiyamba ntchito podalira mphamvu zangazanga

. Ndimapemphera pemphero pamene pali pofunika

. Ndimadzitenga ndekha munthu amene mkati mwanga muli wina

. Ndimazindikira kuti mphamvu zimachokera kwa Mulungu

. Ndimazindikira kuti nzeru zanga zichokera kwa Mulungu

. Ndimazindikira kuti Mulungu ndi podalira panga

. Ndimazitenga ngati muthu amene mwa ine wina amakhalamo

. Ndimazindikira kuti sindigathe kuchita kanthu mwa ine ndekha

. Ndimazindikira kuti chilungamo changa ndi chochokera mwa Khristu Yesu

. Ndimazitenga ndekha monga wovekedwa ndi chilungamo cha Khristu

. Ndimaona ndekha ngati munthu wodzadzidwa ndiwina mkati mwanga

. Pamene ndagonjetsa, ndimazindikira ndi chigonjetso cha Khristu

. Sindimva kupanikizika kapena kutentha komanso kuchita thukuta

. Sindiona kufunika kokasamba pamene palibechochitika mu thupi mwanga

Ndimakhala womasuka zedi

. Mkamwa mwanga simukhala mouma

. Ndimakhala mmaso osati wotopa

. Sindimva kuwawa kwa mutu

. Sindiona kulemera thupi langa

. Mapewa, khosi pamodzi ndi msana wanga sizikhala zomangika

. Thupi langa silikhala la matenda

. Maso anga sakhala odzadzidwa ndi misozi

. Mmimba mwanga mumakhala mwa bata

. Chilakolako changa pa chakudya chimakhala chabwino

KUKHALATCHERU

. Maganizo anga sakhala omwazika

. Sindikhala ndi vuto kukumbukira zomwe ndikuchita

. Ndimakhala mmaso mu zonse

. Pamene ndasokonezeka sikukhala kovuta kuti ndibwerere mwakale



. Maganizo anga amakhala omasuka

. Ndimakhala wokhazikika

. Sindikhala opanda choganiza mutu mwanga

. Zolinga zanga zimakhala zozindikiritsa

. Ndimachita chinthu chimodzi pa nthawi yake

. Ndimakhazikika pa zimene ndikuchita

. Maganizo anga sasokonezeka konse ayi

. Sindilola zosokoneza ine

. Maganizo anga amakhala pa zimene ndikuchita

. Ngakhale zinthu zioneke ngati zosokonekera, ndimagwira ntchito mwa mtendere ndi dongosolo

. Ndimakhala womizidwa ndi ntchito

. Maganizo anga sakhala omwazikana

. Ndimatha kusunga maganizo anga kuti ndigwirizane ndi zimene ndikufuna

. Sindikhala ndi maganizo ogawika

. Ndimakhala nthawi zonse pa chimene ndidalingalira kuti ndichita

. Ndimamaliza kaye ntchito imodzi ndisadayambe yina

. Ndimakhala nthawi zonse mu zochitika za pa nthawiyo

Kulingalira mawu ndi chinthu chimene baibulo limatilamulira kuti tizichita mwa ichi fungilo lilonse pa lokha mwa asanu awa lili lofunikira kuti kulingalira kwathu kukhale kopindula zedi ku moyo wathu wa uzimu. Ganizirani izi zili pansi apa pamodzi ndi ine.

CHILANGIZO CHA MU BAIBULO KUKHUDZANA NDI KUTONTHOLA (MPUMULO) KWA THUPI

....."Momwecho utsalira mpumulo wa sabata wa kwa anthu a Mulungu. Pakuti iye amene adalowa mpumulo wake, adapumulaso mwini wake ku ntchito zake mangaso Mulungu ku zake zake za lye.
Chifukwa chake tichite changu cha kulowa mpumulowo kuti wina angagwe mchitsanzo chomwe cha kusamvera...." (Aheberi 4:9-11).

....."Ndipo adawalumbirira ayai kuti asalowe mpumulo wake? Siawo kodi osamverawo? ndipo tiona kuti sanakhoza kulowa chifukwa cha kusankhulupirira...." (Aheberi 3:18-19).

CHILANGIZO CHA MU BAIBULO KUKHUDZANA NDI KUKHALA WOPENYETSETSA

....."Titaye cholemetsa chirichose ndi chimoli limangotizinga ndipo tithamange mwa chipiriro makaniwo adatiikira ndi kupenyerera woyambira ndi womaliza wa chikhulupiriro chathu...." (Aheberi 12:1-2).
....."Indetu, Idetu ndinena kwa inu, sankhoza mwana kuchita kanthu payekha koma chimene aona Atate achichita ndicho. Pakuti zimene lye achita zomwezo mwananso azichita momwemo...." (Yohane 5:19-20).

CHILANGIZO CHA BAIBULO KUKHUDZANA NDI KUKHALA MODZIMASULA

....."Khalani chete ndipo dziwani kuti Ine ndine Mulungu (Masalimo 46:10)



...."Musadere nkhawa konse komatu mzonse di pemphero ndi pembedzero pamodzi ndi chiyamiko. zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu. Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana chidziwitso chonse udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Khristu Yesu....." (Afilipo 4:6-7)

CHILINGANIZO CHA MU BAIBULO KUKHUDZANA NDI KUKHALA OMASUKA KULANDIRA

...."Khalani mwa Ine ndi Ine mwa inu. Monga nthambi siingathe kubalachipatso pa yokha ngati siikhala mwa mpesa motero mulibe inunso ngati simukhala mwa ine. Ine ndine mpesa inu ndinu nthambi zake, wakukhala mwa Ine ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu....." (Yohane 15:4-5)

CHILANGIZO CHA MU BAIBULO CHOKHUDZANA NDI KUYENDA KWA MPHAMVU

.....Iye wokhulupirira Ine monga chilembo chinati mitsinje ya madzi amoyo idzayenda kuturuka mkati mwake. Koma ichi anati za mzimu woyera amene iwo akukhulupirira Iye anati adzalandira pakuti mzimu panalibe pamenepo chifukwa Yesu sanalemekezedwa pa nthawi pomwepo....." (Yohane 7:38-38).

KUTONTHOLA KWA THUPI

Mtima wanga umapuma mwabwino

- Kupuma kwanga kumakhala koyenera
- Akatumba anga sakhala omangika
- Sindioneka ngati wotopa
- Sindiona kulimbana kulikonse mkati mwanga ndikalankhula kanthu

Kukuthandiza kuti upeze mtendere wa mkati, ukhoza kulembera mayankho a Mulungu okhudzana ndi mafunso otsatirawa.

Ambuye, kodi mukufuna kulankhula kwa ine chiyani kukhudzana ndi umo ndingathetsere mkwiyo mwa ine?

Ambuye kodi mukufuna kulankhula kwa ine chiyani kukhudzana ndi umo ndingathetsere kutsutsika?

Ambuye, kodi mukufuna kulankhula kwa ine chiyani kukhudzana ndi umo ndingathetsere mantha mu moyo wanga?

Ambuye kodi mukufuna kulankhula kwa ine chiyani kukhudzana ndi umo ndi ngathetsere kusowa chitetezo?

## KULINGALIRA MAWU A MULUNGU MOGWIRIZANA NDI BAIBULO - KUKHALA MOMASUKA

Baibulo limagwiritsa ntchito mawu oti "kulingalira mawu" kufotokoza kuti kukhala mwa mzimu kuti ulandire kuchokera kwa Ambuye mavumbulutso. Munthu amene amakhala ali "kulingalira mawu" amakhala womasuka,wotonthola, wodalira pa mzimu woyera nthawi zonse. Umu ndimo munthu ayenera kukhala kuti mphamvu ya kulenga ikayende mwa iye nthawi zonse.

## KUZINDIKIRA MAFUNGURO ASANU OGWIRITSA NTCHITO MU NTHAWI YOLINGALIRA MAWU A MULUNGU

Chigawo ichi chikuthandiza kuona mafungilo asanu ogwiritsa ntchito pa kulingalira mawu a Mulungu ndipo izi zikuthandiza kuzindikira umo ungazigwiritse ntchito izi ku moyo wako.

Kulingalira mawu a Mulungu (meditation) ku mazindikirika ndi kudzikhalitsa wekha mwa bata, kukhala wotchera khutu kumasula, kukhala womasuka kulandira ndipo pomaliza kuyenda kwamphamvuyo. Zina zotsutsana ndi izi ndi kulimbana kwa thupi,



kupsyinjika, kudziletsa kavyola, kutakataka, pamodzi ndi kuganiza. Pansi apa pali chinthunzi ndipo uike x pa malo pamene ukuona kuti pakufotokoza moyo wako wonse.

Kulimbana kwa thupi — kukhala bata

0 1 2 3 4 5

Kupsyinjika — kukhala tcheru

0 1 2 3 4 5

Kudziletsa kovyola — kudzimasula wekha

0 1 2 3 4 5



Kutakataka — kukhala womasuka ku mphamvu

0 1 2 3 4 5

Kuganiza — kuyenda kwa mphamvu

0 1 2 3 4 5

Chithu chimodzi chimene ndingakambe pa nthawi ino ndi choti kwa ine, mtendere wa mkati uwu udapezedwa pamene ndidaphunzira kukhala pa chiyanjano ndi Mulungu. Ndimapita kwa Mulungu ndi zothodwetsa za mkati mwanga ndi kudzifotokoza kwa Iye ndipo Iye amalankhula ndi Ine kukhudzana za zinthuzo. Iye amandiuza umo Iye akuonera zinthuzo ndi umo Iye akufunira kuti ndichitire ndikukhulupirira mu mphamvu yake yachigonjetso kupirira pamene Iye akundigwirira ntchito. Ndimaona kuti ndikatha kulandira pamodzi ndi kulembera mawu awa ndi kukonza maganizo anga pamodzi ndi mtima wanga mogwirizana ndi malangizo ake, mtendere umayamba kuyenda mwa ine - ndipo kenako mphamvu ya kulenga. Mwa ichi, sindingathe kulankhula mwa tchutchutchu komanso motsindika kufunikira kophunzira kukhala pa chiyanjano ndi Mulungu komanso kuchichita. Ndalemba mabuku awiri a malangizo kukhudzana ndi ichi. Limodzi likutchedwa - Chiyanjano ndi Mulungu ndipo lotsatira likutchedwa...."Kulankhulana ndi Mulungu.....". Onse kapena limodzi mwa ilo lili lofunika munthu kuphunzira luntha. Ndifotokoza mwa chidule umo munthu amalandirira kulankhula kwa Ambuye pamodzi ndi masomphenya a Mulungu muma chaputala awiri itsatirawo. Tilinso ndi zolembera (mmene ukhoza kulembera zolankhula zako ndi Mulungu. Zonse izi zikhoza kugulidwa potsata ndondomeko yomwe ili kumapeto kwa bukuli.

ZINTHU ZINA ZOYENERA KUCHITA KUTI UPEZE MTENDERE WA MU MTIMA

1. Pemphera kuti uone umo Mulungu akufunira kuti ukhalira pa zinthu zimene zikukuchotsera mtendere upemphe Iye zimene akufuna kutiuchite kukhudzana ndi vutolo. Lemba funso lako pamodzi ndi yankho lako pa pepala. Monga kulankhula kwake nthawi zose kumabwera ngati mwa maganizo mwa ichi tchera khutu lako lauzimu. Udzimouna Iye ali nawe pamodzi pamene uku pemphera. Iye ali ndi iwe.



2. Yenda mwa mzimu nthawi zonse. Werenga pamodzi ndi kuchita zonse pamaso pa Mulugu. Buku la m'bale Lawrence lotchedwa "kuchita pamaso pa ulemelero wa Mulungu" ndi lofunika kuwerega komanso lothandiza mu madera otere. Udziona ngati kuti Yesu ukukhala naye pomwepo mulambire mwa kachetechete komanso kukhala naye mu chiyanjano tsiku lonse.

3. Udzikhala nthawi yaitali uli pamaso pake pa Mulungu ukukandira kuchokera kwa Iye mavumbulutso ndipo uzichita zimene akuvumbulutsira.

4. Kumbukira kuti "mtima wa chisangalalo uli ngati mankhwala". Khala wosangalalanthawi zonse. Usakhale wokakala. Gwira ntchito mu uzimu wa chimwemwe.

5. Ukhale pa chinthu chimodzi pa nthawi yake.

6. Gwiritsa ntchito zinthu zokukhalitsa moyo womasuka.

7. Lingalira mozama (zitanthauzo kugwiritsa ntchito mbali ya manja ya bogo lako kumene chidzodzo chimachokera). Ukhale wodzipereka ku chidzodzocho.

8. Udzipereke moyo wako chifukwa cha mzako potaya moyo wako udzaupeza.

ZINTHU ZINAYI ZIMACHOTSA MTENDERE WA MU MTIMA

Pali zinthu zinayi zimene zimachitika kuchotsa mtendere mmoyo wa munthu izi ndi mkwiyo, kutsutsika, mantha, pamodzi ndi kusowa chitetezo. palibe cholakwika pozindikira izi koma nkoyenera kuti tizindikire msangamsaga pa maso pa Mulungu kuti tikakhoze kukhala ndi mphamvu ya kulenga mu moyo mwathu.

ZOYENERA KUCHITA
(Chidziwitso kwa wophunzitsa ndi choti zina mwa izi ziyenera kuchitika pa kalasi)

Tsopano utenge zochitika zina zomwe uku komana nazo padakali pano ndipo uyende mu sitenji yomweyo koma tsopano mosamalitsa ukulemba kuyambira sitepe yoyamba mpaka ya chisanu. Uone moyo wodzadza pamodzi ndi mphamvu yakulenga zomwe zikuberekedwa pamene ndondomeko iyi ikulemberedwa.

Zochitika, nkhani kapena ganizo lidali.....

1. "Ambuye, Kodi mukufuna kulankhula ndi ine chiyani kukhudzana ndi zochitikazi?"
2. "ambuye, Ndiloleni ndione zochitika monga inu muonera
3. Lingalira mozama kulankhula kwa Mulungu pamodzi ndi masomphenya a Mulungu wamphamvu yonse
4. Afunse Ambuye Mulungu umo lye akufunira iwe kuti ulankhule icho. Lembera zimene iye akulankhula ndipo uyambe kulankhula pamene lye akukufunsa iwe.
5. Funsa Mulungu ngati pali china chake chapadera choti uchite. Lembera ichi ndipo uyambe kuchita monga lye akukutsogolera.
6. Lembera zimene Mulungu akubereketsa kupyolera mwa iwe

PEMPHERO LOTSEKA:

Zikomo Ambuye pondipanga ine kuzindikira zonse izi zokhudza kulinga kupyolera mu mzimu wanga.

Chaputala 4

CHIKONZERO CHA KULANDIRA MAGANIZO A KULENGA A MULUNGU

....."Khalani chete ndipo dziwani....." (Masalimo 46:10)
...."Moyo wanga ukhalire chete Mulungu yekha pakuti chiyembekezo changa chifuma kwa iye....." (Masalimo 62:5). Palibe kenakalikonse kamene kangalamule mphamvu ya kulenga ya mzimu wa munthu kapena mzimu woyera mkati wa mzimu



wa Munthu koposa kotonthola kwa mkatikati kwa maganizo pamodzi ndi ntima wa munthu pamaso pa Mulungu. Monga momwe kupanikizika kwa mwa munthu kumadukiza mphamvu za kulenga kuti zigwire ntchito chowecho mtendere wa mkati umamasula mphamvuyo.

....."Mtendere wanga ndikupatsani....."akutero Amuye. Monga a Khristu tiyenera kukhala ndi mtendere ndi kukhala mu mtenderewo. Kupyolera mu ichi, tidzakhala ndi mwayi wakumasula mphamvu ya kulenga ya Mulungu kuti iyende mwa ife mu mitima yathu kopanda ichi, sitingakhale nayo.

Mulungu wakhazikitsa munthu kuti akhozakugwira ntchito iliyonse pamene akukhala mu mtendere wa Mulungu. Pamene talekerera a nunkhadala kumbali ya manja ya bongo amatsegukira kulola mwazi wa mbiri kuchotsa umunthu wako. Kuyenda kwa mphamvu ya mzimu kumakhala cha mbali ya kumanja ya bongo lako. Mtendere ndi chipatso cha mzimu woyera chimene chimavalidwa pamene tikukhala pamodzi ndi kuyanjana ndi Mulungu. Mulungu amadzadzanso ife ndi chikhulupiriro, chiyembekezo, pamodzi ndi chikondi ndipo akutilamulira ife kukhala mu zinthu zimene zili zachikondano, zolungama, zoyenera, za mtendere, za mbiri yabwino. Pamene tikukhala mu zotere, apa ndiye kuti tikuchita bwino bwino ndipo mlengi wathu amalandira ulemelero, ndipo mphamvu yake ya kulenga imayenda mwa ife mosavuta.

Pamwamba pa zonse, tiyenera kuphunzira kukhala mu mtendere ndi Mulungu umene uposa chidziwitso chonse. Zotsamwitsa za mkati zimene zimatsekereza mtendere zili monga mkwiyo, kutsutsika, mantha,kusowa chitetezo. Chilichonse pa chokha mwa izi chafotokozedwa mozama mu buku lotchedwa "Kupangiridwa uphungu ndi ulungu" Lolembedwa ndi Mark Virkler, mwa ichi sitikhoza kufotokoza mwa tchutchutchu umo munthu angachilitsidwe ku izo - pa nthawi ino. Yemwe akufuna akhoza kuitanitsa bukulo mogula osati ulele.

KULENGA IMFA PODZADZA MASENSEZI ASANU ONSE A MZIMU WAKO NDI SATANA

1. Umakhala ndi lingaliro lomwe siukadachita konse ayi.
2. Umakhala ndi chinthunzi cha iwe yekha ukuleohera
3. Umayamba kulingalira maganizo otere pamodzi ndi zinthunzi izi
4. Uyamba kuzilankhula
5. Umayamba kuchita kukana mwayi uja

KULENGA MOYO PODZADZA MASENSEZI ASANU ONSE MZIMU WAKO NDI MULUNGU

1. Pamene ukupemphera zinthu zina zake, Mulungu amalankhula kuti iye ali nawe pamodzi ndipo adzakupatsa mphatso zonse zofunikira kuti upambane mu zonsezo.
2. Mulungu amakupatsa masomphenya a moyo wake mwa iwe pamene ukuyenda mwatsopano.
3. Umalingalira mozama malingaliro pamodzi ndi zinthuzi zotero
4. Umayamba tsopano kuzilankhula ndi pakamwa pako
5. Umayamba kuchita molimba mtima kuchita zimenezo

KUFOTOKOZA MWACHIDULE ZA CHIKHULUPIRIRO CHA MMALEMBA

1. THANTHAUZO LA CHIKHULUPIRIRO

...."Chikhulupiriro ndicho chikhazikitso cha zinthu zoyembekezeka, chiyeseri cha zinthu zosapenyeka...." (Aheberi 11:1)
.....Ndi chikhulupiriro tizindikira kuti zinthu zopenyeka zina pngidwa zochokera mwa zoonekazo...." (Aheberi 11:3)

2. KUKHALA NDI PAKATI PA CHIKHULUPIRIRO

....."Chikhulupiriro chidza ndi mbiri ndi mbiri idza mwa mawu a Khristu....."



3. KUFUNIKIRA KWA CHIKHULUPIRIRO

....."Wopanda chikhulupiriro sikutheka kumukondweretsa Mulungu pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo ndi kuti ali wobwezera mphoto iwo akumfuna Iye..." (Aheberi :6)
....."chinthu chilichonse chosaturuka mchikhulupiriro ndicho uchimo ....." (Aroma 14:23)

CHIKHULUPIRIRO CHOONETSEDWA

Abraham - "Iye pokhala kholo la onse akukhulupirira..." (Aroma 4:11)
.....Iwo amene atsata mayendedwe a chikhulupiriro.." (Aroma 4:12)
Abraham "analimbika mu chikhulupiriro.." (Aroma 4:20)

ZOYENERA KUTI UCHITE

Pozindikira za izo zodzadza masensezi onse asanu a mtima wako pa malo, nkhani, kapena ganizo zomwe wakhala ukuchita masiku apitawo, tsopano ulembe umo wadzadzira masensi asanu ako a mzimu wako ndi umo wakhala ukugwirira. Lembera mayankho ako pansipo. Ngati nkotheka ulembere "umboni" womwe ungakulimbikitse komanso ngakhale "wofooketsa" umene uzikuphunzitsa kena kake.

Zochitika kapena ganizo lidali.....
1. Ganizo lomwe ndidasankha kuti ndilandire limakhudzana ndi.....
2. Chithunzi kapena masomphenya amene ndidasankha kulumikizana nawo adali.....
3. Ndidayaba kulingalira mozama ganizo ili kuganizira....(Kufotokoza umo umalingalira mozama) umoumalingalira mozama)
4. Ndidayamba kulankhula za ichi mu njira yotere.....
5. Ndidayamba kuchita ichi munjira yotere.....
6. Ndidapenyerera kubadwa kwake mu machitidwe otere.....

Mu phunziro lathu lonse ili, tidzaona mosamalitsa gawo lililonse la chinthunzicho. Titenga chaputala pachokha pa sensi iliyonse mwa asanu awa a mzimu wa munthu komanso umo Mulungu kapena satana kapena Mulungu angawadzadze. Tidzakuphunzitsa umo ungakhalira wozindikira za masensi ako asanu a mzimu wako mu tsiku lili lonse. Uzazindikira msanga msanga amene akuwadzadz komanso pa siteji imene iwe uli. Izi zikuthandiza kuzindikira umo ungakhalire ndi Mulungu nthawi zonse kubereketsa moyo wako nthawi zonse.

Njira yodzadzitsira ma sensezi asanu awa ndi yosavuta komanso yochitika yokha. Timatha kuichita mosazindikira tsiku ndi tsiku.

Poyamba, timayamba ndi lingaliro kenako umakhala ndi chinthunzi cha makwanilitsidwe ake. Kenako umatenga nthawi yaitalipo kulingalira mozama za ichi. Kenako umaganiza kuti ulankhule za ichi kupyolera mu mphamvu za kulenga za mzimu wako zomwe zapatsidwa pathupi pamodzi ndi kufungatiridwa mkati mwako.



KUFUNGATIRA YESU YEKHA
KUFUNGATIRA YESU

| | SENSI | KAGWIRITSIDWE NTCHITO UMO IMFA | CHITSANZO CHA M'BAIBOLO | SITEJI |
|---|---|---|---|---|
| 1. | MAKUTU AMKATI KHUTU LA MKATI | KULANDIRA MAWU A MULUNGU | GENESIS 12:1-3 | KATENGA PAKATI |
| 2. | MASO A MKATI 2 CHIVU LUTSO 4:1 | KULANDIRA MASO MPHENYA A MULUNGU | GENESIS 15:5-6 | |
| 3. | MALINGALIRO AMKATI LUKA 2:19 | KULINGALI MAGANIZO A MULUNGU | AROMA 4:20-21 | KUFUNGATIRA |
| | CHIFUNIRO CHA MKATI MACHITIDWE 19:21 | KULANKHULA MAWU AMULUGU | GENESIS 17:5 | |
| | ZOTSATIRA ZAKE | KUFA KWA MASOPHENYA | GENESIS 16:2 GENESIS 17:18-19 | KUBADWA |
| | | KUUKA KWA MASO MPHENYA | GENESIS 21:1-2 AGALATIYA 4:4 | |

KUBEREKA MOYO KAPENA IMFA KUPYOLERA MU MZIMU YATHU DI KOCHITIRABE KOMANSO MWA DZIDZIDZI

Tiyeni tiganizire chitsanzo chosavuta cha kubadwa kwa moyo pamodzi ndi imfa kopyolera mu mphamvu za kulenga za mzimu wako.

ZOCHITIKA: Mwapatsidwa utmiki watsopano mwa mwayi kapena kukwezedwa pa mpando ntchito zomwe siudali kuziganizira.

Chaputala 3

## KUONA MASENSENZI ASANU A MZIMU WA MUNTHU NDI UMO MULUNGU AKUFUNA

Chikhulupiriro cha mtima: Ichi ndi chimodzi cha chuma pa moyo wa munthu nthawi zonse. Ndi mphatso yoperekedwa ndi Mulungu imene pamene yafungatiridwa mkati mwa munthu imabereka zolinga za Mulungu. Chikhulupiriro chosuntha mapiri, chochilitsa odwala, komanso chothandiza kuti munthu alandire

Kodi chimapezeka wanji? Kodi chimavyalidwa bwanji? Kodi chikupezeka mu baibulo? Kodi chikupezeka mu mabuku a malamulo a mpingo? Kodi chimapezeka mwa anthu olungama?

Kulankhula moona, ichi sichikupezeka monsemo. Chimapezeka mwa Mulungu yekha basi. Chikhulupiriro cha mutu chikhoza kuyamba ndi munthu koma chikhulupiriro cha mu mtima nthawi zonse chimayamba ndi Mulungu. Amalankhula vumbulutso mu mtima mwako ndipo kenako kukupatsa masomphenyaoti ukhale nawo monga adachitira ndi Abrahamu "tate wa chikhulupiriro. Poyamba Mulungu adalankhula lonjezo kwa Abrahamu. Kenako adapereka masomphenya a lojezano lokwanilitsidwa pomuonetsera iye nyenyezi za kumwamba komanso mchenga wakunyanja. Umo ndimo Abrahamu adayambira kufungatira kulankhula kwa Mulungu (mawu) pamodzi ndi masomphenya a Mulungu kukolera masensezi ena atatu a mzimu kukhala omezedwa ndi iye. Abrahamu adadzadza maganizo a mzimu wake ndi mawu ochokera kwa Ambuye.Iye adapereka chifuniro cha mkati mwake kulankhula lonjezo pamodzi ndi masomphenya okha a Mulungu. Zochitika za mzimu wake zidakoleletsedwa ndi kulankhula kwa Mulungu pamodzi ndi masomphenya kotero kuti zidamupanga kuti tsopano ayende mwa chikhulupiriro pamalonjezano a Mulungu. Mu nthawi yake yoyenerera, Mulungu adabweretsa imfa ya masomphenya aja ndipo keneko kukwanilitsidwa kwa masomphenya mwa uzimu.



Mu buku ili tidzasanthula siteji iliyonse pa yokha mwa ma siteji asanu ndi limodzi awa kuchokera kukufungatira mpaka ku kukwanilitsidwa komanso kusanthula ma sensezi asanu a mtima wa munthu kapena mzimu wake ndi umo Mulungu amadzadza onse awa pokhazikitsa chikhulupiriro cha mtima. Monga Dr. Paulo Yonggi cho akufotokoza kuti munthu amakhala woyembekezera ndi maloto pamodzi mdi mawu a Mulungu (rhema).

Ichi ndi chinthuzi cha phunziro lathu lomwe tisanthule. Chonde onani masesi awa)

## ABRAHAMU - TATE WA CHIKHULUPIRIRO

1. Adamva kulankhula kwa Mulungu (Genesis 12:1-3)
2. Adaona ndi maso a chikhulupiriro (Genesis 15:5-6) kukhala ndi pakati
3. Adaganizira ndi mtima wa chikhulupiriro (Aroma 4:20-21) kufungatira
4. Adalankhula mawu achikhulupriro (Genisis 17:5) kufugatira
5. Adachita mwa chikhulupiriro (Genesisi 17:23) kufungatita
6. Kuona imfa ya masomphenya (Genesis 17:18-91) kubadwa
7. Kulandira cholonjezedwa (Genesis 21:5) kubabwa

Chinthunzi pa tsamba la khumi ndi chisanu ndi chitatu(18)
Chikuonetsera masensezi asanu a mzimu wa munthu ndi umo Mulungu akufuna kudzadza iwo.

ndipo umafufuza mwatchutchutchu ndi kupeza njira imene lingaliro lako likhoza kukhazikika pamodzi ndi kutambasula. Pamene tikupita kwa Ambuye kuti akupatse chitsogozo ukhoza kupeza kuti Iye sakufuna iwe kuti njira zonse koma akhoza kukutsogolera ku njira yake yoti ukazindikire kena kake katsopano. Chitsogozo chotere cha uzimu chikhoza kukupulumutsa ku nthawi yaikulu yogwira ntchito.

Sitepe yachitatu imakhudzana ndi kufangatira. Apa umatenga vutolo nkuliika mu mtima mwako, mbali ya manja ya bongo lako ndikuliganizira mozama kwambiri. Umatenga kaulendo, kusamba kugona pa kanthawi chifukwa choganizira za vutolo. Umalipereka pamaso pa Ambuye kutialione wino kufikira limaumika kukhala chinthunzi chenicheni changwiro.

Sitepe ya chinayi imakhudza ndi kulifotokoza. Apa chiweruziro cha mnzeru komanso chodziwika bwino chimachokera mu zitsanzo za mmalembo chimagwiritsidwa ntchito kuti uyese kudzodzako ndipo uone ngati zikhoza kutsimikizilika kapena kukanika. Apa ulole mtendere wa Mulungu kulamulira moyo wako. Lola anthu ena kuti ayensenso. Nchodziwika bwino zipatso zake zimene zimatsimikizira zonse. Pamene ukugwira ntchito kupyolera mu kuyesa izi, bwerezaso malingaliro aja monga koyenerera.



Masensezi asanu a mzimu wako amene mu chaputala chotsatira amagwiritsidwa ntchito mu masitepe a yachiwiri ndi yachitatu. Mu sitepe yachiwiri kulankhula kwa Mulungu pamodzi ndi masomphenya a Mulungu kumagwiritsidwa ntchito kukutsogolera kuzindikira zomwo uyenera kufufuza pamodzi ndi kusanthula ndipo umaigwiritsa ntchito kukutsogolera mu nthawi yakafukufuku. Musitepe ya chitatu, apa umalingalira ozama mu mtima mwako pamene uli mkati mwa kufungatira.

ZOYENERA KUTI UCHITE

Pakumaliza kwa chaputala ichi chakuphunzira kuzindikira mphatso ya Mulungu ya kulenga mwa munthu, tiyeni tifufuzenso pa masitepe anayi aja omwe takambilana.

Ndimachita izi:

1. Sikawirikawiri 2. Nthawi zina 3. Nthawi zonse
Chidziwitso:
Ndimaona vuto, chosowa kapena yankho
.....1 2 3
Chikonzekero; Ndimagwiritsa ntchito ma sensezi anga onse kuphatikizapo ndi pemphero mu nthawi ya kufufuza chatsopano
.....1 2 3
Kufungatira:
Ndimakhala momasuka - kupumula kuti mtima wanga ugwire ntchito pa icho:
.....1 2 3
Kulifotokoza: Ndimaonetsera malingaliro olenga awa kuti afotokozeredwe
.....1 2 3

Ngati upambane zigoli zambiri uyenera kunyadira. Ngati sizili zambiri unyadirebe basi chifukwa choti mu phunziro ili uphunzira mwa thandizo la Mulungu umo ungakhalire moyo womasuka mu zoterezi.

Mwa ichi tikuona kuti munthu ali ndi mphamvu za kulenga. akhoza kusankha kugwiritsa mphamvu ya kulengayo kwa iye yekha. Akhoza kusankha kudzipereka komanso mzimu wake kwa Mulungu wamphamvu yose kuyenda mwa iye kapena akhoza kulolera satana kumpatsa mwayi kugwira ntchito kupyolera mu mphamvu zake za kulenga zomwe Mulungu waika mwa iye.

Ganizira mozama kuti uone ndi chinthunzi chiti mwa izi zili pamwamba apa chili chogwirizana ndi moyo wako.

MALINGALIRO OMWE MUNTHU AKHOZA KUKHALA NAWO AMENE AKHOZA KULETSA MUNTHU KUKHALA WOLENGA

Uchonge nambala yomwe ikuyimirira moyo wako pamene ukuganizira mphamvu zako zokhala wolenga;

0- sindidakhalepo ndi ganizo lotere
1- nthawi zina ndimakhala nalo ganizo lotere
2- nthawi zonse ndimakhala ndi ganizo lotere
1. Ndine wamkuru.....0 1 2
2. Ndili wotangwanika.....0 1 2
3. Kodi anthu ena adzaganiza chiyani? .....0 1 2
4. Ndilibe zondiyenereza zokwanira.....0 1 2
6. Ndimagwira ntchito.....0 1 2
   pa bungwe lina sindingathe kulenga
7. Ndine wamkazi koma amuna okha ndi amene
   .amalenga.....0 1 2

Tsono uwonkhetsa zonse pamodzi. Ngati siuli pa 0, apa ndiye kuti uli ndi malingaliro ena ake amene amaletsa mphamvu yako kukhala wolenga. Uyenera kusintha maganizo otero ndipo ukhale ndi maligaliro ena amene ali aphindu.

Mwina ukhoza kufuna kuloweza chaputala cha Afilipo 4:8 pamene akufotokoza motere, ".....Chotsalira abale, zinthu zili zonse zolemekezeka, zili zonsee zoyenera, zirizonse zokongola, zirizonse



zimeka zokoma, ngati kuli chokoma mtima china kapena chitamando china kapena zilingirireni izi....."

ZOLANKHULA ZINA ZOMWE ZIMAIMITSA KUYENDA MALINGALIRO A KULENGA

Sizigwira ntchito.... Inde. koma.....
Sizitheka..... siuli mwambo.....
Tipitanso kawiri.....sizili mu chikonzero.....
Za mbiri yakale..... ndife ochepa pa ichi.....
Chidzafuna nthawi.....osafulumira kwambiri
Limenelo sivuto lathu.....
Silidakonzedwe zimenezo.....
Siudindo wathu kutero.....
Adzaganiza kuti tapenga.....
Tili ndi zochita zambiri panopa.....
Sitidayambe tachitapo mu njira yotere.....
Tikambilane za ichi nthawi yina yake.....
Siukumvetsa vutolo.....
Zikumveka bwino ndithu koma sindilidziwa.....
kuti zikhoza kutheka
Sitidayambe tafikirapo motero.....
Takhala tikuchita mu njira yotere ndipo mwa ichi ziyenera.....
Kukhala zolondola
Tiyeni tikambilanenso pa kanthawi ndipo tionerere zotsatira zake.....
Zikumveka bwino ndithu koma kodi ukhoza kuzichita ndi anzako. Izi ndi zimene zimaononga mphamvu yako ya kulenga.

UMO MPHAMVU YAKULENGA IMAGWIRIRA NTCHITO

Sitepe yoyamba imakhudzana ndi chidziwitso. Apa umaona vuto kapena chosoweka kapena yankho ku vutolo.

Sitepe yachiwiri imakhudzana chikonzekero. Apa umakonzekera wekha kubereka njira ya kulengera pogwiritsa ntchito ma sensi ako

Ngakhale kuti Mulungu adalenga munthu mu chifaniziro chake (monga milungu yaing'ono nalingana ndi chipangano chakale cha baibulo la chiheberi) Mulungu sadakonze kuti Mulungu adzigwira ntchito yekha osati ndi anzake. Munthu nthawi zonse adali mbali imodzi ya kenakake ka kakuru kuposa iye. Iye adali nthambi yolumikizitsidwa kumpesa-kachisi yemwe mkati mwake muli wina. Iye adayenera kulolera moyo wa Mulungu amene adamlenga iye kuti udziyendayenda mwa iye. Mu njira yotere, adzamasula mphamvu yodzadza ya kulenga ya Mulungu kudziko lonse lapansi kumene iye akukhala. Iye sikuti ankati azigwiritsa ntchito mphamu ya kulenga kwa iye yekha koma kuti adali woti aipereke kwa Mulungu wamphamu yonse. Munthu walamulidwa "kudzadzidwa ndi mzimu wa Mulungu" pamodzi ndi kuyenda mu uzimu. Munthu ayenera "kukhala mwa khristu", osati mwa iye yekha".

Mphamvu ya kulenga ya munthu idzakhala yambiri kuposa mphamvuyomasulidwa ndi munthu amene amangoyang'ana zakulengedwa mwa mzimu wake. Sikuti munthu wodzidalira yekha amamasula mphamvu ya kulenga ya mzimu wake yopatsidwa ndi Mulungu koma ngati kuti adzazyola pa kufikira ku kumasula mphamvu yakulenga ya Mulungu-mlengi wazonse pamene iye ayang'ana kwa Mulungu pamodzi ndi kutchera khutu lake ku kuyenda kwa mzimu mwa iye.

## WOPANDA MPHAMVU YA KULENGA

Munthu amene angakhale wosalenga ndi amene sadapezepo choonadi cheni-cheni cha ich komanso umo angathe kukhalira mu dziko la uzimu-munthu yemwe angoyenda mwa thupi basi.

## WOLENGA KOMA MONYENGA

Chinthu choipitsitsa ndi satana kudzadza munthu ndi mphamvu za kulenga mu njira yotere, phamvu yakulenga mwa munthu imagwiritsidwa ntchito koma mosayenera. Munthu amakhala kuti



waonongedwa mtima wake ndi ganizo loipa kapena masomphenya oipa. Munthu amathundira-kufungatira ndipo pomaliza pake amadzabereka mphamvu zoononga za satana kudziko lapansi kumene iye akukhala. Izi zajambulidwa pa tsaba la chisanu ndi cinayi (9).

## NJIRA ZINAYI ZOKHUDZA MPHAMVU YA KULENGA



lapansi. Mulungu akulakhula kuti munthu mmodzi akhoza kuchita nkhondo anthu chikwi (1000) ndipo anthu awiri akhoza kuchita nkhondo ndi munthu zikwi khui (10,000). Mphamvu ya kulenga ya munthu imachulukira pamene akugwirira limodzi ndi anzako. Pamene uli womasukira mtima pamodzi ndi maganizo kwa anzanthu, apa ndi pamene umakula mwachangu komanso umasanduka wolenga. Ndidakula moyo wanga ndili pa mpingo umene umakhulupirira kuti iwo okha amene adzapite kumwamba. Apo padalibe mwayi wokhala ndi mphamvu zakulenga kapena kuchulukana. Chipatso chake chidali chodziwika. Ndimaganizira kuti mpingo uli kutali zedi pafupifupi zaka 50 ku choonadi chenicheni. Lero linondili womasuka kuphunzira kuchokera kwa munthu aliyense. Ndimawerenga pamodzi ndikusanthula abuku zikwi zikwi za anthu osiyanasiyana komanso amiyambo yosiyanasiyana. Apa sikuti ndimaqwirizana ndi zonse amalakhula koma kuti ndimapeza choonadi chochuluka komanso mzeru mu mabukuwo amene ndimatenga ngati opanda ntchito komanso a mafano. Mulungu amavumbitsa madalitso ake pa olungama pamodzi ndi osalungama omwe.

Mukhoza kulankhula motere, "Koma siuli pa ngozi yonyegedwa ngati uwerenge zochuluka zotere za anthu ambiri?

Ayi sizili choncho chifukwa choti ndili wotetezeka pa moyo wanga wauzimu chifukwa choti ndili ndi atsogolerri anga mu uzimu amene amandifungatira. Ndikaona kuti pena pake sindikumvetsa bwino, ndimakomana ndi tsogoleri anga awa ndikuona umo angandithandizire.

Mwa ichi ndikulimbikitsa iwe kuzamitsa moyo wako kuti ulandire zochuluka kuchokera kwa iwo. Uwalole kuti akuphunzitse kanthu kenakake ndipo udzakhala wozama.



Ndikulonjeza kuti maphunziro akuru omwe ndaphunzira pamodzi ndi masitepe okula mu uzimu omwe ndatenga pa moyo wanga wa uzimu adachitika pamene ndidaturuka mu mpingo wanga kenako ndikulandira chidziwitso cha mawu kuchokera kwa anthu osiyanasiyana. Mwa ichi uyenera kuchotsa mantha ako. Khazikitsa maziko enieni olimba ndipo kweza maso ako kuti uone zozama zina zatsopano. Siudzakhumudwitsidwa. Udzalowa mu uzimu wa kulenga. Mulungu akudalitse pamene akuyenda ulendo wako wauzimu!.

Chaputala 2

## MULUNGU WAPANGA MUNTHU KUKHALA NDI MPHAMVU ZOLENGA

Mulungu, Mlengi wazakumwamba ndizadziko lapansi, adapanga munthu mu chifaniziro chake" - mawu awa ali atanthauzo kwambiri makamaka mu baibulo lachiheberi. Mulungu adauzira mwa munthu mphweya wamoyo ndipo munthuyo adakhala wamoyo.

## ZA UMUNTHU-KOCHOKERA KU MPHAMVU ZOLENGA MU MZIMU WA MUNTHU

Chifukwa cha mphweya wa moyo wa Mulungu umene udaikidwa mwa munthu, munthu tsopano akukhala ndi mphamvu yakulenga. Anthu ena akukhala akupeza chinsinsi cha mphamvu ya kulenga yomwe Mulungu adaika mwa iwo ndipo akugwiritsa ntchito kuchidzalo chake. Izi timazitcha kuti "Humanism" (umunthu). Munthu waphunzira kuchokera ku mutu wake mpaka tsopano mu mtima mwake pamene mphamvu ya kulenga ya mphweya wa moyo wa Mulungu ikugwira ntchito ndi kuonetsera ntchito zake. Vuto ndi loti anthu otere ali a thupi ndipo mphamvu ya kulenga ya Mulungu sakuizindikira kwamphumphu.

## KHRISTU WODZADZIDWA NDI MZIMU WOYERA - MPHAMVU YA KULENGA YA MULUNGU

koma kuti kukhala ozindikira pamodzi ndi wodalira Iye amene amakhala pambali pa ine komanso amakhala mwa ine. Yesu ayenera kukhala mwa ife osati kudzidalira mwa ife tokha. Mwa ichi ndidakhala nthawi yaitali kuphunzira "kukhala mwa khristu" ndipo pomaliza pake ndidalemba bukulo lokamba za ichi.

Mwa ichi ndidakhala nthawi yaitali kuphunzira "kukhala mwa khristu" ndipo pomaliza pake ndidalemba bukulo lokamba za ichi.

Nchifukwa tsopano ndikulankhula za ichi? Kodi kapena ndikufuna kukamba za mabuku anga kapena kukuuza za kupambana kwanga kuti ndine wamkuru? Ayi sizili chomwecho! ndili wokhulupirira kuti aliyense wa ife ayenera kuphunzira maphunziro mu kuyenda kwake ndi Mulungu. Ndi ulendo woyenda sitepe imodzi imodzi osati mwachangu. Ngati ukufuna kuti uyende mwachangu, mapeto ake chimangokhala chikhristu cha maphunziro ndipo sichipindula kwenikweni. Kwa ine padadutsa chaka kuphunzira maphunziro onse atatu. Ndidatenga chaka chimodzi kuphunzira kukhala pachiyanjano ndi Mulungu, chaka chimodzi kuphunzira kukhala mwa Yesu chaka china kuphunzira kuulora Mulugu kuchilitsa zopweteka pamodzi ndi tchimo la ukapolo mkati mwa moyo wanga. Keneko Mulungu adaona kuti kuli koyenera kuti andiphunzitse zamphamvu ya kulenga mwa mzimu. Ndatenga chaka chimodzi kuphunzira za ichi.

KUZINDIKIRA PAMENE ULI MU ULENDO WAKO WAUZIMU.

Mwa ichi ndikudandaulira kuti nkoyenera kuti uzindikire pamene iwe uli mu ulendo wako woyenda ndi Mulungu komanso chimene Mulungu akufuna kuti ukhale sitepe yotsatirayo. Ngati bukulo ndi ili, chonde gwiritsa ntchito koma ngati ali ena, uyenera kusiya ili ndi kutenga lina labwino. Tikulankhula pano zokhudza moyo. Moyo ndi wako uyenera kuupatsa chomwe ukusowa. Upatse chimene Mulungu akukulangiza kuti upatse.



Usafunefune mphamvu ya kulenga mwa mphatso pa yokha ya Mulungu. Mmalo mwake uyenera kuzindikira kuti zotsatira za kuyenda kwa mzimu wa moyo mu chidzalo chake mwa iwe. Ngati ufunefune madulira- njira yophweka, mapeto ake sizikhala bwino chifukwa choti satana akukola. Satana anadikirira Yesu ndipo adapereka njira yachidule yotengera dziko lonse lapansi ngati angamugwadire ndikumulambira iye. Yesu adakana kutero Iye adatenga mbali yokhala mu chiyanjano ndi Atate ndipo adalankhula motere, "sindichita kanthu kwa Ine ndekha". Tiyenera kukhala anthu otere olankhulanso kuti, "Sindichita kanthu mwa ine ndekha". Mwa ichi uyenera kukhazikitsa umodzi ndi mlengi wako poyamba kuti mphamvu ya kulenga iyende monga mwa chipatso cha mphamvu ya wolenga ndipo siungayesedwe kulambira ziliza za anthu oyeramtima akale.

MPHAMVU YOLENGA YA MUNTHU

Mutha kuona kuti mtima wa munthu uli wolenga chifukwa choti tidalengedwa mu chifaniziro cha Mulungu. Mwa ichi munthu akhoza kumasula mphamvu yakulenga mu mtima mwake ndikukhala wolenga ndipo akhozanso kuzinyenga yekha ndi kukola mu sampha wa satana ngati sasamalira izi ndi zimene a m'badyo watsopano achita. Iwo adapeza mphamvu yakulenga ya mtima wa munthu ndipo tsopano akuphunzira umo angamasuleichi koma amakana kukhukupirira mphamu ya kulenga ya Mlengi ndipo chifukwa cha ichi amagwa mu uchimo wolambira, munthu. Mwa ichi, madulira sakhalanso madulira koma ali "olalikitsa".

KUKHAZIKITSA UMODZI NDI ANTHU ENA

Chinthu china chomwe ndikufuna kukulimbikitsa pamene ukusanthula ndi kuzindikira kufunikira kochitiira limodzi zinthu pomasula mphamvu ya kulenga. Mulungu wapanga munthu kukhala pamodzi ndi kugwira ntchito mwa umodzi. Palibe munthu angakhale ndi moyo ngati akhala yekha. Zidatengera pafupifupi anthu awiri (mamuna ndi mkazi) kuti mtundu ubadwe padziko

Ndimangophunzitsidwa za malamulo a mpingo pamodzi ndi ziphunzitso za mpingowo basi osati zinthu zoti zindibweretsere chiyanjano ndi Mulungu wa baibulo. Poonjezera apo, ndidali wosaphunzitsidwa komanso wosakhoza kuphunzira kumvera kwa anthu ena.

KUKHAZIKITSA UMODZI NDI MULUNGU

Padatenga zaka khumi ndikuyendayenda kufunafuna chaka ndi chaka ndipo pomaliza pa zonse ndidapeza njira ya umo ndingakhale mu chiyanjano ndi Mulungu wokhala mwa ine. Pomaliza pake ndidaphunzira umo ndingachitire. Sikudali kovuta ayi.Chifukwa chiyani? Chifukwa choti ngakhale mwana akhoza kuchita mosavuta! Kumbukirani kuti Yesu anati, "Lolani ana kudza kwa Ine pakuti ufumu wa kumwamba uli wa otere.....". Pamene mwana wanga wa mkazi adali ndi zaka zisanu ndi zitatu (8) adaphunzira kumvetsera kulankhula kwa mlengi mkati mwa moyo wake. Monga ena onse, iye adamva kulankhula kwenikweni kwa Mulungu. Tidapeza munthu amene adachilitsa ife komanso kutikonda kwambiri koposa umo timaganizira kapena timalotera. Nchosadabwitsa kuti Paulo adachitcha ichi kuti chikondi chosasanthulika.

Chimene ndingalankhule mubukuli pokhudzana ndi kumasula mphamvu ya kulenga ya Mulungu wamphamvu yonse ndi choti munthu akhoza kumva kulankhula kwa mzimu woyera mtima mwake komanso akhoza kuphunzira kukhala mu chikondi chodabwitsa cha mphamvu ya machilitso. Ngati udakalibe wokodwa mu ukonde wa kangaude wa chikhristu wachipembedzo ndipo ukufuna kumasuka, ndikupempha kuti uike buku ili pambali kaye pa miyezi ingapo ndipo mmalo mwake uwerenge buku langa lotchedwa "chiyanjano ndi Mulungu." Sali ovuta ayi. Tilinso ndi buku la ana osachepera zaka khumi. Ngati ungathe kutsatira malaulo a mmenemo mapeto ake ukhoza kukhala mu umodzi ndi Mulungu. Moyo wanga wasinthika pamene ndidaphunzira umo ndingalankhulane ndi Mulugu komanso umo ndingathe kumva kulankhula kwa mawu ake.



Moyo wakonso ukhoza kusintha chimodzimodzi.

Mu buku la "chiyanjano ndi Mulungu" tikuphunzitsa umo ungazitontholetse wekha komanso kutchera khutu umve kulankhula kwa Mulungu (kumene kumabwera ngati maganizo) kagwiritsidwe ntchito ka masomphenya komanso kuyamba kulemba zonse zochokera kwa mzimu (mu mtima mwako). Uwu ndi mtsinje wamadzi amoyo umene baibulo likufotokoza kuti udzayenda mkati mwa mitima (Yohane7:37-39).

Ndi mzimu woyera amene tonse timakhulupirira. Ichi ndi chikhristu cheni cheni. Ndi mphamvu pamodzi ndi moyo! ndi Mulungu mwini!

Pamene ukukhala moyo wa "chiyanjano ndi Mulungu" mapeto ake kumakhala kosavuta kumasula mphamvu yakulenga mu moyo wao.

KUKHAZIKITSA CHIYANJANO NDI MTIMA WAKO

Kwa ine mphamvu ya kulenga sichidali sitepe yotsatira kuchokera pa yoyamba. Mmalo mwake ndimafuna kuchilitsidwa ku maganizo anga kupyolera mu kulankhula kwa Mulungu pamodzi ndi masompheya a mphamvu yonse amene ali Mulungu. Iye adayamba kulankhula za chikondi pamodzi ndi machilitso mu mtima mwanga zonse zidachotsa zokhumudwitsa, zophweteka pamodzi ndi machimo. Ndi kulankhula kwa mawu ake kumene kumachotsa zotsekereza zonse zomwe zakhala zilipo pa zaka zambiri. Inde, mwazi wake udandilungamitsa ine pamaso pa Mulungu komabe ndidali kukhala pakati pa zokoma zambiri. Machilitso ku zonse zokomazo adabwera kwa ine kupyolera mu kumva kwa kulankhula. Buku langa lotchedwa "kupatsidwa uphungu ndi Mulungu" lifotokoza umo kulankhula kwa Mulungu kumachilitsira mkwiyo, kulakwa, kutsutsika, kupsyinjika pamene khristu akumasulidwa kuti tsopano akhale ndi chikhulupiriro chiyembekezo, chikondi, kuzindikirika ndi Yesu ndi zina zotere.

Penepake munthu ayenera kuphunzira kuyenda pamodzi ndikukhala mwa Yesu kwa ine, izi sizitanthauza kuchita zinthu mwa ine ndekha

Nditatha kuchita maganizo angaanga pa miyezi itatu, ndi kutaya zomwe ndidali nazo kutsala kamodzi kokha, pomaliza Ambuye adalankhula nane motere, Mark kodi ukadachita zolakwika pokhulupirira zolembera zako zomwe?" Ine ndimati "Ayi" ndipo kenako ndidayamba kukhulupira zolembera zanga. Zoonadi zonse ndidataya zidabwezeretsedwa patangopita masabata anayi okha.

Choncho, vuto lachitatu ukhoza kukhala nalo ndi zolembera mu buku ili ndi loti ukhoza kuona kuvuta kukhulupirira zomwe Ambuye akulankhula kukhudzana ndi zolembera zako pamene ukulowa mu madera atsopano ndi zolembera zako. Izi ndi zofunika. Uyenera kuzilandila izi monga mwa chikhalidwe. Ngati ukufuna, ukhoza kusiya zimene Mulungu akulankhula mu zolembera zako ndipo ukhoza kuchita mu njira imene ukuganizira kuti ndi yofunikira keneko ukhoza kulembera zotsatira ake. Nthawi yina yake, ngati ukhoza kutero, chita kalondolondo wa zolembera zako ndipo ulembere zotsatsatira ake. Ulolele zotsatirazo kukutsimikizira iwe pamene nthawi ikudutsa. Ndimagwirizana ndi nthawi monga nthawi zophunzirapo kanthu kena kake.

Kwa ine, kukhazikitsa mtima wa chikhulupiriro pamodi ndi kumasula mphamvu ya kulenga ndi zinthu zofanana. Ndi pamene Mulungu akudzadza masensenzi asanu azimu wanga ndi lye pamene mtima wa chikhulupiriro umakhazikitsidwa ndipo mphamvu ya kulenga imamasulidwa. Bwerani ndi kukhala nafe limodzi mu kuphunzira malamulo akumasula, mphamvu ya kulenga ya Mulungu.

Kwa :
Maurice Fuller, Roger Miller, Mart Vahi pamodzi ndi John Watson omwe ndi anzathu apa mtima komanso alangizi athu apa zauzimu.





## KULENGA - ZOTSATIRA ZA UMODZI

Kodi kuonjezera mphamu ya kulenga ndi cholinga mwa zolinga zako pa moyo wako? Kodi ukufuna kupeza njira zolenga ku mavuto amene ukakomana nawo tsiku ndi tsiku ku nyumba kwako kapena ku ntchito kwako? Kodi ukufuna kupeza njira zolenga ku mavuto amene umakomana nawo tsiku ndi tsiku ku nyumba kwako kapena ku ntchito kwako? Kodi ukufuna kulipatsa dziko lapansi kanthu kenakake kokhala nako kukongola kosatha? Kodi ukufuna kuzamitsa maonekedwe a moyo wa anthu ali ndi iwe kupyolera mu zolenga pamodzi ndi maganizo atsopano? Nkosakayika ukufuna kutero. Nchifukwa chiyani ukuwerenga buku ili lokhudzana ndi mphamvu ya kulenga?

Mwatsoka ngati ungaone mphamvu ya kulenga monga ngati cholinga chako pa ntchito yako, apa ndiye kuti sukuchita bwino. Kulenga (makamaka mphamvu ya kulenga) sikuti ndi mapeto azonse. Mmalo mwake ndi zotsatira za umodzi pakati pa Mulungu ndi Munthuyo Mphamvu ya kulenga imabadwa kuchokera ku umodzi wa mtima wa munthu ndi mtima wa Mulungu. Ichi ndi chimodzi mwa chipatso cha umodzi ndi mzimu woyera. Chimakula pamene tikuphunzira kumva mu mtima mwake komanso kulankhula kwa mzimu woyera. Imakula pamene munthu akuphunzira kumvera kuchokera ku mitima ya anzake ndi kulumikiza zomwe pamodzi ndi zoveredwa kukhala zolengedwa zatsopano.

Mu zaka zanga zoyambirira pa moyo wanga wachikhristu, sindidali kudziwa bwino kwambiri za kulenga. Ichi sichodabwitsa popeza kudziwa kena kalikonse umo munthu angakhalire mu chiyanjano ndi mzimu woyera. Sindidali kuzindikira umo ndingakhalire ndikukomana ndi mzimu wa Mulungu. Sindidali kuzindikira umo ndingakhalire ndikukomana ndi mzimu wa Mulungu. Sindidali kumvetsa kulankhula kwa Mulungu kapena kulankhula naye monga amachitira anthu akale opezeka mu malembo opatulika. Chikhristu changa chidali chamaphunziro, malamulo a mpingo osati cha uzimu ayi. Nkosavuta, nkosadabwitsa kuti ndidali kulephera kumasula mphamu ya kulenga ya Mulungu. Ndikudziwa kuti ndidali wopulumutsidwa chifukwa choti mtima wanga udali kutsamila kwa Mulungu ndipo ndidali kuchita zonse ndimadziwa kuti zikhoza kundipangitsa kumusangalatsa lye. Icho chidangokhala chidziwitso changa cha umo ndingalumikizanire ndi Mulungu amene ali mzimu ndipo chidali chosakhala chozama.

Pamene Thomas Jefferson adasiya ntchito ku Moticello adalenga zinthu ambiri pamene adali ndi zaka makumi asanu ndi atatu. Dr. George Washngton Carver adali munthu waphindu pa kulenga fundo zofunikira za malimidwe ali ndi zaka makumi asanu ndi atatu (80). Alexander Graham Bello adakonza ungwiro wa telefoni (lamya) ali ndi zaka makumi asanundi mphambu zisanu ndi zitatu (58) ndipo adakonza vuto la penda penda wa ndege ali ndi aka makumi asanu ndi awiri (70). Mark Twain adalemba mabuku awiri, "Eve's Diary" ndi THE $30,000 Bequest" ali ndi zaka makumi asanu ndi awiri ndi mphambu imodzi (71). Benjamini Frranklin adagwira ntchito yolemba ali ndi zaka makumi asanu ndi atatu pamodzi ndi mphambu zinayi. Mdandanda ukhoza kupitirirabe.

Pulofesara Harvey Lehman mu kusanthula kwa zinthu zosachepera chikwi zidalengedwa pamene adali ndi aka makumi asanu ndi awiri ndi mphambu zinayi (74). Izi zingopherezera kuti pamene tikugwiritsa ntchito kwambiri mphamu zathu zolenga, zolengedwazo zimakhazikitsidwa kukhala zooneka kwa anthu onse.

Mphamvu yakulenga mwa mzimu siyochitika mwa ngozi. Imangofunika cholinga chenicheni chabwino pochita zimenezo. Buku ili litsegula makomo a kumvetsa kwako kwabwino kuti kulenga kwa Mulugu kukhoza kuchitika mwa iwe mu njira imene mwina umangolota chabe. Pamene uli mu uzimu wa Mulungu Malire ako ako amangokhala mwa Mulungu. Udzaona kuti ukuchita koposa mmene umaganizira chifukwa choti palibe malire kwa iwe. Apa tsopano waphunzira kukhala mu mphamvu ya Mulungu.

Muchaputala choyamba mudaona kuti mphamvu yakulenga ndi zotsatira a kukhala mu umodzi ndi mulungu. Mu chaputala chachiwiri tiphunzira kuti Mulungu adamupanga munthu kukhala wolenga. Mu chaputala chachitatu tidzaona kuti mphamvu ya kulenga iyi imasulidwa pamene talola Mulungu kudzadza masensezi anthu omwe ndi asanu mmoyo wathu ndi Iye mwini. Mu chaputala chachinayi tidzaona umo tingazitonthonzere tokha kuti tikathe kuona kuyenda



kwa mzimu wake mwa ife. Mu chaputala chachisanu tidzasanthula sitepe ndi sitepe umo Mulungu amadzadzira sensi iliyonse mwa zisanu izi mmoyo wathu ndi Iye mwini.

Mu chaputala cha khumi tidzapeza lamulo la imfa ya masomphenya ndipo tidzaphunzira kufunikira kwa kuleka masomphenya kuti akhale monga Mulungu akufunira kutsogolera ife. Mu chaputala cha khumi ndi chimodzi chidzzafikitsa kupherezera zonse makwanilitsidwe kumene kuli kubadwa kwa mphamvu ya kulenganso ya Mulungu mwa ife.

KUKHUDZANA NDI KULEMBERA

Bukuli lisowa kuti udzilembera kwambiri pamene ukusanthula. Ndikadakonda kutchulapo zinthu zambiri zokhudzana ndi izi zomwe zili zothandiza.

1. Khala womasuka kubwerezanso mafunso kuti akhale ogwirizana ndi zosowa zako.

2. Ukhoza kuona kuvuta kulembera zinthu zina zomwe zili zofunikira monga zachuma kapena za bizinesi. Ngati zili chomwecho tiyenera kuzikumbutsa tokha zomwe zokhudzana ndi moyo zili zopatulika.

Mwa chitsanzo pamene ndidayamba kugwira ntchito ndi aza malonda ndidali wokaikira kulembera za izo pazifukwa zingapo. Poyamba ndimafuna kukhala wotsimikizika kuti Mulungu akugwirizana nazo. Mwa ichi ndidalembera za ichi. Kenako ndidali wa mantha kukhulupirira zolembera zanga pamene zimafika pakujambula komanso kulembera olowa ndi zoturuka. Ambuye adandiuza kuti sindipanga ndalama pa miyezi ingapo yoyambirira koma kuti ndidayenera kudikira mpaka mwezi wa Juni. Sindidakhulupirire kuti ndingapange ndalama komanso sindidali wotsimikizika mtima kugwiritsa ntchito zolembera zanga ndipo kenako ndidayamba kugulitsa zinthu zanga ndipo ndimaganiza kuti zidali zokhonzeka.

D. Maphunziro ena amene Abraham adaphunzitsidwa pamene amakula muchikhulupiriro (223) Nkofunika kuti maphunziro okhudzana ndi "chiyanjano ndi Mulungu" mu buku komanso mu ma vidiyo a Mark ndi Patt Virkler ayenera kuti awerengedwe mwa gulu la anthu musadayambe kuwerenga buku ili. Ngati izi sizingachitike chonde werengani komanso buku lotchedwa "kulankhulana ndi Mulungu." Izi zikunthandizani kuti mumvetse bwino zonse zili mubukuli.

MUTU WOYAMBIRIRA * NDANI? INE? KULENGA?

Mafunso ndi mayankho pa chikhulupiriro chako kukhudzana ndi mphamu yakulenganso (ulembe kuti zoona kapena zabodza mosalembedwamo.

1. Kukhala wolenga kutanthauza kulingalira kapena kuchita kanthu kena kake kachilendo kotheratu.
2. Okhawo ozama, alunso, ndi amene angathe kulenga kanthu kenikeni katanthauzo
3. Anthu okhala ochepa amphatso za uzimu amene akhoza kukhala olenga
4. Kulenga ndi kosatheka ndipo ngati misala chabe.
5. Ngati uli nazo mphamvu za kulenga, munthu wina wake adzakuzindikira ndipo adzadziwa luso lako.
6. Malingaliro ali ngati zinthu za masenga. Sikoyenera kumawagwiritsa ntchito.
7. Maganizo a kulenga ali abwino ngosatheka kuchitika.
8. Kulenga kutanthauza ku kukhazikitsa
9. Njira yolongosoka yopezedwa kale

Mwina mwake siudafufuze fundo ili yonse apa kuti ndi yoona popeza iliyonse ndi yonamiza ndipo pa zaka zambiri mu mbiri ya moyo wa dziko lapansi zakhala zikukhulupiriridwa motero (Onani zitsanzo zambiri mu buku lotchedwa "kulingalira" (Imaginner) lolembedwa ndi Michael Le Boenf).



Timaganizira za Einstein monga munthu wodziwika ndi wanzeru ndipo adalidi chomwecho koma anthu chomwe sazindikira ndi choti adatenga nthawi yake yaikuru akugwira ntchito mu ofesi zake ku dziko la Swiss. Malo otani otsitsimutsidwa mwakuganizira pamodzi ndi kulenga kwa anthu ena!

Timanganizira a Dale Carnegie, monga munthu amene adalenga maganizo amene athandiza zikwi kuphatikiza zikwi za anthu kukhala moyo wosangalala, waphindu komanso wabwino. Carnegies adapherezera mphamu yakulenga motere:

....."Malingaliro amene ndikuimilira sali anga. Ndidawabwereka kuchokera kwa Socrates. Ndidawachotsa kwa Chestaer Field. Ndidawaba kwa Yesu. Ndipo tsopano ndidawaika mu buku. Ngati siukonda malamulo awo, nanga udaqwiritsa a ndani?

Anthu ambiri alenga zinthu zambiri zimene iwo sadzaphunzira. Mwa chitsanzo Eli Whitney amene adalenga makina a nthonje adali mphunzitsi.

Samueli Morse pamodzi ndi Robert Fulton, adalenga telegalafu pamodzi ndi boti ya mmadzi ndipo onse awa awiri adali anthu ojambula zinthuzi pogwiritsa ntchito zolembera. Kukhala wosaphunzira pa china chake ndi kwabwino chifukwa siuchititsidwa khungu ndi miyambo ya anthu.

Maganizo ofuna kulenga chinthu ndi ofunikira koposa anthu okhala ndi mphamvu kapena luso lolenga zomwe munthu angakhale nazo. Mwa chitsanzo mu nthawi ya nkhondo ya chiwiwi ya dziko lonse lapansi,BF Goodrich adalandira maganizo a anthu zikwi zitatu wolembedwa ntchito pa chaka chilichonse ndipo magawo atattu a iwo adali abwino kubweretsa chuma.

Kukula kwa nsinkhu kumaonjeranso koposa kukhala wochepa nsinkhu. George Bernard Shaw adapambana mphoto ya NOBLE PRIZE pamene adali ndi zaka makumi asanu ndi awiri (70).

Lalembedwa mchaka cha 1990 - ndi Patt Virkler-
Lobwezeredwanso kusidikizidwa mu chaka cha 1984, 1987, 1989.

Buku ili ndi lotetezedwa ndi bungwe la za malamulo okopera luso lolemba la dziko la Amerika. Buku ili siliyenera kuti likoperedwe kapena kusindikizidwa ndi kumagulitsa. Kukopera dime zina mu bukuli ndi kumagwiritsa ntchito pagulu posanthula malembo ndi kovomerezeka. Chilolezo chikhoza kuperekedwa pokhapokha munthu atapempha. Malembo onse opatulika mubuku ili akuchokera mu mtundu wa baibulo lotchedwa "King James Viarsions.

Osindikiza bukuli ndi a;
Destiny Image Publishers,
P.O. Box 351
Shippensburg, PA 17257

"Kulankhula zolinga za Mulungu ku m'bado uno"
ISNB 1-56043-004-4

Ogawidwa ku dziko lonse lapansi.

Osidikizidwa ku America (USA)

Buku ili ndi zotsatira za kudzipereka kwa a nkonzi onse awiri awa. Onse akhala akugawana maganizo pamodzi ndi mavumbulutso. Mau oti "Ine" akuimilira umodzi wa anthu onse awa pamodzi. Buku ili ndi kutambasula chabe pamodi ndi kuzamitsa pa choonadi chomwe adalemba mu buku lotchedwa "KUKHAZIKITSA MTIMA WA CHIKHULUPIRIRO.
Lolembedwa ndi ankonzi onsewa awiri.



ZA MKATIMU

MUTU WOYAMBIRIRA - NDANI? INE? KULINGA?

1. Mphamvu yolenga- zotsatira zolumikizana ndi Mulungu
2. Mulungu adapanga munthu wake kukhala wolenga
3. Kuonanso zinthu zisanu (sensezi) za munthu ndi umo Mulungu amafunira kudzadza izo.
SITEJI YOYAMBA - KUKHALA NDI PAKATI
4. Chikonzekero cholandirira maganizo a kulenga a Mulungu
5. Kudzadza sensi yoyamba ya mzimu wa munthu pakumva kulankhula kwa Mulungu
SITEJI YACHIWIRI - KUFUNGATIRA
6. Kudzadza sensi yachiwiri ya mzimu wa munthu pakuona masomphenya a Mulungu (81)
7. Kudzadza sensi yachitatu ya mzimu wamunthu polingalira mozama kulankhula kwa Mulungu pamodzi ndi masompheya (12)
8. Kudzadza sensi ya chinayi ya mzimu wa munthu pakulankhula kwa Mulugu pamodzi ndi masomphenya (133)
9. Kudzadza sensi ya chisanu ya mzimu wa munthu pochita mwa chikhulupiriro (165)
SITEJI YACHITATU - KUBADWA
10. Imfa pamodzi ndi mdzukiro wa masomphenya (183)
11. Kubadwitsa kwa kulankhula kwa Mulungu (rhema) pamodzi ndi masompheya a Mulungu a wamphamu yonse (203)
12. Kupereka ulemelero wonse kwa Mulungu (209)
KUMAPETO
A. Kumvetsa mphamvu ya Rhema (mawu olankhulidwa a Mulungu) 215
B. Kumulola Mulungu kubwezeretsa mphamvu yako ya masomphenya (217)
C. Chidule cha chithunzi cha imfa ya masomphenya (221)

# MPHAMVU YAMZIMU YAKULENGA




LOLEMBEDWA NDI
MARK PAMODZI NDI
PATTI MRKLER